



# Buku la Mphunzitsi

Nthawiyabaibulo  
Kalasi Lachitatu ndi Lachinayi

Maphunziro A1 - A6



# Bible Educational Services

Registered Charity UK (No 1186004)

## Cholinga cha Utumiki

Kukonzera ena maphunziro a Baibulo kuti apereke choonadi cha Yesu ku m'bado otsatira pa dziko lonse lapansi.

## Masomphenya a Utumiki

Kuperekwa ku m'bado wotsatira maphunziro okwanira, m'chiyankhulo chawo powalembera ndi kuwathandiza komanso kuthandiza anzathu ena onse odzipereka pa dziko lonse.

## ZOYENERA KUDZIWA

### Zomwe a Bible Educational Services amachita

A Bible Educational Services (BES UK) amasindikiza maphunziro a "Nthawiyabaibulo", "Moyo Watsopano" ndi "Okolola" a m'Chingerezi komanso amathandiza a Postal Bible Schools ndi mabungwe ena amene amagwiritsa ntchito maphunziro a BES ku UK ndi ku mayiko a kutsidya la nyanja pokawachezera, kugwira nawo ntchito limodzi, kuwalangiza ndi kuwaphunzitsa. BES imagwiranso ntchito pamodzi ndi magulu ena amene akugwira ntchito yomasulira maphunzirowa m'ziyankhulo zavo, pomasulira, kusindikiza ndi kuperekwa maphunziro kwa anthu ena. Maphunzirowa amaperekedwa mwaulere kwa ophunzira onse.

Maphunziro a Nthawiyabaibulo anayamba kugwiritsidwa ntchito ku Kumpoto kwa Ireland zake 60 zapitazo. A Bible Educational Services ndi amene ali ndi udindo woyang'anira ntchito yosindikiza maphunzirowa m'Chingerezi ndi m'ziyankhulo zina zonse. Maphunziro a Nthawiyabaibulo amasindikizidwa mu A4 ndipo amathandiza ophunzira m'madera ena kuti masabata anayi aliwonse azitha kutumiza mayankho ku Postal Bible School Centre kuti akachonge. Posachedwapa, tikuyamika a bungwe la Every Home Crusade (Bungwe la Chitsistimutso) ku Belfast, anayamba kusindikiza maphunziro a miyezi isanu ndi umodzi amene amatchedwa A5. Amenewa amagwiritsidwa ntchito m'matchalichi ndi m'sukulu makamaka ku mayiko akunja kuti akhale osavuta chifukwa kumeneko njira zotumizira ndi zovuta kwambiri.

Maphunziro a BES ndi apadera kwambiri chifukwa amatha kugwiritsidwa ntchito m'nyumba kapena pa gulu (tchalichi kapena sukulu), potsatira ndondomeko imene imalola ophunzira kuphunzira kwa zaka makumi awiri. Gulu lililonse lili ndi maphunziro asanu molingana ndi zaka zavo, Amene sanayambe sukulu (Kalasi 0), zaka 5-7 (Kalasi Yoyamba), zaka 8-10 (Kalasi Yachiwiri), zaka 11-13 (Kalasi Yachitatu), zaka 14-16 (Kalasi Yachinayi). Pali ndondomeko ya kaphunzitsidwe ya zaka zitatu ya gulu lililonse molingana ndi zaka zavo. (Onani peji 4.) Magulu angathe kusintha molingana ndi kuthekera kwavo. A Bibletime Resource amaperekwa mpata kwa ana kuphunzira Mawu a Mulungu ndi kutha kuzindikira kufunika kwa Uthenga Wabwino pa miyoyo.

Maphunziro akupezeka m'Chingerezi pa BES website – [www.besweb.com](http://www.besweb.com) kapena kuchokera kwa Mlembi Wamkulu. Amapezekanso pa website ya ziyankhulo zina. BES ali ndi zomwe analomba zothandiza amene akufuna kugwira nawo ntchitoyi, ndipo zimenezi zilinso pa website yawo.

## Keyala

### International and Northern Ireland Secretary (stockist of all English lessons)

Mr S Balmer, BES Office (UK), 37a Belmore Street, Enniskillen, Northern Ireland. BT74 6AA

Phone: 00 44 286 632 2462

Email: sam@besweb.com

### UK Secretary – Editorial feedback

Mr Stephen Gillham

Email: stephen.gillham@besweb.com

**Web address:** [www.besweb.com](http://www.besweb.com)

**Email address:** info@besweb.com

## BUKU LA MPHUNZITSI

Poyamba, maphunziro awa anakonzedwa ndi cholina choti akhale otumizira anthu, koma lero maphunzirowa akugwiritsidwa ntchito kwambiri pamene njira zotumizira ndi zosadalirika. M'madera ena monga ku mipingo ya ku Afrika, India ndi mayiko ena kulibe njira zotumizira zodalirika. Chifukwa cha ichi, Buku la Mphunzitsi linakonzedwa kuti lithandize amene sangathe kulandira pa positi. Buku la Mphunzitsi m'buku lino ndi la Kalasi Lachitatu ndi Lachinayi.

Buku la Mphunzitsi lililonse lili ndi ndime zonse zimene zili m'maphunziro a Nthawiyabaibulo. Maphunziro a Nthawiyabaibulo ndi Buku la Mphunzitsi zinakonzedwa kuti zigwire ntchito sabata lililonse. Maphunziro a mwezi wa Epulo amafotokoza za Paska ndipo a mwezi wa Disembala za Khirisimasi.

Madera ena amagwiritsa ntchito maphunziro a pa mwezi otchedwa A4, amene ali ndi maphunziro anayi ndipo ena amagwiritsa ntchito maphunziro otchedwa A5 amene ali ndi maphunziro 24. Mphunzitsi kapena mtsogoleri akuyenera kupereka maphunziro a A4, ndipo sabata lililonse azilemba mayankho a phunzirolo m'tchalichi, ku sukulu kapena ku nyumba ndi kupereka mayankhowo sabata lotsatiralo. Kumapeto kwa mwezi, mphunzitsi kapena mtsogoleri adzilandira maphunzirowo ndi kukachonga, akatsiriza abwere nawo ndi kupereka kwa ophunzirawo.

Ngati ophunzira akugwiritsa ntchito buku, mphunzitsi atenge bukulo kumapeto kwa phunziro lililonse ndi kukachonga. Koma tikudziwa kuti madera ena izi ndi zosatheka. Ngati akuphunzira m'kalasi, ophunzira asinthane mabuku awo ndipo mphunzitsi kapena mtsogoleri awathandize kupeza mayankho ndipo ophunzirawo achongelane maphunziro awo. Kumapeto kwa bukuli kuli malo oyika marikisi amene wophunzira wapeza mwezi uliwonse ndiponso malo a ndemanga ya mtsogoleri ya momwe wophunzirayo akuchitira m'kalasi. Palinso satifiketi yomwe wophunzira ayenera kulandira yoonetsa marikisi ake a maphunziro a miyezi isanu ndi umodzi.

Timakondwera pamene anthu akutifotokoza zomwe akukumana nazo pogwiritsa ntchito Buku la Mphunzitsi ndi mabuku a Nthawiyabaibulo ndipo tumizani ndemangazo kwa stephen.gillham@besweb.com.

## KUKONZEKERA KWA APHUNZITSI

Buku la Mphunzitsi si lotsekeka kuti mphunzitsi sangathenso kuyikapo zinthu zina zomwe akuziona kuti ndi zothandiza pophunzitsa. Nawa malangizo othandiza pogwiritsa ntchito Nthawiyabaibulo.

- **Kudziwa bwino nkhanzi** - Aphunzitsi akuyenera kudziwa bwino nkhanzi ya m'Baibulo komanso phunziro la Nthawiyabaibulo lomwe akugwiritsa ntchito. Nkhani ndi yakuti, mphunzitsi awerenge phunzirolo nthawi yophunzitsa isanakwane. Iye amvetse bwino ndondomeko ya phunziro lililonse kuti akonzekere bwino kuphunzitsako.
- **Kumvetsa phunziro lokaphunzitsa** - Poyamba pa ndondomeko ya phunziro lililonse pali mawu akuti, "Ife tikuphunzira kuti" motsatidwa ndi zolinga ziwiri zophonuzirira zomwe mwina ana angamvetse ngati mphunzitsi atafotokoza, kenaka pali gawo lotsiriza phunziro la Nthawiyabaibulo. Cholina chophunzirira ndi kufuna kudziwa nkhanziyo, pamene chachiwiri ndi cholimbikitsa ophunzira kuti aganizire zomwe aphunzirazo ndi kuzigwiritsa ntchito pa moyo wawo. Zolinga zimenezi zikugwirizana kwambiri ndi fundo/choonadi cha m'phunzirolo ndipo aphunzitsi akuyenera kugwiritsa ntchito zimenezi kuti adziwe momwe aphunzitsira ndi zomwe ana aphunzira.
- **Mawu oyamba** - Maphunziro onse akuyamba ndi mawu akuti, "kumene kuli ana" ali ndi zomwe akukumana nazo. Pali njira zambiri zomwe tapereka zothandiza ana kutenga mbali pa zokambirana nthawi ya maphunzirowo.
- **Kuphunzitsa** - Fundo zazikulu za phunziro tapereka. Tikuyembekezera kuti aphunzitsi sadzikhalanso akumaziwerenga pamene akuphunzitsa koma kuti akhala atadziwa bwino nkhanzi yonse ndipo adzitha kufotokoza nkhanziyo mochititsa chidwi. Mphunzitsi ayesetse kuti ana amvetse mitu ya maphunzirowo kuchokera pa nkhanzi yomwe akuphunzira ndiponso awathandize kumvetsetsa zoyenera kuchita kuchokera mu nkhanziyo. Pamene m'poyenera tayesetsa kufotokoza bwino monga nkhanzi chabe. Mawu amenewa tawalemba motere:  
***ITALICS***.
- **Kuphunzira** - Nkhani iliyonse ili ndi Vesi Yoloweza. Malo ena muli Mavesi Oloweza awiri; taonjezera vesi ina yomwe tikuona kuti itha kuhala yothandiza kuti ana aphunzire mosavuta. Tikukhulupirira kuti ana adzaphunzira Mavesi Oloweza ndipo aziwakumbukira koteri kuti adzadziwa mavesi ambiri.

- **Kutsiriza** - Kwa amene akuphunzira m'kalasi, mphunzitsi ayenera kudziwa ngati ophunzira angathe kutsiriza ntchito yawo ndiponso za thandizo lomwe likufunika kuchokera kwa mphunzitsiyo. Kwa ophunzira ena padzafunika kuti mphunzitsi aziwerenga nkhanayo, ophunzirawo n'kumatsatira kapena kumvera. Koma enanso adzatha kuwerenga okha nkhanayo. M'njira zonse ziwiri, ndi kofunika kuwauza malangizo okhudzana ndi mafunso. Ngati Nthawiyabaibulo sikuchitikira m'kalasi, n'kofunika kuti aphunzitsi azipezeka kuti azithandiza kuyankha mafunso osati aziyankha ngati a m'kalasi wamba. Ophunzira ayenera kumasangalala, kulimbikitsidwa ndi kuyamikiridwa pamene kuphunzira.
- **Kukumbutsana** - Zomwe zingattheke chitani, khalani ndi nthawi ya mafunso, ya masewero ndi zina zambiri. Izi zidzathandiza kuphunzira ndi kukumbukira pamtima nkhanayo.
- **Kuonetsa** - Nthawi zina, zinthu zoti muonetse zidzakhala zovuta kuzipeza koma ngati n'kotheka yesetsani kupeza zithunzi kapena zida zina zothandiza kuti ophunzira amvetse nkhanayo. Zinthu zimene ophunzira akuziona zimathandiza kwambiri pofotokoza nkhan. Pamene n'zotheka, pezani zithunzi kuchokera ku [www.freebibleimages.org](http://www.freebibleimages.org) (FBI) zomwe mungathe kulandira. Kumapeto kwa Buku la Mphunzitsi kuli zina zoonjezera momwe akufotokoza kwina kumene mungapeze zithunzi za nkhan za m'Baibulo mwaulere.
- Ngati mungapeze fotokope mutha kukulitsa zithunzizo, kukhala za kalala ndi kuzigwiritsa ntchito pophunzitsa.

## Nthawi ya Phunziro

- **Machitidwe.** M'buku la Mphunzitsi muli machitidwe a phunziro lililonse, koma mphunzitsi ali ndi ufulu nthawi ndi nthawi kusintha machitidwe ake.

1. Mawu Oyamba ndi kufotokoza nkhan - mphindi 15
2. Kuphunzitsa Vesi Yoloweza – mphindi 5 mpaka 10
3. Kutsiriza kulemba - mphindi 20
4. Mafunso ndi zochitika zina mpindi 5 mpaka 10.

Kumbukirani mawu ofunika awa:

“Ndiuzeni ndipo ndidzayiwala,  
ndionetseni ndipo ndidzakumbukira,  
loleni ndichite nawo ndipo ndidzamvetsetsa.”

## Zophunzitsa Nthawiyabaibulo

	KALASI 0 (sanayambe sukulu) Kalasi Yoyamba (Zaka 5-7) Kalasi Yachiwiri (Zaka 8-10)	Kalasi Yachitatu (Zaka 11-13)	Kalasi Yachinayi (Zaka 14+)
MAPHUNZIRO A	1. Chilengedwe 2. Nowa 3. Petulo 4. Petulo - Mtanda 5. Abrahamu 6. Abrahamu 7. Petulo 8. Petulo 9. Yakobo 10. Akhristu Oyambirira 11. Paulo 12. Nkhani ya Khrisimasi	1. Chilengedwe 2. Nowa 3. Petulo 4. Petulo - Mtanda 5. Petulo 6. Abrahamu 7. Yakobo 8. Pemphero 9. Paulo 10. Paulo 11. Paulo 12. Nkhani ya Khrisimasi	1. Chilengedwe ndi Kugwa 2. Zochitika Zoyamba - Genesis 3. Petulo 4. Petulo - Mtanda 5. Petulo 6. Abrahamu 7. Yakobo 8. Moyo wa Chikhristu 9. Paulo 10. Paulo 11. Paulo 12. Nkhani ya Khrisimasi
MAPHUNZIRO B	1. Moyo Woyambirira wa Khristu 2. Zodabwitsa 3. Betaniya 4. Mtanda 5. Mafanizo 6. Yosefe 7. Yosefe 8. Anthu Ankumana ndi Yesu 9. Mose 10. Mose 11. Mose 12. Nkhani ya Khrisimasi	1. Mafanizo 2. Zodabwitsa 3. Betaniya 4. Mtanda 5. Akhristu Oyambirira 6. Yosefe 7. Yosefe 8. Alembi a Uthenga Wabwino 9. Mose 10. Mose 11. Mose 12. Nkhani ya Khrisimasi	1. Mafanizo 2. Zodabwitsa 3. Betaniya 4. Mtanda 5. Akhristu Oyabirira 6. Yakobo ndi Banja Lake 7. Yosefe 8. Machitidwe 2:42 - Zoyenera Kuchita 9. Mose 10. Mose 11. Lamulo 12. Nkhani ya Khrisimasi
MAPHUNZIRO C	1. Danieli 2. Zodabwitsa Zina Zambiri 3. Anthu Ankumana ndi Yesu 4. Imfa ya Khristu 5. Rute ndi Samuele 6. Davide 7. Davide 8. Yoswa 9. Eliya 10. Elisa 11. Yona 12. Nkhani ya Khrisimasi	1. Danieli 2. Anthu Ankumana ndi Yesu 3. Zodabwitsa Zina Zambiri 4. Imfa ya Khristu 5. Rute 6. Samuele 7. Davide 8. Yoswa 9. Eliya 10. Elisa 11. Anthu Amene Mulungu Anawagwiritsa Ntchito - Chipangano Chakale 12. Nkhani ya Khrisimasi	1. Danieli 2. Zoyankhula za Yesu 3. Mphamvu za Ambuye 4. Imfa ya Khristu 5. Rute 6. Samuele 7. Davide 8. Yoswa 9. Eliya 10. Elisa 11. Anthu Ena a mu Chipangano Chakale 12. Nkhani ya Khrisimasi

	<p><b>A1 – KALASI Lachitatu</b>  <b>Phunziro Loyamba – Pachiyambi</b>  <b>Mutu – Mulungu analenga dziko lonse</b></p>	<p><b>A1 – KALASI Yachinayi</b>  <b>Phunziro Loyamba – Chilengedwe</b>  <b>Mutu – Pachiyambi</b></p>
	<p><b>Ndime Yowerenga:</b> <i>Genesis 1:1-19</i>  <b>Vesi Yoloweza:</b> <i>Genesis 1:1</i></p> <p><b>Ife tikuphunzira kuti:</b></p> <ol style="list-style-type: none"> <li>1. Mulungu analenga dziko lapansi lonse ndi zonse zili m'menemo.</li> <li>2. Mulungu analenga, amadziwa ndiponso amakonda munthu aliyense pa yekha.</li> </ol>	<p><b>Ndime Yowerenga:</b> <i>Genesis 1:1-31</i>  <b>Vesi Yoloweza:</b> <i>Ahebri 1:10; Yesaya 45:18</i></p> <p><b>Ife tikuphunzira kuti:</b></p> <ol style="list-style-type: none"> <li>1. Mulungu analenga dziko lapansi lonse.</li> <li>2. Mulungu ndi wamphamvuzonse.</li> <li>3. Mulungu analenga anthu mu chifanizo chake.</li> </ol>
<b>MAWU OYAMBA</b>	<p>Uzani wophunzira aliyense kuti alembe mayankho a mafunso awa. Atha kungolota mayankho ake! Kenaka ophunzira akambirane mayankho awo.</p> <ol style="list-style-type: none"> <li>1. Kodi mlengalenga muli nyenyezi zingati?</li> <li>2. Kodi pa dziko lapansi pali anthu angati?</li> </ol> <p>Pakatha nthawi pang'ono, awuzeni mayankho awa:</p> <ul style="list-style-type: none"> <li>• Molingana ndi European Space Agency, n'kovuta kudziwa chiwerengero cha nyenyezi. Iwo amati muli nyenyezi zikwizikwi mlengalenga mwathumu. Komanso kuli mlengalenga wina kumenenso kuli nyenyezi zosawerengeka!</li> <li>• Ena lero amati pa dziko lapansi pali anthu pafupifupi 7 biliyoni.</li> </ul>	<p>Kambiranani mafunso awa awiriawiri ndipo kenaka pa gulu lonse:</p> <ul style="list-style-type: none"> <li>• Kodi ndi liti lomwe munapanga chinthu chosonyeza luso lanu?</li> <li>• Kodi munakondwera ndi zomwe munapangazo?</li> </ul>
<b>KUTSIRIZA</b>	<p><b>Perekani Nkhani ya m'Baibulo</b></p> <p><b>Kambiranani ndi Kufotokoza:</b></p> <ol style="list-style-type: none"> <li>1. Chilichonse palibe, Mulungu anali alipo.</li> <li>2. Mulungu anapanga dziko m'masiku asanu ndi limodzi.</li> <li>3. Tsiku 1: Mulungu analenga kuwala ndipo anakusyanitsa ndi mdima. Tsiku 2: Mulungu analenga mlengalenga kusyanitsa ndi madzi apansi. Tsiku 3: Mulungu anasonkhanitsa madzi pamodzi ndi kutchula malo owuma kuti "dziko". Dziko linatulutsa zomera zobala mbewu. Tsiku 4: Mulungu anayika zounikira mlengalenga: dzuwa, mwezi ndi nyenyezi. Tsiku 5: Mulungu analenga zamoyo za m'nyanja ndi mbalame. Tsiku 6: Mulungu analenga nyama.</li> <li>4. Kenaka Mulungu analenga munthu m'chifanizo chake, mwamuna ndi mkazi, kuti adzaze dziko ndi kulamulira dziko lapansi ndi zolengedwa zonse.</li> <li>5. Mulungu anapereka chakudya kwa munthu ndi kwa zamoyo zonse.</li> <li>6. Mulungu anaona zomwe analenga ndipo anaona kuti zinali bwino kwambiri! (<i>Genesis 1:31</i>)</li> </ol> <p><b>Fotokozani Vesi Yoloweza ndipo limbikitsani ophunzira kuti aloweze.</b></p> <p><b>Tsirizani Phunziro Loyamba.</b></p> <p><b>Kuonetsa:</b> Onani FBI pa Zoonjezera A – Mulungu alenga dziko lonse.</p>	<p><b>Perekani Nkhani ya m'Baibulo</b></p> <p><b>Kambiranani ndi Kufotokoza:</b></p> <ol style="list-style-type: none"> <li>1. Mulungu analenga dziko lapansi m'masiku asanu ndi limodzi.</li> <li>2. Tsiku 1: Mulungu analenga kuwala ndipo anakusyanitsa ndi mdima. Tsiku 2: Mulungu analenga mlengalenga ndi kusyanitsa ndi madzi apansi. Tsiku 3: Mulungu anasonkhanitsa madzi pamodzi ndi kutchula malo owuma kuti "dziko". Dziko linatulutsa zomera zobala mbewu. Tsiku 4: Mulungu anayika zounikira mlengalenga: Dzuwa, mwezi ndi nyenyezi. Tsiku 5: Mulungu analenga zamoyo za m'nyanja ndi mbalame. Tsiku 6: Mulungu analenga nyama.</li> <li>3. Mphamu za Mulungu ndi zodabwitsa: Iye analenga dziko lonse ndi mawu okha, ndipo zinamatengera masiku asanu ndi limodzi okha!</li> <li>4. Mulungu analenga anthu m'chifanizo chake; Iye analenga mwamuna ndi mkazi.</li> <li>5. Pamene Mulungu anaona chilichonse chimene analenga, mawu ake anali akuti zinali bwino kwambiri. (<i>Genesis 1:31</i>)</li> </ol> <p><b>Fotokozani Vesi Yoloweza ndipo limbikitsani ophunzira kuti aloweze.</b></p> <p><b>Tsirizani Phunziro Loyamba.</b></p> <p><b>Kuonetsa:</b> Onani FBI pa Zoonjezera A – Pachiyambi.</p>
<b>KUKUMBUTSANA</b>	<p>Khalani m'magulu a anthu anayi, konzani chionetsero, choiyimira tsiku liilise pa masiku asanu ndi limodzi amene Mulungu analenga dziko lapansi ndiponso tsiku lachisanu ndi chiwiri pamene lye anapuma. Mwachitsanzo, gwirtsansi ntchito mapepala, lembanipo, chekenirani ndipo mumate pa khoma. Zimene mwamatazo zidzifotokoza nkhani yanu.</p>	<ol style="list-style-type: none"> <li>1. Kodi mwaphunzira chiyani za khalidwe la Mulungu m'phunziro lino? Lembanji ndakatulo yayifupi, kapena ndime yomwe ingasonyeze zomwe mwaphunzira.</li> <li>2. Ganizirani momwe ophunzira angafotokozer za kusya kwa pakati pa nyama ndi anthu pa chilengedwe cha Mulungu.</li> </ol>
<b>KHALANI MOYO UMENEWU</b>	<p><b>Zomwe tikuphunzira m'phunziroli:</b></p> <ol style="list-style-type: none"> <li>1. Mulungu ndi wamphamvuzonse ndipo analenga zinthu zonse. Ngakhale zomwe analenga ndi zochuluka kwambiri, Mulungu amene anazipanga, amazidziwa ndiponso amakonda aliyense wa ife pa yekha.</li> <li>2. Kodi izi zikukhudza motani machitidwe anga pamaso pa Mulungu ndi pa chilengedwe chake?</li> </ol>	<p><b>Zomwe tikuphunzira m'phunziroli:</b></p> <ol style="list-style-type: none"> <li>1. Mulungu analenga dziko lathu ndiponso analenga ife. Kodi izi zikuyenera kusintha motani miyoyo yathu?</li> <li>2. Werengani <i>Genesis 1:26-27</i> ndi <i>Yesaya 45:18</i>. Kodi cholinga cha Mulungu pa anthu chinali chotani?</li> <li>3. Kodi izi zikukhudza motani khalidwe lathu lero?</li> </ol>

	<p><b>A1 – KALASI Lachitatu</b>  <b>Phunziro Lachiwiri – Pachiyambi</b>  <b>Mutu – Mulungu analenga munthu.</b></p>	<p><b>A1 – KALASI Yachinayi</b>  <b>Phunziro Lachiwiri – Chilengedwe</b>  <b>Mutu – Kutsiriza</b></p>
<b>MAWU OYAMBA</b>	<p><b>Ndime Yowerenga:</b> <i>Genesis 1:20-31</i>  <b>Vesi Yoloweza:</b> <i>Genesis 1:27</i></p> <p><b>Ife tikuphunzira kuti:</b></p> <ol style="list-style-type: none"> <li>1. Mulungu analenga nyama, koma anapanga munthu mosiyana.</li> <li>2. Mulungu analenga munthu m'chifanizo chake, kuti akhale wofanana naye ndi kumalamulira chilengedwe chonse.</li> <li>3. Mulungu anapanga munthu kuti akhale naye pa ubale ndipo munthu akhalenso pa ubale wina ndi mnzake.</li> <li>4. Mulungu anamupatsa munthu udindo.</li> </ol>	<p><b>Ndime Yowerenga:</b> <i>Genesis 1:27-31; 2:1-9</i>  <b>Vesi Yoloweza:</b> <i>Yohane 1:1-3</i></p> <p><b>Ife tikuphunzira kuti:</b></p> <ol style="list-style-type: none"> <li>1. Mulungu anapuma tsiku lachisanu ndi chiwiri.</li> <li>2. Mulungu analenga Sabata kuti tizipuma.</li> <li>3. Mulungu anapereka moyo kwa munthu.</li> <li>4. Moyo wa munthu ndi wofunika kwambiri.</li> </ol>
<b>KUTSIRIZA</b>	<p><b>Perekani Nkhani ya m'Baibulo</b></p> <p><b>Kambiranani ndi Kufotokoza:</b></p> <ol style="list-style-type: none"> <li>1. Mulungu analenga nyama kuti ziberekane ndi kuchulukana.</li> <li>2. Mulungu analenga munthu m'chifanizo chake, kuti afanane naye, kuti alamulire nsomba, mbalame ndi nyama.</li> <li>3. Mulungu analenga anthu. Iye anawalenga mwamuna ndi mkazi.</li> <li>4. Mulungu analalitsa anthu ndi kuwapatsa ntchito yapadera ndi maudindo (akuti aberekane ndi kuchulukana, kudzaza dziko lapansi ndi kulamulira zolengedwa zonse za Mulungu).</li> <li>5. Mulungu anawapereka zakudya– zonse tikuzifuna pa moyo wathu.</li> <li>6. Mulungu anakondwera ndi zomwe analenga. Iye anati zinali bwino kwambiri!</li> </ol> <p><b>Fotokozani Vesi Yoloweza ndipo limbikitsani ophunzira kuti aloweze.</b>  <b>Tsirizani Phunziro Lachiwiri.</b></p> <p><b>Kuonetsa:</b> Onani FBI pa Zoonjezera A – Mulungu alenga munthu.</p>	<p><b>Perekani Nkhani ya m'Baibulo</b></p> <p><b>Kambiranani ndi Kufotokoza:</b></p> <ol style="list-style-type: none"> <li>1. Pachiyambi zinthu zonse kulibe, Mulungu analipo. Mawu (Ambuye Yesu) ndi Mulungu ndipo anali ndi Mulungu pachiyambi. Iye analenga zinthu zonse, ndipo popanda lye sukanakanhala kanthu kalikonse. Mulungu ndi mlengi ndipo ndi Mulungu wachiyambi cha zinthu zonse. (Onani Vesi Yoloweza.)</li> <li>2. Mulungu anayika munthu m'munda wa Edeni.</li> <li>3. Mulungu anayikamo mitengo yapadera iwiri mu Edeni: Mtengo Wamoyo, ndi Mtengo Wodziwitsa Zabwino ndi Zoyipa.</li> <li>4. Mulungu anapuma tsiku lachisanu ndi chiwiri ndipo analiyika kuti likhale tsiku limene munthu azipuma.</li> <li>5. Mulungu anapumira mpweya wamoyo mwa munthu. Izzi zinachititsa kuti munthu akhale wosiyana ndi nyama zonse. Moyo wa anthu ndi wapadera kwambiri ndi wamtengowapatali.</li> </ol> <p><b>Fotokozani Vesi Yoloweza ndipo limbikitsani ophunzira kuti aloweze.</b>  <b>Tsirizani Phunziro Lachiwiri.</b></p> <p><b>Kuonetsa:</b> Onani FBI pa Zoonjezera A – Kutsiriza.</p>
<b>KUKUMBUTSANA</b>	<p>1. Mulungu analenga anthu m'chifanizo chake kuti alamulire nsomba, mbalame ndi nyama. Kodi ife tikuyenera kuzisamalira motani zimenezi?</p> <p>2. Mulungu anakonza kuti ife tizikhala pa ubale ndi lye komanso ndi anzathu. Mulungu amatikonda. Kodi ife tingaconetse motani chikondi chathu kwa Mulungu ndi kwa anthu ena - 1) ku nyumba 2) ku sukulu 3) ku tchalichi?</p> <p>3. Kambiranani momwe Mulungu anapangira kuti aliyense wa ife akhale osiyana ndi mnzake. (Salimo 139:14) Jambulani chithunzi chanu choonetsa izi.</p>	<p>1. Kambiranani m'magulu anu ndipo fotozoa zomwe mwapeza pa gulu lonse:</p> <p>2. Werengani Eksodo 20:8 ndi Marko 2:27. Kodi kufunka kwa mavesi amenewa kwa ife n'kotani?</p> <p>3. Ife taphunzira kuti moyo wa munthu ndi wapadera kwambiri.</p> <p>Tsono inu mukuganiza kuti zimenezi zikukhudza motani moyo wathu pa zomwe amachita anthu a sayansi, a zacipatala, a zamalamulo ndi posamalira anthu okalamba?</p>
<b>KHALANI MOYO UMENEWU</b>	<p><b>Zomwe tikuphunzira m'phunziroli:</b></p> <ol style="list-style-type: none"> <li>1. Mulungu anatilenga ife kuti tikhale naye pa ubale komanso ndi anthu ena. Kodi zingsatinthe motani ngati aliyense wa ife atalapa ndi kukhulupirira?</li> <li>2. Pempherani kuti Mulungu atithandize kukwaniritsa udindo wathu ndi kuonetsa khalidwe lake (mwachitsanzo chikondi chake, kukoma mtima ndi chilungamo chake) sabata lino m'mabanja athu, mu sukulu ndi mu mpingo.</li> </ol>	<p><b>Zomwe tikuphunzira m'phunziroli:</b></p> <ol style="list-style-type: none"> <li>1. Kodi timapuma motani kapena kulephera kupuma motani pa miyoyo yathu lero? Kodi kupuma tsiku la Sabata ndi kofunka? Chifukwa chiyani?</li> <li>2. Kodi tingachite chiyani kuti tionetse kuti miyoyo yathu ndi yofunka kwambiri ndipo anatipatsa ndi Mulungu?</li> </ol>

	<p><b>A1 – KALASI Lachitatu</b>  <b>Phunziro Lachitatu – Pachiyambi</b>  <b>Mutu – Zinthu zinayamba kusokonekera!</b></p>	<p><b>A1 – KALASI Yachinayi</b>  <b>Phunziro Lachitatu – Chilengedwe</b>  <b>Mutu – Kubwera kwa tchimo</b></p>
	<p><b>Ndime Yowerenga:</b> <i>Genesis 2:15-17; 3:1-13</i>  <b>Vesi Yoloweza:</b> <i>Genesis 3:3</i></p> <p><b>Ife tikuphunzira kuti:</b></p> <ol style="list-style-type: none"> <li>1. Adamu ndi Hava sanamvere Mulungu.</li> <li>2. Adamu ndi Hava anali ndi manyazi ndipo anakumana ndi zotsatira za tchimo lawo.</li> </ol>	<p><b>Ndime Yowerenga:</b> <i>Genesis 2:14-19; 3:1-7</i>  <b>Vesi Yoloweza:</b> <i>Aroma 3:23; Aroma 6:23</i></p> <p><b>Ife tikuphunzira kuti:</b></p> <ol style="list-style-type: none"> <li>1. Mulungu analamula munthu kuti asadye chipatso cha Mtengo Wodziwitsa Zabwino ndi Zoyipa.</li> <li>2. Njoka inanamiza Hava ndi Adamu kuti asamvere lamulo la Mulungu.</li> <li>3. Adamu ndi Hava anachita manyazi.</li> </ol>
<b>MAWU OYAMBA</b>	Funsani ophunzira ngati ku sukulu kwavo kuli malamulo. N'chifukwa chiyani izi zili zofunika? Kodi chingachitike n'chiyani ngati anthu sakumvera malamulo?	Funsani ophunzira akambiranane awiriawiri: <ul style="list-style-type: none"> <li>• Udindo umene ali nawo ku sukulu/ku ntchito/ku nyumba.</li> <li>• Malangizo kapena ndondomeko zimene tikuyenera kutsatira.</li> <li>• Kodi chingachitike n'chiyani ngati anthu sakumvera zimezezi kapena kuphwanya?</li> </ul>
<b>KUTSIRIZA</b>	<p><b>Perekani Nkhani ya m'Baibulo</b></p> <p><b>Kambiranani ndi Kufotokoza:</b></p> <ol style="list-style-type: none"> <li>1. Mulungu anayika munthu m'Munda wa Edeni ndipo anamupatsa udindo woyang'anira mundawo. Mulungu anamupatsa munthu chilichonse chofunika, koma panali lamulo limodzi loti amvere. Munthu sanaletsedwa kudya chipatso cha "Mtengo Wodziwitsa Zabwino ndi Zoyipa". Mulungu anati akadzadya, adzafa ndithu.</li> <li>2. Kenaka Munthu anapsidswa udindo wopereka mayina kwa nyama ndi mbalame.</li> <li>3. Mulungu anapanga mkazi kuti azimuthandiza pa ntchito yake. M'banja, mwamuna ndi mkazi amayamba banja latsopano ndipo amagwira ntchito pamodzi.</li> <li>4. Njoka yochenjera, mdani wa Mulungu modzibisa, anachititsa kuti anthuwa akayikire lamulo la Mulungu. Iye anauza Adamu ndi Hava kuti akadya chipatsocco sadzafa. Njoka inanamiza mkaziyo ndipo anadya chipatso chimene Mulungu analamula kuti asadye. Ndipo iye anatenga china ndi kukamupatsa mwamuna wake ndipo iyenso anadya.</li> <li>5. Pamene mwamuna ndi mkazi anachita izi sanakhalenso osangalala. Iwo anasoka masamba ndi kupanga zovala zawa, ndipo anabisala pakati pa mitengo. Mulungu anawayitana ndipo iwo anamuza chimene anachita. Adamu analoza chala Hava ndipo Hava analoza chala njoka.</li> <li>6. Mulungu anatemberera njoka. Adamu ndi Hava nawo analandira chilango cha tchimo lawo. Iwo anamva ululu ndipo anayamba kuvutika ndi kugwira ntchito yotulutsa thukuta. Moyo waho unali owawa, ndipo tsiku lina iwo adzafa.</li> <li>7. Mulungu anapangira Adamu ndi Hava zovala za zikopa za nyama ndipo anawatulutsa m'Munda wa Edeni, kuita kutali ndi Mtengo Wamoyo.</li> </ol> <p><b>Fotokozani Vesi Yoloweza ndipo limbikitsani ophunzira kuti aloweze.</b>  <b>Tsirizani Phunziro Lachitatu.</b></p> <p><b>Kuonetsa:</b> Onani FBI pa Zoonjezera A – Zinthu zinayamba kusokonekera!</p>	<p><b>Perekani Nkhani ya m'Baibulo</b></p> <p><b>Kambiranani ndi Kufotokoza:</b></p> <ol style="list-style-type: none"> <li>1. Mulungu anamupatsa Adamu udindo wosamalira Munda wa Edeni ndi kupereka mayina kwa nyama zonse.</li> <li>2. Mulungu anati munthu akhoza kudya zipatso za mtengo uliwonse kupatala Mtengo Wodziwitsa Zabwino ndi Zoyipa. Mulungu anati zotsatira zakudya chipatso chimenechi chikhala imfa.</li> <li>3. Mulungu anamupangira mwamuna mnzake womathandiza, ndipo anamutcha mkazi. Iwo anayenera kuthandizana pa zonse. M'banja, mwamuna ndi mkazi amayamba banja latsopano ndi kugwira ntchito pamodzi.</li> <li>4. Njoka yochenjera, mdani wa Mulungu inanamiza Hava kuti asamvere Mulungu, ndipo anadya chipatso ndi kumupatsa china mwamuna wake amene anadyanso. Mwamuna nayenso sanamvere Mulungu pakudy chipatso. Adamu and Hava, onse awiri analephura kufika pa muyeso wa Mulungu pamene anadya chipatsocho.</li> <li>5. Adamu ndi Hava anadziwa kuti sanamvere Mulungu ndipo anachita manyazi. Iwo anayenera kukumana ndi zotsatira za chisankho chawo chosamvera Mulungu.</li> <li>6. Iwo analangidwa ndi Mulungu ndipo ubale waho ndi Mulungu unaonongeka.</li> </ol> <p><b>Fotokozani Vesi Yoloweza ndipo limbikitsani ophunzira kuti aloweze.</b>  <b>Tsirizani Phunziro Lachitatu.</b></p> <p><b>Kuonetsa:</b> Onani FBI pa Zoonjezera A – Kubwera kwa tchimo.</p>
<b>KUKUMBUTSANA</b>	<ol style="list-style-type: none"> <li>1. Lumikizani phunziroli ndi Aroma 5:12. Popeza Adamu ndi Hava sanamvere Mulungu, tonse timabawda ochimwa. Afunsemi ophunzira kuti apereke zitsanzo za kusamvera Mulungu m'miyoyo yathu.</li> <li>2. Kodi izi zimatikhudza motani 1) ife ndi 2) anthu ena?</li> <li>3. Kumbutsanani nkhaniyi pofunsana mafunso kuchokera pa phunziroli za kusamvera kwa Adamu ndi Hava.</li> </ol>	<ol style="list-style-type: none"> <li>1. Kodi zotsatira za kusamvera kwa Adamu ndi Hava zinali zotanii? Werengani Aroma 5:12-14 ndi 18-19.</li> <li>2. Kodi kusamvera kwa Adamu kukutikhudza motani lero?</li> </ol>
<b>KHALANI MOYO UMENEWU</b>	<p><b>Zomwe tikuphunzira m'phunziroli:</b>  Tikuyenera kupepesa kwa Mulungu kuti lye atikhululukire ndi kutipanga atsopano. Motero tidzayamba kukhala moyo wokondweretsa Mulungu ndi kutsatira malamulo ake.</p>	<p><b>Zomwe tikuphunzira m'phunziroli:</b></p> <ol style="list-style-type: none"> <li>1. N'chifukwa chiyani kumvera Mulungu kuli kofunika?</li> <li>2. Kodi tingamvera motani Mulungu pa miyoyo yathu lero?</li> </ol>

	<p><b>A1 – KALASI Lachitatu</b>  <b>Phunziro Lachinayi – Pachiyambi</b>  <b>Mutu – Kuchita zinthu m’njira ya Mulungu</b></p>	<p><b>A1 – KALASI Yachinayi</b>  <b>Phunziro Lachinayi – Chilengedwe</b>  <b>Mutu – Zotsatira za tchimo</b></p>
	<p><b>Ndime Yowerenga:</b> <i>Genesis 4:1-16</i>  <b>Vesi Yoloweza:</b> <i>Yohane 14:6</i></p> <p><b>Ife tikuphunzira kuti:</b></p> <ol style="list-style-type: none"> <li>1. Abele anatsatira njira ya Mulungu, koma Kaini njira yake. Mulungu analandira nsembe ya Abele koma anakana ya Kaini.</li> <li>2. Kaini anapha Abele. Mulungu anamuthamangitsa ndipo anakhala munthu woyendayenda. Kaini anachoka pamaso pa Mulungu.</li> <li>3. Pali njira imodzi yokha yopita kwa Mulungu, ndipo imeneyi ndi njira yake!</li> </ol>	<p><b>Ndime Yowerenga:</b> <i>Genesis 3:7-24</i>  <b>Vesi Yoloweza:</b> <i>1 Akorinto 15:22; Aroma 6:23</i></p> <p><b>Ife tikuphunzira kuti:</b></p> <ol style="list-style-type: none"> <li>1. Adamu ndi Hava anayesera kubisala kuti Mulungu asawaone.</li> <li>2. Mulungu anatemberera njoka ya chinyengoyo.</li> <li>3. Mulungu anauza Adamu ndi Hava kuti adzamva ululu ndipo adzatuluka thukuta chifukwa cha tchimo lawo.</li> <li>4. Mulungu anapanga zovala zophimba Adamu ndi Hava.</li> <li>5. Mulungu anatulutsa Adamu ndi Hava m’Munda wa Edeni.</li> </ol>
<b>MAWU OYAMBA</b>	Kodi chingachitike n’chiyani ngati titayamba ulendo popanda kudziwa njira ya kumene tikupitako? Kodi munayamba mwasohera chifukwa simunafune kudziwa kumene mukupita? Kaini sanasamale malangizo a Mulungu, zotsatira zake anasanduka wotayika ndi woyendayenda.	Funsani ophunzira kuti aganizire za nthawi imene sanamvere monga ana, ku nyumba kwavo kapena ku sukulu. Kodi iwo anamva bwanjì atachita zimenezo? Kodi iwo analandira chilango chotani?
<b>KUTSIRIZA</b>	<p><b>Perekani Nkhani ya m’Baibulo</b></p> <p><b>Kambiranani ndi Kufotokoza:</b></p> <ol style="list-style-type: none"> <li>1. Adamu ndi Hava anali ndi ana aamuna awiri. Abele anali woweta nkosa, ndipo Kaini anali mlimi wa mbewu.</li> <li>2. Mulungu analandira nsembe ya nyama yomwe Abele anabweretsa: mwanawankosa wabwino woyamba kubadwa kuchokera pa ziweto zake. Mulungu anakana nsembe ya Kaini: zina mwa mbewu zake. Kaini anakwiya ndi kuyipidwa kwambiri.</li> <li>3. Mulungu anadzudzula Kaini chifukwa cha tchimo lake komanso za kufunka kotsatira njira yoyenera ya Mulungu. Kaini sanapepese, ndiponso sanamvere Mulungu.</li> <li>4. Kaini anapha Abele, m’bale wake. Mulungu anamuthamangitsa m’dzikolo ndipo anakhala woyendayenda, kutali ndi Mulungu.</li> <li>5. Abele anadziwa kuti ankayenera kupereka mwanawankosa kwa Mulungu. Kaini sanabwere kwa Mulungu m’njira yake ya Mulungyo, ndipo analangidwa.</li> <li>6. <i>Nsembe ya Abele inali chithunzi cha nsembe imene Ambuye Yesu anapereka pa mtanda.</i></li> </ol> <p><b>Fotokozani Vesi Yoloweza ndipo limbikitsani ophunzira kuti aloweze.</b>  <b>Tsirizani Phunziro Lachinayi.</b></p> <p><b>Kuonetsa:</b> Onani FBI pa Zoonjezera A – Kuchita zinthu m’njira ya Mulungu.</p>	<p><b>Perekani Nkhani ya m’Baibulo</b></p> <p><b>Kambiranani ndi Kufotokoza:</b></p> <ol style="list-style-type: none"> <li>1. Kusamvera kwa Adamu ndi Hava kunachititsa kuti ayambe kudziwa zabwino ndi zoypa komanso kuti anali maliseche. Iwo anachita mantha ndipo anafuna kubisala Mulungu.</li> <li>2. Mulungu anafunsa Adamu ndi Hava mafunso. Iye ankafuna kuti iwo avomereze cholakwa chomwe anachita. Koma, aliyense wa iwo analoza chala mnzake. Adamu analoza chala Hava ndipo Hava analoza chala njoka.</li> <li>3. Adamu ndi Hava analandira zotsatira za kusamvera kwavo: Iwo anamva ululu, anayamba kuvutika ndipo anathamangitsidwa m’Munda wa Edeni ndi pamaso pa Mulungu.</li> <li>4. <i>Ifenso timalandira zotsatira za tchimo lathu – chifukwa Adamu anachimwa, nafenso ndife ochimwa ngati iye, ndipo tonse tidzalangidwa ndi Mulungu.</i></li> <li>5. Mulungu ndi wokoma mtima kwambiri. Iye anapereka zovala za zikopa za nyama kwa Adamu ndi Hava kuti aphimbe umaliseche wawo. <b>Aroma 6:23</b> akutiphunzitsa kuti iye anatipatsa mphatso yaulere ya moyo wosatha kudzera mwa Ambuye Yesu Khristu ngati tingamulandire kukhala Mpulumutsi wathu ndi kulapa machimo athu.</li> </ol> <p><b>Fotokozani Vesi Yoloweza ndipo limbikitsani ophunzira kuti aloweze.</b>  <b>Tsirizani Phunziro Lachinayi.</b></p> <p><b>Kuonetsa:</b> Onani FBI pa Zoonjezera A – Zotsatira za tchimo.</p>
<b>KUKUMBUTSANA</b>	<p>Pa Vesi Yoloweza, Yesu anati lye ndiye njira yokhayo ya kwa Mulungu. Kodi ndi njira zina ziti zomwe anthu amatsatira pofuna kukondweretsa Mulungu?</p> <p>Pezani pepala ndipo mulembepo Vesi Yoloweza.</p>	<ol style="list-style-type: none"> <li>1. Kodi tikuphunzira chiyani za khalidwe la Mulungu pa phunziro limeneli?</li> <li>2. Lumikizani phunziroli ndi Aroma 5:12. Popeza Adamu ndi Hava sanamvere, ife tonse timabadwa ochimwa.</li> <li>3. Funsani ophunzira aganizire zitsanzo za kusamvera malamulo a Mulungu m’miyoyo yathu. Kodi izi zimakhudza motani 1) ife ndi 2) anthu ena?</li> </ol>
<b>KHALANI MOYO UMENEWU</b>	<p><b>Zomwe tikuphunzira m’phunziroli:</b></p> <ol style="list-style-type: none"> <li>1. Lowezani Vesi Yoloweza.</li> <li>2. Kodi inu mukutsatira Yesu, amene ndi njira yokhayo ya kwa Mulungu?</li> </ol>	<p><b>Zomwe tikuphunzira m’phunziroli:</b></p> <ol style="list-style-type: none"> <li>1. Tikuenera kupepesa kwa Mulungu kuti lye atikhululukire ndi kutipanga kukhala atsopano. Motero ife monga Akhristu tidzakhala moyo wokondweretsa Mulungu ndi wotsatira malamulo ake.</li> <li>2. Pemphani Mulungu kuti akupatseni mphamu zumumvera ndipo muyamikeni chifukwa cha kukoma mtima kwake komwe kumachititsa kuti atikhululukire tikalephera komanso kudziwa kuti takhululukidwa. (<i>Onani 1 Yohane 1:9.</i>)</li> </ol>

	<b>A2 – KALASI Lachitatu</b> Phunziro Loyamba – Nowa ndi Chigumula Mutu – Kupanga chombo	<b>A2 – KALASI Yachinayi</b> Phunziro Loyamba – Kaini ndi Abele Mutu – Kupembedza Mulungu
	<p><b>Ndime Yowerenga:</b> <i>Genesis 6:5-22</i>  <b>Vesi Yoloweza:</b> <i>Genesis 6:8</i></p> <p><b>Ife tikuphunzira kuti:</b></p> <ol style="list-style-type: none"> <li>Mulungu ndi Woyerwa. Khalidwe la uchimo la anthu limamvetsa chisoni Mulungu.</li> <li>Mulungu anaganiza zopulumutsa Nowa. Mulungu anauza Nowa kuti apange Chombo kuti apulumutse iye, banja lake, nyama ndi mbalame, zonse ziwiriziwiri.</li> <li>Nowa anachita chomwe Mulungu anamuza. Nowa anali ndi chikhulupiro mwa Mulungu ndipo anamvera.</li> </ol>	<p><b>Ndime Yowerenga:</b> <i>Genesis 4:1-16</i>  <b>Vesi Yoloweza:</b> <i>Ahebri 11:4</i></p> <p><b>Ife tikuphunzira kuti:</b></p> <ol style="list-style-type: none"> <li>Abele anafika pamaso pa Mulungu m'njira imene Mulungu ankafunira. Mulungu analandira nsembe ya Abele.</li> <li>Kaini anafika pamaso pa Mulungu m'njira yake. Mulungu anakana nsembe yake.</li> <li>Mulungu anapereka NJIRA IMODZI yokha imene ife tingafikire pamaso pake.</li> </ol>
<b>MAWU OYAMBA</b>	Perekani malangizo opangira chinthu, kapena njira yopangira keke. Auzeni kufunika kotsatira malangizo pomanga kapena kupanga chinthu. Fotokozani kuti Mulungu anamupatsa Nowa malangizo amene ankayenera kuwatsatira ndi kuti Nowa anatsatira malangizo onse a Mulungu.	Perekani m'ndandanda wa zochitika zomwe zimafunka kutsatira malangizo. Kodi chimachitika n'chiyani tikapanda kutsatira? Ganizani momwe ife tingapezere malangizo a Mulungu.
<b>KUTSIRIZA</b>	<p><b>Perekani Nkhani ya m'Baibulo</b></p> <p><b>Kambiranani ndi Kufotokoza:</b></p> <ol style="list-style-type: none"> <li>Anthu pa dziko lapansi anayipa kwambiri. Khalidwe lawo lauchimo ndi kusamvera kwavo kunachititsa Mulungu kumva chisoni kwambiri.</li> <li>Mulungu anatsimikiza zoononga anthu pamodzi ndi nyama zonse zomwe lye analenga.</li> <li>Nowa anali wosiyana ndi anthu ena onse. lye anakondweretsa Mulungu. lye anali wosiyana ndi anthu onse chifukwa anali wolungama ndipo ankakonda kumvera Mulungu.</li> <li>Mulungu anachenjeza Nowa kuti lye ankafuna kuononga anthu onse ndi zamoyo zonse ndi madzi achigumula chifukwa anadzaza dziko lapansi ndi za chiwawa.</li> <li>Mulungu anamupatsa Nowa malangizo apadera omuthandiza kukonzekera. lye anamuza Nowa momwe akuyenera kupangira Chombo kuti chipulumutse Nowa, banja lake ndi zamoyo zonse ziwiriziwiri.</li> <li>Nowa anakhulupirira Mulungu ndipo anatsatira malangizo onse.</li> </ol> <p><b>Fotokozani Vesi Yoloweza ndipo limbikitsani ophunzira kuti aloweze.</b>  <b>Tsirizani Phunziro Loyamba.</b></p> <p><b>Kuonetsa:</b> Onani FBI pa Zoonjezera A – Kupanga Chombo.</p>	<p><b>Perekani Nkhani ya m'Baibulo</b></p> <p><b>Kambiranani ndi Kufotokoza:</b></p> <ol style="list-style-type: none"> <li>Adamu ndi Hava anali ndi ana aamuna awiri. Abele anali m'busa wa ziweto, ndipo Kaini anali mlimi wa mbewu.</li> <li>Mulungu analandira nsembe ya nyama yomwe Abele anabweretsa: mwanawankhosa woyamba kubadwa wabwino kwambiri pa ziweto zake. Mulungu anakana nsembe ya Kaini ya mbewu zake.</li> <li>Kaini anakwiya ndipo anadzimva kukanidwa.</li> <li>Mulungu anachenjeza Kaini za tchimo lake ndipo anamuza za kufuna kotsatira njira yoyenera ya Mulungu. Kaini sanapepese, ndiponso sanamvere Mulungu.</li> <li>Kaini anapha m'bale wake Abele. Mulungu anamuthamangitsa m'dzikolo ndipo anakakhala woyendayenda kutali, kutali ndi pamaso pa Mulungu.</li> <li>Abele anamvetsetsa kuti ankayenera kuperaka mwanawankhosa kwa Mulungu. Kaini sanafike pamaso pa Mulungu m'njira ya Mulungu, ndipo analangidwa.</li> <li>Lero, anthu amaganiza kuti pali njira zambiri zopitira kwa Mulungu, koma Ambuye Yesu anatiphunzitsa kuti pali NJIRA IMODZI yokha - <i>Yohane 14:6</i>. Yesu ndi "Mwanawankhosa wa Mulungu" amene anapereka moyo wake kukhala nsembe ya ife tonse.</li> </ol> <p><b>Fotokozani Vesi Yoloweza ndipo limbikitsani ophunzira kuti aloweze.</b>  <b>Tsirizani Phunziro Loyamba.</b></p> <p><b>Kuonetsa:</b> Onani FBI pa Zoonjezera A – Kupembedza Mulungu.</p>
<b>KUKUMBUTSANA</b>	Onetsani chithunzi cha Chombo cha Nowa ndi nyama zonse. Perekani mwayi kwa ophunzira kuti apange "malamulo/malangizo" awo oti awatsatire pa za momwe akufunira kuti aonetsera zinthu zowo.	Werengani Vesi Yoloweza, <i>Ahebri 11:4</i> . Kodi vesiyi ikufotokoza chiyani za kusiyana kwa Abele ndi Kaini?
<b>KHALANI MOYO UMENEWU</b>	<p><b>Zomwe tikuphunzira m'phunziroli:</b></p> <p>Nowa anadalira Mulungu ndipo anachita zonse zimene Mulungu anamulamula kuti achite. Kodi ife tingakhale bwanji ndi chikhulupiro mwa Mulungu? Kodi inu mumamudalira? Nowa anali ndi chikhulupiro mwa Mulungu ndipo Mulungu anamupulumsuta.</p>	<p><b>Zomwe tikuphunzira m'phunziroli:</b></p> <ol style="list-style-type: none"> <li>Kodi tikuphunzira chiyani kuchokera pa moyo ndi zochita za Abele ndi Kaini?</li> <li>Kodi maphunziro amenewa tingawagwiritse ntchito motani pa miyoyo yathu lero?</li> <li>Dziwani kuti si zomwe timachita zimene zikatifikitse kumwamba, koma ndi zimene Ambuye Yesu <b>anatichitira</b> ife.</li> </ol>

	<p><b>A2 – KALASI Lachitatu</b>  <b>Phunziro Lachiwiri – Nowa ndi Chigumula</b>  <b>Mutu – Kulowa m'Chombo</b></p>	<p><b>A2 – KALASI Yachinayi</b>  <b>Phunziro Lachiwiri – Enoki ndi Nowa</b>  <b>Mutu – Kuyenda ndi Mulungu</b></p>
	<p><b>Ndime Yowerenga:</b> <i>Genesis 7:1-20</i>  <b>Vesi Yoloweza:</b> <i>Genesis 7:5</i></p> <p><b>Ife tikuphunzira kuti:</b></p> <ol style="list-style-type: none"> <li>1. Mulungu anaperekira njira yopulumutsira Nowa ndi banja lake.</li> <li>2. Nowa anali ndi chikhulupiro mwa Mulungu ndipo anachita zomwe Mulungu anamuza kuti achite.</li> </ol>	<p><b>Ndime Yowerenga:</b> <i>Genesis 5:21-32; 6:1-15</i>  <b>Vesi Yoloweza:</b> <i>Ahebri 11:5</i></p> <p><b>Ife tikuphunzira kuti:</b></p> <ol style="list-style-type: none"> <li>1. Enoki ndi mdzukulu wake, Nowa, anali pa ubale wabwino ndi Mulungu.</li> <li>2. Anthu awiriwa anali osiyana kwambiri ndi anthu ena onse chifukwa cha ubale wawo ndi Mulungu.</li> </ol>
<b>MAWU OYAMBA</b>	Kodi munayamba mwakhalapo pa ulendo ndi banja lanu? Nanga munakonzekera motani? Kambiranani zina zomwe Nowa anachita, iye ndi banja lake ndi nyama, asanalowe mu Chombo.	Kukhala ndi ubale ndi Mulungu kukuyenera kutipanga ife kukhala osiyana ndi aliyense! Kodi Mkhristu akuyenera kukhala wosiyana motani ndi anthu ena? Lembanzi zotisyanitsa zofunika kwambiri.
<b>KUTSIRIZA</b>	<p><b>Perekani Nkhani ya m'Baibulo</b></p> <p><b>Kambiranani ndi Kufotokoza:</b></p> <ol style="list-style-type: none"> <li>1. Mulungu anachenjeza Nowa kuti pakatha masiku asanu ndi awiri, iye adzatumiza madzi achigumula.</li> <li>2. Mulungu anaiza Nowa kuti alowetse nyama m'Chombo kuti zipulumuke nthawi ya chigumula.</li> <li>3. Tsiku limeneli, Nowa anali ndi zaka 600, pa 17 mwezi wachiwiri, iye anatenga banja lake ndi nyama, monga mmene Mulungu anamulamulira ndi kulowa m'Chombo. Madzi achigumula anabwera tsiku lachisanu ndi chiwiri, monga momwe ananenera Mulungu.</li> <li>4. Mulungu anatseka khomo la Chombo, Nowa, banja lake ndi nyama, atalowa, kuti atetezedwe m'kati mwa Chombomo. Nowa yekha pamodzi ndi banja lake ndi nyama ndiye anapulumuka pa nthawi ya madzi achigumula choopsachi. Mvula inakhala ikubwera kwa masiku makumi anayi! Madzi anakwera mamita 7 pamwamba pa mapiri ataliatali.</li> </ol> <p><b>Fotokozani Vesi Yoloweza ndipo limbikitsani ophunzira kuti aloweze.</b>  <b>Tsirizani Phunziro Lachiwiri.</b></p> <p><b>Kuonetsa:</b> Onani FBI pa Zoonjezera A – Nowa ndi chigumula.</p>	<p><b>Perekani Nkhani ya m'Baibulo</b></p> <p><b>Kambiranani ndi Kufotokoza:</b></p> <ol style="list-style-type: none"> <li>1. Enoki anakhala ndi moyo zaka 365, ali pa ubale wabwino ndi Mulungu.</li> <li>2. Baibulo limati Enoki sanamwalire ngati anthu ena onse. Kumapeto kwa moyo wake anasowa, chifukwa Mulungu anamutenga kupita naye Kumwamba.</li> <li>3. Nowa anali mdzukulu wa Enoki. Monga Enoki, naye Nowa anali pa ubale wabwino ndi Mulungu ndipo anali munthu wolungama, kusiyana ndi anthu oyipa omwe iye anali pakati pavo.</li> <li>4. Kuchimwa kwa anthu a nthawi ya Nowa kunamvetsa chisoni Mulungu. Iye anaganiza zowalanga ndi madzi achigumula, koma anapulumutsa Nowa.</li> <li>5. Mulungu analangiza Nowa momwe akanapangira Chombo kuti apulumuke iye ndi banja lake ku madzi achigumula.</li> <li>6. Monga mmene Mulungu analangira Adamu ndi Hava chifukwa cha kuchimwa kwawo, chonchonso Mulungu analanga anthu a nthawi ya Nowa chifukwa sankalingalira za Mulungu. (<i>Genesis 6:5-7</i>)</li> </ol> <p><b>Fotokozani Vesi Yoloweza ndipo limbikitsani ophunzira kuti aloweze.</b>  <b>Tsirizani Phunziro Lachiwiri.</b></p> <p><b>Kuonetsa:</b> Onani FBI pa Zoonjezera A – Kuyenda ndi Mulungu.</p>
<b>KUKUMBUTSANA</b>	Ganizani choti muchite! Jambulani chithunzi cha Nowa, banja lake, nyama zili m'Chombo, chikuyandama pa madzi. Dzina la chojambula chanu: "Kupulumutsidwa ndi Mulungu."	<ol style="list-style-type: none"> <li>1. Lembanzi zinthu zofanana pakati pa anthu a nthawi ya Nowa ndi anthu amasiku ano.</li> <li>2. Kodi Enoki ndi Nowa anali anthu otani?</li> <li>3. Kodi chinawachititsa kukhala osiyana ndi anthu onse chinali chiyani?</li> </ol>
<b>KHALANI MOYO UMENEWU</b>	<p><b>Zomwe tikuphunzira m'phunziroli:</b></p> <ol style="list-style-type: none"> <li>1. Mulungu anakonda Nowa ndipo anamupatsa njira yoti akonzekere, njira yoti apulumikire ku madzi achigumula. Choyamba Nowa ankayenera kumvera malangizo a Mulungu.</li> <li>2. Mulungu akutifunsa ife kuti tikonzekere chiweruzo. Iye akufuna kuti tikhulupiro Ambuye Yesu Khristu amene anafa pa mtanda kuti atipulumutse. Kodi inu munamukhulupirira? Kodi ndinu wokonzeka kupulumutsidwa?</li> </ol>	<p><b>Zomwe tikuphunzira m'phunziroli:</b></p> <ol style="list-style-type: none"> <li>1. Onani m'ndandanda wa makhalidwe amene amachititsa Akhristu kukhala osiyana ndi anthu ena onse ndipo muganizire za Enoki ndi Nowa pa ubale wawo ndi Mulungu.</li> <li>2. Pemphani Mulungu kuti akuthandizeni kumukhulupirira ndi kuyenda m'njira yake sabata ino. Inu mutha kusankha khalidwe limodzi la Mkhristu wokhulupirika ndi kupempha Mulungu kuti mukhale nalo.</li> </ol>

	<p><b>A2 – KALASI Lachitatu</b>  <b>Phunziro Lachitatu – Nowa ndi Chigumula</b>  <b>Mutu – Kupulumuka mu chombo</b></p>	<p><b>A2 – KALASI Yachinayi</b>  <b>Phunziro Lachitatu – Nowa ndi Madzi a Chigumula</b>  <b>Mutu – Kugwira ntchito ya Mulungu</b></p>
	<p><b>Ndime Yowerenga:</b> <i>Genesis 8:1-22</i>  <b>Vesi Yoloweza:</b> <i>Genesis 8:1</i></p> <p><b>Ife tikuphunzira kuti:</b></p> <ol style="list-style-type: none"> <li>1. Mulungu anakumbukira ndipo anayang'ana Nowa ndi banja lake pamodzi ndi zomwe zinali mu Chombo.</li> <li>2. Nowa anayamika kwambiri Mulungu chifukwa anamupulumsa m'Chombo.</li> <li>3. Mulungu analonjeza kuti sadzaononganso zamoyo zonse</li> </ol>	<p><b>Ndime Yowerenga:</b> <i>Genesis 6:14-22; 7:1-24</i>  <b>Vesi Yoloweza:</b> <i>Ahebri 11:7</i></p> <p><b>Ife tikuphunzira kuti:</b></p> <ol style="list-style-type: none"> <li>1. Mulungu anapereka malangizo omveka bwino kwa Nowa a kamangidwe ka Chombo.</li> <li>2. Nowa anamvera malangizo a Mulungu ndipo zotsatira zake, iye ndi banja lake anapulumsa.</li> <li>3. Chombo ndi chithunzi cha chipulumsa chimene Mulungu amapereka kwa amene amukhulupirira.</li> </ol>
<b>MAWU OYAMBA</b>	<ol style="list-style-type: none"> <li>1. Lembari mathandizo onse amene munalandira kuchokera ku banja lanu ndi anzanu kapena aphunzitsi anu.</li> <li>2. Lembari njira zonse zimene Mulungu amatithandizira tsiku ndi tsiku.</li> <li>3. Kumbutsani gulu kufunika kwa kuthokoza banja lathu, anzathu ndi aphunzitsi athu pa zonse zimene amatichitira. Ndipo choposa zonsezi, tikuyenera kuthokoza Mulungu amene amatipulumsa tikamukhulupirira.</li> </ol>	<p>Kambiranani ndi anzanu malangizo a chitezezo pa sukulu zanu. Kodi ophunzira amatsatiradi zimenezi? N'chifukwa chiyani amatero? N'chifukwa chiyani satero? N'chifukwa chiyani kwa Nowa kunali kofunika kumvera malangizo onse amene Mulungu anamupatsa?</p>
<b>KUTSIRIZA</b>	<p><b>Perekani Nkhani ya m'Baibulo</b></p> <p><b>Kambiranani ndi Kufotokoza:</b></p> <ol style="list-style-type: none"> <li>1. Mulungu anakumbukira Nowa, banja lake ndi nyama mu Chombo. Iye anatumiza mphepo pa dziko lapansi ndipo madzi a chigumula anayamba kuphwa.</li> <li>2. Patatha masiku 150 (miyezi isanu) Chombo chinayima pa Phiri la Ararati. Patathanso miyezi iwiri ndi theka, madzi anapitirira kuphwa ndipo mapiri ena anayamba kuonekanso.</li> <li>3. Patapitanso masiku ena makumi anayi, Nowa anatsekula zenera la Chombo ndipo anatulutsa khwangwala, amene sanabwerereno. Kenaka anatulutsa nkhunda. Nkhunda sinapeze malo owuma, choncho inabwerera. Patapitanso masiku ena asanu ndi awiri, Nowa anatulutsanso nkhunda m'Chombo. Nthawi imeneyi nkhunda inabwerere koma itatenga tsamba la olivi. Motero Nowa anadziwa kuti madzi a chigumula aphwa tsopano. Patathanso masiku ena asanu ndi awiri, anatumiza nkhunda ija, ndipo sinabwerereno.</li> <li>4. Potsiriza pake, patapita miyezi khumi ndi iwiri ndi theka chigumula chitachitika, dziko lapansi linaumanso!</li> <li>5. Mulungu anaauza Nowa kuti atuluke m'Chombo, iye, banja lake pamodzi ndi nyama zonse.</li> <li>6. Nowa anali woyamika kwambiri. Iye anamanga guwa lansembe ndi kupereka nsembe yopseresa kwa Mulungu. <i>Fotokozani momwe ankayamikira Mulungu nthawi imeneyi.</i></li> <li>7. Mulungu anakondwera ndi nsembe ya Nowa. Iye analonjeza kuti sadzaononganso zamoyo zonse.</li> </ol> <p><b>Fotokozani Vesi Yoloweza ndipo limbikitsani ophunzira kuti a loweze.</b></p> <p><b>Tsirizani Phunziro Lachitatu.</b></p> <p><b>Kuonetsa:</b> Onani FBI pa Zoonjezera A – Kupulumuka mu chombo.</p>	<p><b>Perekani Nkhani ya m'Baibulo</b></p> <p><b>Kambiranani ndi Kufotokoza:</b></p> <ol style="list-style-type: none"> <li>1. Mulungu anamupatsa Nowa malangizo omveka bwino a momwe angapangire Chombo pokonzekera madzi a chigumula amene ankawatumiza.</li> <li>2. Mulungu anachenjeza Nowa za tsatanetsatane wa chigumula.</li> <li>3. Mulungu analonjeza kupulumsa Nowa, banja lake ndi nyama.</li> <li>4. Mulungu anamupatsa Nowa malangizo a momwe angapulumsire nyama. Nowa, banja lake pamodzi ndi nyama analowa m'Chombo ndipo Mulungu anatseka pa khomo.</li> <li>5. Madzi a chigumula anatenga masiku makumi anayi akubwerabe ndipo chamoyo chilichonse chimene chinali kunja kwa Chombo chinafa ndi mvula yamphamvysi.</li> <li>6. Nowa yekha ndi banja lake pamodzi ndi nyama zimene zinali m'Chombo anapulumsa. Mulungu anawateteza ku madzi a chigumula.</li> <li>7. Mulungu anapereka Mpulumsi, kuti aliyense amene akhululupirira iye adzapulumsi ku chilango cha Mulungu. (<i>Onani Yohane 3:36.</i>)</li> </ol> <p><b>Fotokozani Vesi Yoloweza ndipo limbikitsani ophunzira kuti a loweze.</b></p> <p><b>Tsirizani Phunziro Lachitatu.</b></p> <p><b>Kuonetsa:</b> Onani FBI pa Zoonjezera A – Kugwira ntchito ya Mulungu.</p>
<b>KUKUMBUTSANA</b>	<p>Pangani posita ndipo mulembepo zinthu zimene tikuyenera kumuthokozena Mulungu, makamaka chipulumsa chathu.</p>	<ol style="list-style-type: none"> <li>1. Kodi tikuphunzira chiyani za khalidwe la Nowa ndi la Mulungu m'nhkani imeneyi?</li> <li>2. Lembari mawu amene mungagwiritsa ntchito pofotokoza khalidwe la Nowa ndi la Mulungu.</li> </ol>
<b>KHALANI MOYO UMENEWU</b>	<p><b>Zomwe tikuphunzira m'phunziroli:</b></p> <ol style="list-style-type: none"> <li>1. Mulungu anapulumsa Nowa ndipo anamusamira. Nowa anayamika Mulungu.</li> <li>2. Mulungu angathe ndipo ndi wokonzeka kutipulumsa ndi kutisamalira. Ife tikuyenera kumukhulupirira ndi kumuyamika.</li> </ol>	<p><b>Zomwe tikuphunzira m'phunziroli:</b></p> <ol style="list-style-type: none"> <li>1. Werengani Vesi Yoloweza. Kodi ife tingatsatire motani chitsanzo cha Nowa m'miyoyo yathu?</li> <li>2. Kodi izi zingakhudze motani anthu amene atiyandikira ife?</li> </ol>

	<p><b>A2 – KALASI Lachitatu</b>  <b>Phunziro Lachinayi – Nowa ndi Chigumula</b>  <b>Mutu – Kunja kwa chombo</b></p>	<p><b>A2 – KALASI Yachinayi</b>  <b>Phunziro Lachinayi – Nowa ndi Banja Lake</b>  <b>Mutu – Kupembedza Mulungu</b></p>
	<p><b>Ndime Yowerenga:</b> <i>Genesis 9:7-17</i>  <b>Vesi Yoloweza:</b> <i>Genesis 9:15</i></p> <p><b>Ife tikuphunzira kuti:</b></p> <ol style="list-style-type: none"> <li>1. Mulungu anachita pangano la lonjezo ndi Nowa. Iye analonjeza kuti sadzaononganso zamoyo zonse pa dziko lapansi ndi madzi a chigumula.</li> <li>2. Mulungu anayika utawaleza kuti ukhale chikumbutso cha lonjezo lake.</li> </ol>	<p><b>Ndime Yowerenga:</b> <i>Genesis 8:1-22; 9:11-16</i>  <b>Vesi Yoloweza:</b> <i>Aefeso 2:8</i></p> <p><b>Ife tikuphunzira kuti:</b></p> <ol style="list-style-type: none"> <li>1. Mulungu anakumbukira Nowa, banja lake ndi nyama m'chombomo.</li> <li>2. Nowa anayamika ndi kupembedza Mulungu asanayambe kuchita chilichonse atatuluka m'Chombomo.</li> <li>3. Mulungu analonjeza kuti sadzaononganso anthu okhala pa dziko lapansi ndi madzi a chigumula.</li> </ol>
<b>MAWU OYAMBA</b>	<p>Khalani awiriawiri ndipo kambiranani za mitundu yosiyana ya malonjezo amene anthu amachita. Kodi anthu nthawi zonse amasunga malonjezo awo? N'chifukwa chiyani sasunga? Kodi tingatsimikize bwanji kuti Mulungu adzasunga malonjezo ake?</p>	<p>Awiriawiri: Kambiranani zopanga makadi othokoza Mulungu. N'chifukwa chiyani anthu amatumizirana makadiwa? Kodi inu munatumiza yanu? Chifukwa chiyani? Lembanu zina mwa zinthu zomwe mungayamike nazo tsiku ndi tsiku.</p>
<b>KUTSIRIZA</b>	<p><b>Perekani Nkhani ya m'Baibulo</b></p> <p><b>Kambiranani ndi Kufotokoza:</b></p> <ol style="list-style-type: none"> <li>1. Mulungu anauza Nowa ndi banja lake kuti achulukane pa dziko lapansi.</li> <li>2. Mulungu anachita lonjezo lapadera lomwe limatchedwa pangano ndi Nowa ndi ana ake aamuna pamodzi ndi nyama zonse ndi zamoyo zonse za pa dziko lapansi.</li> <li>3. Mulungu analonjeza kuti sadzaononganso dziko lapansi pamodzi ndi zamoyo zonse ndi madzi a chigumula.</li> <li>4. Mulungu anayika utawaleza m'mitambo kukhala chikumbutso cha pangano lake lamuyaya. Pangano limeneli silidzatha. Iye sadzaphwanya lonjezo lake.</li> <li>5. <i>Nthawi zonse tikaona utawaleza umatikumbutsa kuti Mulungu amasunga lonjezo lake nthawi zonse.</i></li> </ol> <p><b>Fotokozani Vesi Yoloweza ndipo limbikitsani ophunzira kuti aloweze.</b>  <b>Tsirizani Phunziro Lachinayi.</b></p> <p><b>Kuonetsa:</b> Onani FBI pa Zoonjezera A – Kunja kwa chombo.</p>	<p><b>Perekani Nkhani ya m'Baibulo</b></p> <p><b>Kambiranani ndi Kufotokoza:</b></p> <ol style="list-style-type: none"> <li>1. Mulungu anamupatsa Nowa malangizo omveka bwino a momwe angapangire Chombo ndi momwe angachitire pokonzekera kupulumuka pa nthawi ya chigumula chomwe iye ankachitumiza.</li> <li>2. Mulungu analonjeza kupulumutsa Nowa, banja lake ndi nyama m'Chombo.</li> <li>3. Madzi a chigumula anabwera kwa masiku makumi anayi. Nowa yekha pamodzi ndi banja lake pamodzi ndi nyama zomwe zinali m'Chombomo, anapulumuka.</li> <li>4. Chigumula chinatha ndipo madzi anayamba kuphwa pang'ono pang'ono. Chombo chinakayima pa Phiri la Ararati.</li> <li>5. Patapata masiku makumi anayi, Nowa anatulutsa khwangwala m'Chombomo, iye ankangouluka mpaka madzi anawuma pa dziko lapansi. Kenaka anatulutsa nkhunda. Nkhunda sinapeze malo owuma otera ndipo inabwerera, koma patapitanso masiku asanu ndi awiri, Nowa anayitulutsanso. Nthawi iyi inabweretsa nthambi ya olivi. Nowa atayitulutsanso, nkhunda sinabwerereno. Dzikolo linawuma.</li> <li>6. Mulungu anauza Nowa ndi banja lake kuti atuluke m'Chombo ndi kuti achulukane ndi kudzaza dziko lapansi.</li> <li>7. Chinthu choyamba chomwe Nowa anachita pamene anatuluka m'Chombo chinali kupereka nsembe kwa Mulungu.</li> <li>8. Mulungu anachita lonjezo lapadera lotchedwa pangano ndi Nowa ndi ana aamuna ndiponso ndi nyama zonse ndi zamoyo zonse pa dziko lapansi</li> <li>9. Mulungu analonjeza kuti sadzaononganso dziko lapansi ndi zolengedwa zonse ndi madzi a chugumula.</li> <li>10. Mulungu anayika utawaleza m'mitambo monga chikumbutso cha pangano lake lamuyaya. Iye sadzaphwanya lonjezo lake.</li> </ol> <p><b>Fotokozani Vesi Yoloweza ndipo limbikitsani ophunzira kuti aloweze.</b>  <b>Tsirizani Phunziro Lachinayi.</b></p> <p><b>Kuonetsa:</b> Onani FBI pa Zoonjezera A – Kupembedza Mulungu.</p>
<b>KUKUMBUTSANA</b>	<p>Ganizirani chopanga! Jambulani pa pepala utawaleza. Upatseni dzina: "Mulungu amasunga lonjezo kwamuyaya!"</p>	<p>Kambiranani m'magulu kenaka mudzafotokozere gulu lone: Kodi tikuphunzira chiyani za kuyamika Mulungu ndi kupembedza?</p>
<b>KHALANI MOYO UMENEWU</b>	<p><b>Zomwe tikuphunzira m'phunziroli:</b>  Lonjezo la Mulungu kwa Nowa ndi lamuyaya. Mulungu amasunga malonjezo ake kwamuyaya! Kodi izi zikuyenera kusintha motani miyoyo yathu? Onani pa <i>Tito 1:2</i>.</p>	<p><b>Zomwe tikuphunzira m'phunziroli:</b>  Nowa anayamika Mulungu chifukwa cha chipulumutso chake. Kodi ifeyo tingachite chiyani pofuna kusonyeza kuyamika kwathu chifukwa cha madalitso ake pa moyo wathu? Onani pa <i>Afilipi 4:6</i>.</p>

	A3 – KALASI Lachitatu Phunziro Loyamba – Moyo wa Petulo Mutu – Yesu ayitana Petulo	A3 – KALASI Yachinayi Phunziro Loyamba – Petulo Mutu – Mayitanidwe ake
	<p><b>Ndime Yowerenga:</b> <i>Mateyu 4:17-22</i>  <b>Vesi Yoloweza:</b> <i>Mateyu 4:19</i></p> <p><b>Ife tikuphunzira kuti:</b></p> <ol style="list-style-type: none"> <li>1. Yesu amayitana anthu kuti amutsatire.</li> <li>2. Kutsatira Yesu zimatanthauza kukhala ndi chikhulupiriro mwa lye komanso kutembenuka mtima ndi kusiyat chimo.</li> </ol>	<p><b>Ndime Yowerenga:</b> <i>Mateyu 4:17-22; Yohane 1:35-42</i>  <b>Vesi Yoloweza:</b> <i>Mateyu 4:19</i></p> <p><b>Ife tikuphunzira kuti:</b></p> <ol style="list-style-type: none"> <li>1. Andreya ndi Yohane, ndiye anayamba kukumana ndi Yesu kenaka ndi kukhala ophunzira ake.</li> <li>2. Andreya anabweretsa Petulo kwa Yesu.</li> <li>3. Iwo anazindikira kuti Yesu anali Mesiya ndi Mpulumutsi.</li> </ol>
MAWU OYAMBA	Kambiranani zomwe zimachitika m'matimu kapena pa ntchito za anthu amene amachitira zinthu pamodzi. Yesu anayamamba utumiki wake ndipo ankafuna anthu amene akanawaphunzitsa kuti adzagwire ntchito yake lye akadzapita. Petulo ndi Andreya anali asodzi, ndipo Yesu anawayitana kuti akhale "asodzi a anthu."	<ol style="list-style-type: none"> <li>1. Kambiranani zomwe anthu amachita kuti akhale masapota kapena otsatira timu ya mpira kapena woyimba ndi ena ambiri.</li> <li>2. Fotokozani za Yesu, makhalidwe ake. mawu ake ndi zomwe zinabweretsa anthu kwa lye.</li> <li>3. Fotokozaniso kuti Yesu anasankha anthu ena kuti akhale ophunzira ake.</li> </ol>
KUTSIRIZA	<p><b>Perekani Nkhani ya m'Baibulo</b></p> <p><b>Kambiranani ndi Kufotokoza:</b></p> <ol style="list-style-type: none"> <li>1. Uthenga umene Yesu analalikira. (4:17)</li> <li>2. Yesu anaona Simoni Petulo ndi Andreya akuponya makoka awo.</li> <li>3. Yesu anayitana asodzi amene ankagwira ntchito molimbika, monga gulu, ndipo lye anadziwa kuti adzawaphunzitsa kugwira ntchito yake.</li> <li>4. Iwo anamvera nthawi yomwego mayitandidwe ake.</li> <li>5. Yesu anayitananso Yakobo ndi Yohane ndipo iwonso nthawi yomwego anamvera. Awa anali ophunzira ake oyamba.</li> </ol> <p><b>Fotokozani Vesi Yoloweza ndipo limbikitsani ophunzira kuti aloweze.</b></p> <p><b>Tsirizani Phunziro Loyamba.</b></p> <p><b>Kuonetsa:</b> Onani FBI pa Zoonjezera A – Yesu ayitana Petulo.</p>	<p><b>Perekani Nkhani ya m'Baibulo</b></p> <p><b>Kambiranani ndi Kufotokoza:</b></p> <ol style="list-style-type: none"> <li>1. Yohane M'batizi anati Yesu anali Mwanawankhosa wa Mulungu ndipo Andreya ndi mnzake anazindikira kuti anali Mesiya. (<i>Yohane 1:35, 41</i>)</li> <li>2. Andreya anabweretsa Petulo kwa Yesu.</li> <li>3. Sizinali zodabwitsa atakumana ndi Yesu nthawi imene ankasodza, ndipo anawayitana kuti amutsatire, nthawi yomwe anamvera.</li> <li>4. <i>Ganizirani chitsanzo cha Andreya chokachitira umboni.</i></li> <li>5. <i>Ganizirani za kufunika koti munthu pa yekha kuti akumane ndi Yesu, amukhulupirire ndi kupita kukaiza ena za lye.</i></li> </ol> <p><b>Fotokozani Vesi Yoloweza ndipo limbikitsani ophunzira kuti aloweze.</b></p> <p><b>Tsirizani Phunziro Loyamba.</b></p> <p><b>Kuonetsa:</b> Onani FBI pa Zoonjezera A – Mayitanidwe ake.</p>
KUKUMBUTSANA	<p>Mafunso kwa ophunzira:</p> <ol style="list-style-type: none"> <li>1. N'chifukwa chiyani Yesu anayitani anthu amenewa?</li> <li>2. Kodizikutanthauza chiyani lero kumvera mayitanidwe a Mulungu?</li> <li>3. Kodi ndi ziti zomwe zimachititsa kumvera Mulungu kukhala kovuta?</li> <li>4. Kodi Yesu anawalonjeza chiyani? (<i>Onani 4:19</i>.)</li> </ol>	<p>Mafunso kwa ophunzira:</p> <ol style="list-style-type: none"> <li>1. Kodi Yesu anali ndi chikonzero chotani pa ophunzira awa?</li> <li>2. Kodi mukudziwa bwanji kuti Mulungu ali ndi chikonzero ndi moyo wanu?</li> <li>3. Kodi phindu lodziwa chikonzero cha Mulungu ndi lotani?</li> <li>4. Kodi ife tingazindikire bwanji chikonzero cha Mulungu pa miyoyo yathu, ndipo tingavomereze motani?</li> </ol>
KHALANI MOYO UMENEWU	<p><b>Zomwe tikuphunzira m'phunziroli:</b></p> <ol style="list-style-type: none"> <li>1. Kambiranani za tanthauzo la kutembenuka mtima lero.</li> <li>2. Lembanji pemphero la kutembenuka mtima ndipo mulitaye.</li> <li>3. Fufuzani za mayitanidwe a Akhristu ena otchuka lero, monga David Livingstone.</li> <li>4. Kodi inu mungasiye kapena kutaya chilichonse kuti mutsatire Yesu?</li> </ol>	<p><b>Zomwe tikuphunzira m'phunziroli:</b></p> <ol style="list-style-type: none"> <li>1. Kambiranani njira zomwe tingachitire umboni Mulungu lero.</li> <li>2. Lembanji mayina ena a Yesu kuchokera mu ndime zowerenga za m'baibulo.</li> </ol>

	<p><b>A3 – KALASI Lachitatu</b>  <b>Phunziro Lachiwiri – Moyo wa Petulo</b>  <b>Mutu – Kugwira nsomba zambiri</b></p>	<p><b>A3 – KALASI Yachinayi</b>  <b>Phunziro Lachiwiri – Petulo</b>  <b>Mutu – Mavuto ake</b></p>
	<p><b>Ndime Yowerenga:</b> <i>Luka 5:1-11</i>  <b>Vesi Yoloweza:</b> <i>Aroma 3:23</i></p> <p><b>Ife tikuphunzira kuti:</b></p> <ol style="list-style-type: none"> <li>1. Ophunzira anaphunzira kumvera Yesu.</li> <li>2. Yesu ndi wamkulu ndi wamphamvu ndipo angathe kuchita zodabwitsa zazikulu.</li> <li>3. Mulungu atha kugwiritsa ntchito munthu aliyense amene watembenuka mtima.</li> </ol>	<p><b>Ndime Yowerenga:</b> <i>Mateyu 14:22-33</i>  <b>Vesi Yoloweza:</b> <i>Mateyu 14:33</i></p> <p><b>Ife tikuphunzira kuti:</b></p> <ol style="list-style-type: none"> <li>1. Ophunzira anazindikira kuti Yesu anali Mwana wa Mulungu, ndi kuti ali wokonzeka kuthetsa mantha athu.</li> <li>2. Kudalira Yesu kumathandiza kuthetsa namondwe wa moyo wathu.</li> </ol>
<b>MAWU OYAMBA</b>	<p>Kambiranani zifukwa zimene nthawi zonse ku sukulu kumakhala mayeso, mayeso amene aphanzitsi amafuna kudziwa zomwe ophunzira akukumbukira pa zimene aphanzira.  Yesu ankayesa chikhulupiro ndi kumvera kwavo pa nkhan imeneyi.</p>	<p>Fotokozani kuti moyo wathu uli ngati ulendo, umene umayamba tsiku lobadwa mpaka tsiku limene tidzamwalire. Pali nthawi za bata, pamene moyo umakoma komanso tili ndi nthawi imene moyo umawawa.  Funsani ophunzira aganize za nthawi imene “zinthu zinali bwino” ndiponso nthawi imene “moyo unkawawa”.</p>
<b>KUTSIRIZA</b>	<p><b>Perekani Nkhani ya m’Baibulo</b></p> <p><b>Kambiranani ndi Kufotokoza:</b></p> <ol style="list-style-type: none"> <li>1. Yesu ankayankhula ndi gulu la anthu ali m’bwato la Petulo.</li> <li>2. Pamene anamaliza kuyankhula, anawauza kuti apitenso akaphe nsomba. (Iwo n’kuti atayesera kupha nsomba usiku wonse, ndipo anali atatopa komanso ndi njala, koma sanagwire nsomba.)</li> <li>3. Petulo anachita zomwe Yesu analamula ndipo anapha nsomba zambiri.</li> <li>4. Petulo anazindikira ukulu wa Yesu, ndi kuchepa kwake pamaso pake! <b>(5:8)</b></li> <li>5. Ophunzira anasiya chilichonse ndi kuyamba kutsatira Yesu.</li> </ol> <p><b>Fotokozani Vesi Yoloweza ndipo limbikitsani ophunzira kuti aloweze.</b>  <b>Tsirizani Phunziro Lachiwiri.</b></p> <p><b>Kuonetsa:</b> Onani FBI pa Zoonjezera A – Kugwira nsomba zambiri.</p>	<p><b>Perekani Nkhani ya m’Baibulo</b></p> <p><b>Kambiranani ndi Kufotokoza:</b></p> <ol style="list-style-type: none"> <li>1. Yesu anachita chodabwitsa chachikulu chimodzi ndipo kenaka anauza ophunzira ake kuti awoloke Nyanja ya Galileya.</li> <li>2. Iye anapita ku phiri kukapemphera.</li> <li>3. Ophunzira anakumana ndi namondwe pa nyanja.</li> <li>4. Yesu anadziwa zimenezi ndipo anabwera akuyenda pa madzi.</li> <li>5. Petulo anapempha kuti apite kumene kunali Yesu ndipo anapita akuyenda pa madzi.</li> <li>6. Iye anayamba kumira, anafulua kwa Yesu ndipo Yesu anamupulumsa.</li> <li>7. <i>Fotokozani kufunika kokhala ndi chikhulupiro mwa Yesu.</i></li> <li>8. <i>Fotokozani momwe iye angatithandizire pamene takumana ndi namondwe wa moyo wathu.</i></li> </ol> <p><b>Fotokozani Vesi Yoloweza ndipo limbikitsani ophunzira kuti aloweze.</b>  <b>Tsirizani Phunziro Lachiwiri.</b></p> <p><b>Kuonetsa:</b> Onani FBI pa Zoonjezera A – Mavuto ake.</p>
<b>KUKUMBUTSANA</b>	<p><b>Mafunso kwa ophunzira:</b></p> <ol style="list-style-type: none"> <li>1. Kodi yankho la Simoni Petulo pa <b>vesi 5</b> likutanthauza chiyani?</li> <li>2. Kodi tikuphunzira chiyani kuchokera kwa Petulo pamene akuvomoreza tchimo lake?</li> <li>3. Kambiranani tanthauzo la kutembenuka mtima.</li> <li>4. Kodi ife “tingasiye zonse” motani ndi kutsatira Yesu?</li> </ol>	<p><b>Mafunso kwa ophunzira:</b></p> <ol style="list-style-type: none"> <li>1. Kodi mawu a Yesu amene ali pa <b>vesi 27</b> akutilimbikitsa motani?</li> <li>2. Kodi tikuphunzira chiyani za chikhulupiro ndi kulephera kwa Petulo?</li> <li>3. Kodi tikuphunzira chiyani za pamene tikukumana ndi mavuto m’moyo wathu?</li> </ol>
<b>KHALANI MOYO UMENEWU</b>	<p><b>Zomwe tikuphunzira m’phunziroli:</b></p> <ol style="list-style-type: none"> <li>1. Tchulani njira zitatu zomwe mungatsatire kuti mumvere Yesu sabata lamawa.</li> <li>2. Funsani Mkristu amene mukumudziwa kuti akuuzeni nthawi imene anazindikira kuti Mulungu wamukhululukira.</li> <li>3. Monga Akhristu tikuyenera kulangizidwa ndi Yesu - Petulo anali katswiri pa usodzi koma analandira uphungu kuchokera kwa Yesu. (Mpalamatabwa!)</li> </ol>	<p><b>Zomwe tikuphunzira m’phunziroli:</b></p> <ol style="list-style-type: none"> <li>1. Kambiranani ngati gulu za “namondwe” amene munakumana naye pa moyo wanu ndipo muganizire momwe Yesu anakuthandizirani pamene munamadalira.</li> <li>2. Werengani <b>Yesaya 43:2</b>. Taganizani za omwe akutsatira Yesu ndiponso momwe vesi iyi ikugwirizana ndi Ndime Yowerenga ya lero?</li> </ol>

	<p><b>A3 – KALASI Lachitatu</b>  <b>Phunziro Lachitatu – Moyo wa Petulo</b>  <b>Mutu – Yesu apulumutsa Petulo</b></p>	<p><b>A3 – KALASI Yachinayi</b>  <b>Phunziro Lachitatu – Petulo</b>  <b>Mutu – Kuvomereza kwake</b></p>
	<p><b>Ndime Yowerenga:</b> <i>Mateyu 14:22-33</i>  <b>Vesi Yoloweza:</b> <i>Mateyu 14:33</i></p> <p><b>Ife tikuphunzira kuti:</b></p> <ol style="list-style-type: none"> <li>1. Yesu ndi Mwana wa Mulungu.</li> <li>2. Kudalira Yesu kumatithandiza kugonjetsa namondwe wa moyo wathu ndi mantha athu.</li> </ol>	<p><b>Ndime Yowerenga:</b> <i>Mateyu 16:13-28</i>  <b>Vesi Yoloweza:</b> <i>Aroma 10:9</i></p> <p><b>Ife tikuphunzira kuti:</b></p> <ol style="list-style-type: none"> <li>1. Yesu ndi "Khristu" kapena "Mesiya."</li> <li>2. Yankho la Ambuye kwa Petulo likufotokoza maziko a mpingo.</li> </ol>
<b>MAWU OYAMBA</b>	<p>Yankhula za anamondwe a moyo. Fotokozani kuti moyo uli ngati ulendo umene umayamba tsiku limene tabadwa ndipo udzatha tsiku limene tidzamwalira. Fotokozani kuti pa ulendo umenewu pali anamondwe ochuluka, ena aakulu kuposa ena. Funsani ophunzira kuti aganizire za "nthawi zabwino" ndi "nthawi zowawa" m'miyoyo yawo.</p>	<ol style="list-style-type: none"> <li>1. Yankhulanu kuti vuto limodzi mwa mafunso aakulu lero ndi funso lakuti kodi Yesu ndi yani.</li> <li>2. Fotokozani kuti m'nthawi ya Yesu anthu ankapereka mayankho osianasiyana pofuna kunena za chomwe Yesu anali, ndipo Yesu anafunsa ophunzira ake za chomwe lye anali.</li> <li>3. Funsani ophunzira kuti afotokoze zimene iwo akuganiza za chomwe Yesu ali.</li> </ol>
<b>KUTSIRIZA</b>	<p><b>Perekani Nkhani ya m'Baibulo</b></p> <p><b>Kambiranani ndi Kufotokoza:</b></p> <ol style="list-style-type: none"> <li>1. Yesu anachita chodabwitsa chachikulu ndipo kenaka anauza ophunzira ake awoloke Nyanja ya Galileya.</li> <li>2. Iye anapita ku phiri kukapemphera.</li> <li>3. Ophunzira ake anali m'kati mwa namondwe.</li> <li>4. Yesu anadziwa zimenezi ndipo anabwera kudzawathandiza akuyenda pa madzi.</li> <li>5. Petulo anapempha kuti apite komwe kunali Yesu, ndipo anapita akuyendanso pa madzi.</li> <li>6. Iye anayamba kumira, anafuula kwa Yesu ndipo Yesu anamupulumsa.</li> <li>7. <i>Fotokozani kufunika kokhala ndi chikhulupiriro mwa Yesu.</i></li> <li>8. <i>Fotokozani momwe kukhulupirira Yesu kungatithandizire pamene tikudutsa mu namondwe wa moyo wathu.</i></li> <li>9. <i>Ganizirani kufunika kwa kudalira Yesu m'nthawi yathu yovuta.</i></li> </ol> <p><b>Fotokozani Vesi Yoloweza ndipo limbikitsani ophunzira kuti aloweze.</b>  <b>Tsirizani Phunziro Lachitatu.</b></p> <p><b>Kuonetsa:</b> Onani FBI pa Zoonjezera A – Yesu apulumutsa Petulo.</p>	<p><b>Perekani Nkhani ya m'Baibulo</b></p> <p><b>Kambiranani ndi Kufotokoza:</b></p> <ol style="list-style-type: none"> <li>1. Yesu ali kumsonga ya kumpoto kwa dzikoli kumene anapita. (Onani pa mapu m'phunzirolu.)</li> <li>2. Iye akufunsa, "Kodi anthu amati ndine yani?" - Onani mayankho anayi.</li> <li>3. Kenaka lye akufunsa, "Inu mumati ndine yani?" Onani yankho la Petulo nthawi yomwego.</li> <li>4. Iye akufotokoza kuti amene amakhulupirira kuti lye ndi Mwana wa Mulungu Wamoyo ndiwo mpingo. Mpingo si nyumba koma gulu la anthu okhulupirira.</li> <li>5. Kenaka Yesu akufotokoza kuti akafa adzaukanso</li> <li>6. Petulo akuti zimenezi sizingatheke.</li> <li>7. <i>Taganizani chifukwa chimene Petulo anadzudzulira Yesu ndi yankho la Ambuye kwa Petulo.</i></li> </ol> <p><b>Fotokozani Vesi Yoloweza ndipo limbikitsani ophunzira kuti aloweze.</b>  <b>Tsirizani Phunziro Lachitatu.</b></p> <p><b>Kuonetsa:</b> Onani FBI pa Zoonjezera A – Kuvomereza kwake.</p>
<b>KUKUMBUTSANA</b>	<p><b>Mafunso kwa ophunzira:</b></p> <ol style="list-style-type: none"> <li>1. Kodi Yesu angatithandize motani kuthetsa mantha athu?</li> <li>2. Tchulani zovuta zina zimene achinyamata amakumana nazo.</li> <li>3. Kodi ndime iyi ikuthandiza motani?</li> <li>4. Pangani mtanda ndipo uyimikeni. Lembanu pa mapepala mavuto anu ndipo muwamate pa mtandapo. Jambulani utawaleza ndipo lembanipo malonjezo ena a Mulungu pamenepo.</li> </ol>	<p><b>Mafunso kwa ophunzira:</b></p> <ol style="list-style-type: none"> <li>1. Kodi tingatsimikize bwanji kuti ndife ake a Yesu?</li> <li>2. Kodi timakhala gawo la mpingo motani?</li> <li>3. Kodi zinthu zabwino zokhalira gawo la mpingo ndi ziti?</li> </ol>
<b>KHALANI MOYO UMENEWU</b>	<p><b>Zomwe tikuphunzira m'phunzirolu:</b>  Petulo anadalira Yesu.</p> <ol style="list-style-type: none"> <li>1. Ife tikuyenera kuyika maso athu pa Yesu tikapanda kutero tidzamira!</li> <li>2. Ife tisatanganidwe ndi zochita zathu kapena zomwe zikutichitikira ndi kuyiwala kudalira Yesu.</li> </ol>	<p><b>Zomwe tikuphunzira m'phunzirolu:</b></p> <ol style="list-style-type: none"> <li>1. Aliyense alembe pemphero loyamika Mulungu chifukwa cha mpingo.</li> <li>2. Ganizirani za munthu mmodzi amene mukagawane naye nkhanu yabwino ya Yesu.</li> </ol>

	<p><b>A3 – KALASI Lachitatu</b>  <b>Phunziro Lachinayi – Moyo wa Petulo</b>  <b>Mutu – Kodi Yesu ndi yani?</b></p>	<p><b>A3 – KALASI Yachinayi</b>  <b>Phunziro Lachinayi – Petulo</b>  <b>Mutu – Pa phiri</b></p>
	<p><b>Ndime Yowerenga:</b> <i>Mateyu 16:13-23</i>  <b>Vesi Yoloweza:</b> <i>Aroma 10:9</i></p> <p><b>Ife tikuphunzira kuti:</b></p> <ol style="list-style-type: none"> <li>1. Ife tikuyenera kuchitira umboni za Yesu amene ndi Mwana wa Mulungu.</li> <li>2. Yesu ndi Mutu wa Mpingo.</li> <li>3. Yesu ndi Khristu Mwana wa Mulungu Wamoyo.</li> </ol>	<p><b>Ndime Yowerenga:</b> <i>Mateyu 17:1-13</i>  <b>Vesi Yoloweza:</b> <i>2 Petulo 1:16-18</i></p> <p><b>Ife tikuphunzira kuti:</b></p> <ol style="list-style-type: none"> <li>1. Yesu ndi Mwana wapadera wa Mulungu.</li> <li>2. Yesu ndi wamkululu kuposa Mose kapena Eliya.</li> <li>3. Ndi Yesu amene angagwire ntchito ya Mulungu ya Chipulumutso.</li> </ol>
<b>MAWU OYAMBA</b>	<p>Yankhulani za anthu otchuka kwambiri ndipo muganizire chifukwa chomwe iwo amatchedwa otchuka. Yesu anatchuka koma anthu ambiri sankadziwa kuti anali yani.</p>	<p>Yankhulani za nthawi yopambana imene ophunzira sadziyiwala.  Fotozani kuti ophunzira atatu sanakanayiwala zimene anaona Yesu ali mu ulemerero wake pa phiri paja.</p>
<b>KUTSIRIZA</b>	<p><b>Perekani Nkhani ya m’Baibulo</b></p> <p><b>Kambiranani ndi Kufotokoza:</b></p> <ol style="list-style-type: none"> <li>1. Yesu akufunsa, “Kodi anthu amati ndine yani”? - <i>Onani mayankho anayi.</i></li> <li>2. Kenaka lye akufunsa, “Kodi inu mumati ndine yani”? - <i>Onani yankho la Petulo nthawi yomweyo. Fotokozani kufunika kwa kuvomereza kwa Petulo ndi zomwe zikutanthauza kwa okhulupirira.</i></li> <li>3. Kenaka lye akufotokoza kuti amene amakhulupirira kuti lye ndi Mwana wa Mulungu Wamoyo amapanga mpingo. <i>Mpingo si nyumba koma gulu la anthu okhulupirira!</i></li> <li>4. Yesu akufotokoza kuti akupita kukafa ndipo kenaka adzaukanso.</li> <li>5. Petulo akuti zimenezi sizingatheke. Ganizirani yankho la Yesu kwa Petulo.</li> </ol> <p><b>Fotokozani Vesi Yoloweza ndipo limbikitsani ophunzira kuti aloweze.</b>  <b>Tsirizani Phunziro Lachinayi.</b></p> <p><b>Kuonetsa:</b> Onani FBI pa Zoonjezera A – Kodi Yesu ndi yani?</p>	<p><b>Perekani Nkhani ya m’Baibulo</b></p> <p><b>Kambiranani ndi Kufotokoza:</b></p> <ol style="list-style-type: none"> <li>1. Yesu wasankha ophunzira atatu kuti apite naye ku phiri.</li> <li>2. Iye akuoneka mu ulemerero waufumu wonse pamodzi ndi Mose ndi Eliya.</li> <li>3. Petulo akufuna akhale pa phiripo ndi kuwamangira misasa itatu.</li> <li>4. Mulungu akuyankhula kumwamba kuwakumbutsa kuti Yesu ndi woposa munthu wina aliyense.</li> <li>5. Ophunzira akuchita mantha koma Yesu akuwatonthoza ndi kuwafotokozeru zomwe zangochitika kumenezo.</li> <li>6. <i>Fotokozani kuposa kwa Yesu komanso ndi ubwino wake.</i></li> <li>7. <i>Ganizani za kufunika kwa Yesu kuhala woyamba m’miyoyo yathu.</i></li> </ol> <p><b>Fotokozani Vesi Yoloweza ndipo limbikitsani ophunzira kuti aloweze.</b>  <b>Tsirizani Phunziro Lachinayi.</b></p> <p><b>Kuonetsa:</b> Onani FBI pa Zoonjezera A – Pa Phiri.</p>
<b>KUKUMBUTSANA</b>	<p>Ikani pa khoma pepala lomwe mujambule tchalichi ndipo m’kati mwake mulembe phindu lokhala gawo la mpingo.</p> <p>Pezani munthu amene mukufuna kumuchitira umboni ndipo muzimupempherera nthawi ndi nthawi.</p>	<p><b>Mafunso kwa ophunzira:</b></p> <ol style="list-style-type: none"> <li>1. N’chifukwa chiyani kunali kofunika kuti Petulo aonerere za kusandulika kwa Yesu?</li> <li>2. Kodi mukuganiza kuti ophunzira anaphunzira chiyani pamenepe?</li> </ol>
<b>KHALANI MOYO UMENEWU</b>	<p><b>Mafunso kwa ophunzira:</b></p> <ol style="list-style-type: none"> <li>1. N’chifukwa chiyani mawu a Petulo (<b>vesi 22</b>) anali olakwika?</li> <li>2. Kodi mpingo wathu ungaithandize motani kutumikira bwino Mulungu?</li> <li>3. Kodi tingachitire umboni motani, kufotokozena ena chimene Yesu ali?</li> </ol>	<p><b>Mafunso kwa ophunzira:</b></p> <ol style="list-style-type: none"> <li>1. Kodi tingamupatse motani malo oyamba m’miyoyo yathu?</li> <li>2. Lembani zinthu zochitika zomwe zimatilepheretsa kuti Yesu asakhale woyamba.</li> <li>3. <b>Vesi 5</b> akuti, “Mverani lye.” Kodi ife tingamve bwanji zomwe Mulungu akuyankhula nafe?</li> <li>4. Khalani ndi nthawi sabata ino kuti mumve zimene Mulungu akuyankhula kwa inu.</li> </ol>

	<p><b>A4 – KALASI Lachitatu</b>  <b>Phunziro Loyamba – Moyo wa Petulo</b>  <b>Mutu – Chitsanzo cha chikondi</b></p>	<p><b>A4 – KALASI Yachinayi</b>  <b>Phunziro Loyamba – Petulo</b>  <b>Mutu – Maphunziro a kudzichepetsa</b></p>
	<p><b>Ndime Yowerenga:</b> <i>Yohane 13:1-17</i>  <b>Vesi Yoloweza:</b> <i>Yohane 13:15</i></p> <p><b>Ife tikuphunzira kuti:</b></p> <ol style="list-style-type: none"> <li>Yesu anali mtumiki woona.</li> <li>Ifenso tikuyenera kumatumikira ena.</li> </ol>	<p><b>Ndime Yowerenga:</b> <i>Yohane 13:1-17</i>  <b>Vesi Yoloweza:</b> <i>Yohane 13:15</i></p> <p><b>Ife tikuphunzira kuti:</b></p> <ol style="list-style-type: none"> <li>Yesu anali Mtumiki wodzichepetsa, womvera chifuniro cha Mulungu.</li> <li>Kudzichepetsa ndi kofunika kwambiri mu utumiki wa Chikhristu.</li> </ol>
<b>MAWU OYAMBA</b>	<p>Kumene Yesu ankakhala kunali kotentha ndi kowuma. (Fananitsani ndi kumene akukhala ophunzira anu lero.) Anthu ankayenda m'misewu ya fumbi ndipo ankati akafika pa nyumba ya munthu, mwini nyumbayo ankasambitsa mapazi a alendo ake asanayambe kudya. (Taganizirani kwanuko za chikhaldwe chomwe chimachitika pamene munthu akulowa m'nyumba.)</p>	<p>Ambuye Yesu nthawi zambiri ankafotokoza za choonadi cha moyo wa Chikhristu kudzera m'mafanizo. Koma nthawi iyi anafuna kuphunzitsa pochita chinthu china ndipo fanizo limeneli timalitcha "Fanizo la Zochita."</p> <p>Fotokozani kuti nthawi imeneyi chifukwa cha misewu ya fumbi, chinali chikhaldwe chawo kusambitsa mapazi a alendo akangofika pa nyumba ya munthu.</p>
<b>KUTSIRIZA</b>	<p><b>Perekani Nkhani ya m'Baibulo</b></p> <p><b>Kambiranani ndi Kufotokoza:</b></p> <ol style="list-style-type: none"> <li>Ili linali tsiku loti Yesu apachikidwa mawa, ndipo ankadya chakudya chotsiriza ndi ophunzira ake.</li> <li>Palibe amene anachita mwambo wa nthawi zonse wosambitsa mapazi awo. Yesu anakonzekera kuwasambitsa mapazi awo (<b>vesi 4-5</b>).</li> <li>Petulo sankafuna kuti Yesu asambitse mapazi ake.</li> <li>Yesu anaftokoza kuti ankayenera kutero ndipo ngati sakanatero, Petulo sakanakhala mmodzi wa lye (vesi 8).</li> <li>Yesu anagwiritsa ntchito kusambitsa mapazi awo pofuna kuonetsa kuti tonse ndife odetsedwa ndi machimo ndipo tikuyenera kusambitsidwa kapena kuyeretsedwa ku machimo athu, ndipo ndi lye yekha amene angachite chifukwa anatifera pa mtanda.</li> <li>Yesu ankaonetsano kuti ife tikuyenera kugwira ntchito iliyonse chifukwa cha anthu ena.</li> <li><i>Fotokozani tanthauzo la kusambitsana mapazi.</i></li> </ol> <p><b>Fotokozani Vesi Yoloweza ndipo limbikitsani ophunzira kuti aloweze.</b>  <b>Tsirizani Phunziro Loyamba.</b></p> <p><b>Kuonetsa:</b> Onani FBI pa Zoonjezera B – Chitsanzo cha chikondi.</p>	<p><b>Perekani Nkhani ya m'Baibulo</b></p> <p><b>Kambiranani ndi Kufotokoza:</b></p> <ol style="list-style-type: none"> <li>Yesu anali pa phwando la Paska pamodzi ndi ophunzira ake ndipo ankakumbukira zonse zimene zinachitika pamene Airraeli ankatuluka m'dziklo la Igupto.</li> <li>Inali nthawi ya chakudya chimenechi pamene lye anachita zinthu ziwiri zofunka kwambiri.</li> <li>Choyamba, lye anakhala ngati wantchito ndi kusambitsa mapazi awo, kuonetsa kuti anali wokonze kaugwira ntchito wamba ndi kuwapatsa chitsanzo. (Onani Vesi Yoloweza.)</li> <li>lye ankaonetsa kuti tonse tikuyenera kuyeretsedwa machimo athu (akupereka chitsanzo cha kusamba thupi lonse - <b>vesi 10</b>), komabe tikufunika kumasamba mapazi athu tsiku ndi tsiku pamene takhala Akhristu pakuti tsiku lililonse timachimwa ndipo timafuna kuti azitikhululukira.</li> <li>Onani zomwe Ambuye anamuua Petulo kuti muthandize ophunzira kumvetsetsa.</li> <li>Chachiwiri, lye anatenga buledi ndi vinyo ndi kufotokoza kuti buledi akuyimira thupi lake limene lidzapachikidwa ndipo vinyo akuyimira magazi ake amene adzakhetsedwa pa mtanda. (<b>Onani Luka 22:19 ndi 20</b>)</li> </ol> <p><b>Fotokozani Vesi Yoloweza ndipo limbikitsani ophunzira kuti aloweze.</b>  <b>Tsirizani Phunziro Loyamba.</b></p> <p><b>Kuonetsa:</b> Onani FBI pa Zoonjezera B – Mapunziro a kudzichepetsa.</p>
<b>KUKUMBUTSANA</b>	<ol style="list-style-type: none"> <li>Fotokozani njira zina zomwe Akhristu angatsatire potumikirana wina ndi mnzake sabata la mawa.</li> <li>Ganizirani momwe mungatumikirire anthu amene ali kunja kwa mpingo wanu chaka chamawa.</li> </ol>	<ol style="list-style-type: none"> <li>Kodi Petulo anaphunzira chiyani kuchokera pa nkhanu imeneyi?</li> <li>Kodi kuyeretsedwa ku machimo athu kumatanthauza chiyani, ndipo ife tikuyenera kumachita chiyani tsiku ndi tsiku kuti tizikhala chifupi ndi Ambuye ndi kutsatira chifuniro chake m'moyo wathu?</li> </ol>
<b>KHALANI MOYO UMENEWE</b>	<p><b>Zomwe tikuphunzira m'phunziroli:</b></p> <ol style="list-style-type: none"> <li>Kodi Yesu ali pa dziko lapansi anatumikira anthu ena motani?</li> <li>Yesu ankaphunzitsano kuti ngakhale tili Akhristu, nthawi zina timachimwa ndipo tsiku lililonse tikuyenera kupempha kuti azitiyeretsa ndi kutikhululukira.</li> </ol>	<p><b>Zomwe tikuphunzira m'phunziroli:</b></p> <ol style="list-style-type: none"> <li>Kambiranani njira zomwe tingeonetsere kudzichepetsa lero.</li> <li>Ganizirani zomwe tingachite kuti Mulungu akhale woyamba m'miyoyo yathu.</li> <li>Fufuzani za moyo wa Mkhristu amene amadziwika kuti anatumikira modzichepetsa.</li> </ol>

	<p><b>A4 – KALASI Lachitatu</b>  <b>Phunziro Lachiwiri – Moyo wa Petulo</b>  <b>Mutu – Iye anakana Mbuye wake</b></p>	<p><b>A4 – KALASI Yachinayi</b>  <b>Phunziro Lachiwiri – Petulo</b>  <b>Mutu – Phunziro la kudzipereka</b></p>
	<p><b>Ndime Yowerenga:</b> <i>Luka 22:31-34, 54-62</i>  <b>Vesi Yoloweza:</b> <i>Luka 22:31-32</i></p> <p><b>Ife tikuphunzira kuti:</b></p> <ol style="list-style-type: none"> <li>1. N'zovuta kunena kuti ndife ake a Yesu.</li> <li>2. Tikuyenera kunena zonna nthawi zonse.</li> </ol>	<p><b>Ndime Yowerenga:</b> <i>Luka 22:31-34, 39-62</i>  <b>Vesi Yoloweza:</b> <i>Luka 22:31-32</i></p> <p><b>Ife tikuphunzira kuti:</b></p> <ol style="list-style-type: none"> <li>1. Petulo anakhumudwitsa Yesu.</li> <li>2. Ife tikuyenera kupewa kudzidalira, koma tikuyenera kudalira Yesu.</li> <li>3. Tikuyenera kumva chisoni ndi tchimo lathu monga anachitira Petulo.</li> </ol>
<b>MAWU OYAMBA</b>	<ul style="list-style-type: none"> <li>• Ganizani za nthawi yomwe ophunzira angayesedwe kuti aname kapena kuyankhula zabodza.</li> <li>• Tafufuzani chomwe timaopa nthawi zina kunena zonna.</li> <li>• Fotokozani kuti Petulo anafika nthawi yotero.</li> <li>• Kambiranani za kusavuta kokhala munthu wa mantha m'malo mokhala munthu wolimba mtima.</li> </ul>	<ul style="list-style-type: none"> <li>• Lembanji khalidwe lomwe likuyenera kukhala mwa abwenzi abwino.</li> <li>• Yambani kuyankhula nkhaniyi ndi kufotokoza kuti Petulo anadzitamandira kuti iye sangakhumudwitse Yesu, ndi kuti anali wokonze ka kupita ku ndende chifukwa cha lye. (<i>Luka 22:33</i>) Ife tikudziwa kuti kunyada kumabweretsa chionongeko. (<i>Miyambo 16:18</i>)</li> <li>• Kwa Petulo, kunyada kwake kunamugwetsa.</li> </ul>
<b>KUTSIRIZA</b>	<p><b>Perekani Nkhani ya m'Baibulo</b></p> <p><b>Kambiranani ndi Kufotokoza:</b></p> <ol style="list-style-type: none"> <li>1. Petulo anatsatira anthu amene anagwira Yesu mpaka ku nyumba ya Mkulu wa Ansembe.</li> <li>2. Iye anakhala pamodzi ndi anthu ena pa bwalo la nyumbayo.</li> <li>3. Ena anamufunsa ngati iye anali bwensi ndi wotsatira wa Yesu ndipo katatu konse iye anakana kuti sakumudziwa Yesu ndipo anawanamiza.</li> <li>4. Tambala analira ndipo Yesu anatembenuka ndi kuyang'ana Petulo. Kenaka Petulo anazindikira zomwe wachita. Iye anakumbukira zomwe Yesu anayankhula maora ochepta apitawo. (<i>Luka 22:34</i>) Iye anapita kunja kwa nyumbayo ndipo analira kwambiri. Iye wamukhumudwitsa Yesu nthawi imene anamufuna, ndipo iye anasanduka munthu wa mantha m'malo mokhala munthu wolimba mtima.</li> </ol> <p><b>Fotokozani Vesi Yoloweza ndipo limbikitsani ophunzira kuti aloweze.</b>  <b>Tsirizani Phunziro Lachiwiri.</b></p> <p><b>Kuonetsa:</b> Onani FBI pa Zoonjezera B – Iye anakana Mbuye wake.</p>	<p><b>Perekani Nkhani ya m'Baibulo</b></p> <p><b>Kambiranani ndi Kufotokoza:</b></p> <ol style="list-style-type: none"> <li>1. Mwina Petulo anazunguzika kwambiri. Iye ankadziwa kuti Yesu anayankhula za kumukana (<i>22:34</i>). Iye ankaganiza kuti anali ndi mphamvu zotetezera Yesu.</li> <li>2. Pamene nthawi inafika, iye anachita mantha kwambiri kuti ayankhule zonna. Kunena zonna, iye anamukana Yesu monga momwe Yesu ananera.</li> <li>3. Taganizani momwe Petulo anamvera mu mtima mwake atazindikira kuti wakhumudwitsa Yesu. Iye anataluka kunja mofulumira ndipo analira kwambiri. N'chifukwa chiyani anali wokhumudwa?</li> <li>4. Kambiranani momwe mayesero a Petulo analili.</li> <li>5. Kambiranainso za kufunika kwa kumene timapita, anthu amene timacheza nawo ndi momwe timaganizira.</li> </ol> <p><b>Fotokozani Vesi Yoloweza ndipo limbikitsani ophunzira kuti aloweze.</b>  <b>Tsirizani Phunziro Lachiwiri.</b></p> <p><b>Kuonetsa:</b> Onani FBI pa Zoonjezera B – Phunziro la kudzipereka.</p>
<b>KUKUMBUTSANA</b>	<ol style="list-style-type: none"> <li>1. Lembanji zifukwa zomwe zimatilepheretsa kukhala wa Yesu ndipo lembani lonjezo lochokera m'Baibulo.</li> <li>2. Petulo anakhumudwitsa Yesu; kodi iye akanakhlulukidwa?</li> <li>3. Pezani momwe Davide anavomerezera tchimo lake ndi Batiseba (<i>2 Samuele 11</i>) pa <i>Salimo 51</i> ndipo anakhlulukidwa.</li> </ol>	<ol style="list-style-type: none"> <li>1. Ganizirani chomwe Yesu ankatanthauza pamene anachenjeza Petulo za zimene zidzachitika. (<i>Luka 22:32</i>)</li> <li>2. Tchulanji njira imodzi yomwe inu mungaonetsera kukhulupirika kwanu kwa Yesu sabata ino.</li> </ol>
<b>KHALANI MOYO UMENEWU</b>	<p><b>Zomwe tikuphunzira m'phunziroli:</b></p> <ol style="list-style-type: none"> <li>1. Kodi ndi chifukwa chiyani nthawi zina zimakhala zovuta kwa Akhristu kunena kuti ndi a Yesu?</li> <li>2. Kodi ndi chiyani chimatilepheretsa kuyankhula choona?</li> </ol>	<p><b>Zomwe tikuphunzira m'phunziroli:</b></p> <ol style="list-style-type: none"> <li>1. Kodi tingachite chiyani pofuna kuonetsa kuti tikumva chisoni chifukwa cha tchimo lathu?</li> <li>2. Kodi timesankha motani abwenzi amene tikufuna kuti tizicheza nawo nthawi zonse?</li> </ol>

	<p><b>A4 – KALASI Lachitatu</b>  <b>Phunziro Lachitatu – Moyo wa Petulo</b>  <b>Mutu – Imfa ya Ambuye Yesu</b></p>	<p><b>A4 – KALASI Yachinayi</b>  <b>Phunziro Lachitatu – Petulo</b>  <b>Mutu – Nthawi yachisoni ndi yachimwemwe</b></p>
	<p><b>Ndime Yowerenga:</b> <i>Marko 15:22-40</i>  <b>Vesi Yoloweza:</b> <i>Agalatiya 2:20</i></p> <p><b>Ife tikuphunzira kuti:</b></p> <ol style="list-style-type: none"> <li>1. Yesu analibe tchimo ndipo anali wangwiyo.</li> <li>2. Ife tikuyenera kuyamika chifukwa cha imfa ya Yesu pa mtanda.</li> </ol>	<p><b>Ndime Yowerenga:</b> <i>Luka 24:1-12, 33-49</i>  <b>Vesi Yoloweza:</b> <i>Luka 24:46-47</i></p> <p><b>Ife tikuphunzira kuti:</b></p> <ol style="list-style-type: none"> <li>1. Yesu analangidwa chifukwa cha machimo athu kuti ife tipulumutsidwe.</li> <li>2. Yesu amakhululukira ndi kupereka moyo wosatha.</li> </ol>
<b>MAWU OYAMBA</b>	<ul style="list-style-type: none"> <li>• Kambiranani zomwe ophunzira akanachita ngati wina akanawakhumudwitsa monga anachitira Petulo.</li> <li>• Taganizani zomwe Petulo ankafuna kuchita ndi mmene zinalili zovuta kutero.</li> </ul>	<p>Fotokozani kuti sitikudziwa zomwe Petulo ankachita pamene Yesu anali pa mtanda, koma tikudziwa kuti pa tsiku loyamba la Sabata la Paska, m'mawa, iye anapita ku manda, ndipo Baibulo limati anakumana ndi Yesu tsiku limenelo. (<b>Onani vesi 34.</b>)</p>
<b>KUTSIRIZA</b>	<p><b>Perekani Nkhani ya m'Baibulo</b></p> <p><b>Kambiranani ndi Kufotokoza:</b></p> <ol style="list-style-type: none"> <li>1. Fotokozani momwe Yesu anamutengera kupita kunja kwa mzinda kukapachikidwa.</li> <li>2. Fotokozani zomwe anamuchita ndi momwe omwe anali pafupi anamunyozeria ndi kumuseka.</li> <li>3. Fotokozani kuti mdima wa maora atatu umene unabwera chinali chodabwitsa ndipo zikunthandiza kumvetsetsa kuti Mulungu sanayang'ane Mwana wake amene ankalangidwa chifukwa cha machimo athu.</li> <li>4. Nthawi imeneyi Yesu analandira chilango cha machimo m'malo mwathu.</li> <li>5. Fotokozani zomwe zinachitika Yesu atafa. (<b>15:38-39</b>)</li> <li>6. Fotokozani zomwe anayankhula Kenturiyo amene anayima pafupi ndi mtanda.</li> </ol> <p><b>Fotokozani Vesi Yoloweza ndipo limbikitsani ophunzira kuti aloweze.</b>  <b>Tsirizani Phunziro Lachitatu.</b></p> <p><b>Kuonetsa:</b> Onani FBI pa Zoonjezera B – Imfa ya Ambuye Yesu.</p>	<p><b>Perekani Nkhani ya m'Baibulo</b></p> <p><b>Kambiranani ndi Kufotokoza:</b></p> <ol style="list-style-type: none"> <li>1. Fotokozani momwe mayi uja anapitira ku manda m'mawa tsiku loyamba la Sabata la Paska.</li> <li>2. Fotokozani zomwe anakapeza ndi uthenga umene anauzidwa.</li> <li>3. Pamene Petulo anamva nkhani imeneyi, fotokozani zomwe iye anachita. (<b>vesi 12</b>)</li> <li>4. Fotokozani chifukwa chomwe ena zinkawavuta kukhulupirira kuti Yesu ali moyo.</li> <li>5. Fotokozani zomwe zinachitika pamene Ambuye Yesu anaonekeraka pakati pawo.</li> <li>6. Petulo ndi anzake anali ndi chimwemwe chachikulu pamene anaona kuti Ambuye Yesu auka.</li> <li>7. Kodi Yesu anafotokoza chiyani za masautso ake? (<b>24:45-47</b>)</li> </ol> <p><b>Fotokozani Vesi Yoloweza ndipo limbikitsani ophunzira kuti aloweze.</b>  <b>Tsirizani Phunziro Lachitatu.</b></p> <p><b>Kuonetsa:</b> Onani FBI pa Zoonjezera B – Nthawi yachisoni ndi yachimwemwe.</p>
<b>KUKUMBUTSANA</b>	<ol style="list-style-type: none"> <li>1. Ganizirani za kupambana kwa imfa ya Yesu pa mtanda, tanthauzo la Vesi Yoloweza, komanso za kuti Yesu anafera munthu aliyense.</li> <li>2. Kambiranani za madalitso a imfa ya Yesu pa mtanda. Pezani malo amene mungakoleke mtanda monga chikumbusso cha nsembe imene Yesu anapereka.</li> <li>3. Pangani kadi ya chiyamiko ndipo m'kati mwake mulembe pemphero loyamika Mulungu.</li> </ol>	<ol style="list-style-type: none"> <li>1. Kambiranani za njira zomwe tingaonetsera kuti ife tikuvomereza machimo athu.</li> <li>2. Pekani nyimbo yosangalalira kuti Yesu anagonjetsa imfa komanso anauka kwa akufa.</li> </ol>
<b>KHALANI MOYO UMENEWU</b>	<p><b>Zomwe tikuphunzira m'phunziroli:</b></p> <ol style="list-style-type: none"> <li>1. Kodi inu mukuganiza kuti Yesu anafa pa mtanda chifukwa chiyani?</li> <li>2. Ife tikuyenera kuyamika Mulungu chifukwa cha imfa ya Yesu pa mtanda.</li> </ol>	<p><b>Zomwe tikuphunzira m'phunziroli:</b></p> <ol style="list-style-type: none"> <li>1. Kodi ife tingatsimikize bwanji kuti Yesu ndi wamoyo?</li> <li>2. Kodi kukhala ndi moyo wosatha zikutanthauza chiyani?</li> <li>3. Kodi tingadziwe bwanji kuti takhululukidwa machimo athu?</li> </ol>

	<p><b>A4 – KALASI Lachitatu</b>  <b>Phunziro Lachinayi – Moyo wa Petulo</b>  <b>Mutu – “Kodi umandikonda Ine?”</b></p>	<p><b>A4 – KALASI Yachinayi</b>  <b>Phunziro Lachinayi – Petulo</b>  <b>Mutu – Maphunziro mwa chikondi</b></p>
	<p><b>Ndime Yowerenga:</b> <i>Yohane 21:1-17</i>  <b>Vesi Yoloweza:</b> <i>Yohane 21:17</i></p> <p><b>Ife tikuphunzira kuti:</b></p> <ol style="list-style-type: none"> <li>1. Ngakhale pamene takhumudwitsa Yesu, monga anachitira Petulo, titha kukhululukidwa.</li> <li>2. Yesu akufuna kuti tiphunzitse ena ndi kuwasamalira monga mmene m'busa amasamalira nkosa zake.</li> </ol>	<p><b>Ndime Yowerenga:</b> <i>Yohane 21:1-20</i>  <b>Vesi Yoloweza:</b> <i>Yohane 21:15</i></p> <p><b>Ife tikuphunzira kuti:</b></p> <ol style="list-style-type: none"> <li>1. Petulo anapatsidwa mwayi woyamba mwatsopano.</li> <li>2. Yesu ndi wokonzeka kutipatsa mwayi woyambanso kwa ife tonse.</li> <li>3. Ngakhale timalephera, Yesu amatikondabe.</li> </ol>
<b>MAWU OYAMBA</b>	<p>Petulo akufuna kuyambanso moyo wake Yesu atafa ndi kukonza zolephera zake. Iye wabwerera ku mudzi kwawo ndi ku ntchito yake ndipo wapita kukapha nsomba ku Nyanja ya Galileya.</p>	<p>Ambuye Yesu anasonyeza kuti anali ndi moyo pamene anaonekera kwa ophunzira ake kangapo atauka kwa akufa. (<i>1 Akorinto 15:3-8</i>)  Tsopano akukumana mwapadera ndi ophunzira ake asanu ndi awiri.</p>
<b>KUTSIRIZA</b>	<p><b>Perekani Nkhani ya m'Baibulo</b></p> <p><b>Kambiranani ndi Kufotokoza:</b></p> <ol style="list-style-type: none"> <li>1. Ophunzira anayesa kupha nsomba usiku wonse koma sanagwire kanthu. Iwo akubwerera ku mtunda, atatopa, ali ndi njala ndiponso ali okhumudwa.</li> <li>2. Yesu ali m'mbali mwa nyanja akuwayitani koma sakumuzindikira. Iye akuwafunsa ngati ali ndi nsomba.</li> <li>3. Iwo akumvera zomwe walamula ndipo akuponya khoka kumbali ina ya bwato lawo ndipo akugwira nsomba zambiri.</li> <li>4. Yohane akuzindikira kuti ndi Yesu ndipo Petulo akusambira kupita pa mtunda kukakumana naye.</li> <li>5. Yesu akuwayitanira chakudya chammawa ndipo akufunsa Petulo ngati amamukonda iye.</li> <li>6. Petulo akuyankha kuti amamukonda, ndipo Yesu akumumapatsa ntchito yatsopano yoyang'anira otsatira ake (nkosa).</li> <li>7. <i>Kambiranani chifukwa chomwe Yesu akufunsa funso limodzi lomwelo katatu.</i></li> <li>8. <i>Taganizirani momwe Ambuye anakhululukira Petulo mpaka pofika kumupatsa ntchito yatsopano yofunika kwambiri.</i></li> </ol> <p><b>Fotokozani Vesi Yoloweza ndipo limbikitsani ophunzira kuti aloweze.</b>  <b>Tsirizani Phunziro Lachinayi.</b></p> <p><b>Kuonetsa:</b> Onani FBI pa Zoonjezera B – “Kodi umandikonda Ine?”</p>	<p><b>Perekani Nkhani ya m'Baibulo</b></p> <p><b>Kambiranani ndi Kufotokoza:</b></p> <ol style="list-style-type: none"> <li>1. Kuonekera kwina atauka kwa akufa kunali kwa ophunzira asanu ndi awiri amene anapita kukapha nsomba ku Nyanja ya Galileya.</li> <li>2. Iye anawatsimikizira chomwe anali powathandiza kupha nsomba zambiri.</li> <li>3. Ophunzira anadya chakudya chammawa ndi Ambuye m'mbali mwa nyanja.</li> <li>4. Ambuye Yesu ankafuna kuti atsimikize ngati Petulo analapadi chifukwa anamukhumudwitsa kumapeto a moyo wake.</li> <li>5. Katatu konse Petulo anavomereza chikondi chake pa Ambuye pamaso pa ena onse.</li> <li>6. Tsopano Petulo akhala m'busa amene azisamalira otsatira a Ambuye mu mpingo watsopano. Iye akupatsidwa mpata wachiwiri wotumikira Ambuye.</li> <li>7. <i>Kambiranani za chikondi cha Mulungu pa ife, ngakhale ife timalephera, ndipo iye akufuna kuti tizimukonda.</i></li> <li>8. <i>Kumbutsani ophunzira kuti Mulungu samatikhumudwitsa ngakhale ife timamukhumudwitsa nthawi zambiri.</i></li> </ol> <p><b>Fotokozani Vesi Yoloweza ndipo limbikitsani ophunzira kuti aloweze.</b>  <b>Tsirizani Phunziro Lachinayi.</b></p> <p><b>Kuonetsa:</b> Onani FBI pa Zoonjezera B – Maphunziro mwa chikondi.</p>
<b>KUKUMBUTSANA</b>	<p>1. Kambiranani zomwe mungachite sabata lino kuti mukhale ndi nthawi yomvetsera kwa Yesu.</p> <p>2. Fufuzani za munthu wotchuka amene anaphunzira kukhala ndi nthawi yomvetsera kwa Yesu kenaka ndi kuchita chifuniro chake.</p>	<p>Fufuzani moyo wa Mkhristu wotchuka amene Mulungu anamupatsa mpata winanso watsopano.</p>
<b>KHALANI MOYO UMENEWU</b>	<p><b>Zomwe tikuphunzira m'phunziroli:</b></p> <ol style="list-style-type: none"> <li>1. Ganizirani kufunika kwa kuonetsa chikondi chathu kwa Ambuye chifukwa cha zonse zimene watichitira.</li> <li>2. Zindikirani kuti Ambuye wokonzeka kutipatsa mpata wokwanira pamene tamukhumudwitsa ngati ife titalapa machimo athu.</li> </ol>	<p><b>Zomwe tikuphunzira m'phunziroli:</b></p> <ol style="list-style-type: none"> <li>1. Kambiranani momwe chikondi cha Mulungu ndi kukhululukira kwa Mulungu zitingatilimbiksire ife.</li> <li>2. Kodi ife tingachite chiyani pofuna kusonyeze chikondi cha Mulungu?</li> </ol>

	<b>A5 – KALASI Lachitatu</b> Phunziro Loyamba – Moyo wa Petulo Mutu – Petulo alalikira	<b>A5 – KALASI Yachinayi</b> Phunziro Loyamba – Moyo wa Petulo Mutu – Pentekosite
	<p><b>Ndime Yowerenga:</b> <i>Machitidwe 2:1-43</i>  <b>Vesi Yoloweza:</b> <i>Machitidwe 1:8</i></p> <p><b>Ife tikuphunzira kuti:</b></p> <ol style="list-style-type: none"> <li>1. Mzimu Woyerwa waperekedwa kwa otsatira Yesu monga mphatso.</li> <li>2. Uthenga wa ophunzira unali wa kuti tikuyenera kutembenuka mtima kuti Mulungu atikhululukira.</li> </ol>	<p><b>Ndime Yowerenga:</b> <i>Machitidwe 2:1-42</i>  <b>Vesi Yoloweza:</b> <i>Machitidwe 2:38</i></p> <p><b>Ife tikuphunzira kuti:</b></p> <ol style="list-style-type: none"> <li>1. Pentekoste ndi chikondwerero cha Ayuda, chinkachitika tsiku la makumi asanu atakondwerera Paska.</li> <li>2. Mzimu Woyerwa anabwera tsiku la Pentekoste.</li> <li>3. Petulo atalalikira, Mpingo unayambika.</li> </ol>
<b>MAWU OYAMBA</b>	<ol style="list-style-type: none"> <li>1. Ganizira momwe ophunzira angamvere ngati zinthu pa miyoyo yaho zitasintha kwambiri. Sukulu yatsopano, nyumba yatsopano, zochitika zina, kusintha m'banja mwawo.</li> <li>2. Fotokozani kuti ophunzira ankayenera kusintha kwambiri chifukwa tsopano Ambuye apita kumwamba, ndipo iwo ankayenera kupitiriza ntchito yake.</li> </ol>	<ol style="list-style-type: none"> <li>1. Ganizirani za masiku obadwa, chikondwerero cha chaka, ndi zikondwerero za chipembedzo kuti ndi zofunika kwambiri m'mabanja. Ganizirani za masiku apadera amene akubwera m'myezi yamtsogolo.</li> <li>2. Mtundu wa Chiyuda unakondwerera Pentekoste imene inkachitika tsiku la makumi asanu atakondwerera Paska kukumbukira pamene anataluka m'dziklo la Igupto ndi pamenenso Mose analandira Malamulo pa Phiri la Sinai.</li> </ol>
<b>KUTSIRIZA</b>	<p><b>Perekani Nkhani ya m'Baibulo</b></p> <p><b>Kambiranani ndi Kufotokoza:</b></p> <ol style="list-style-type: none"> <li>1. Ophunzira ankadikira kubwera kwa Mzimu Woyerwa amene Yesu anawalonjeza. (<i>Machitidwe 1:8</i>)</li> <li>2. Pa tsiku la Pentekoste Mzimu Woyerwa anabwera monga mmene akufotokozena pa <b>vesi 2-3</b>.</li> <li>3. Ophunzira anayamba kuyankhula ziyankhulo zina kuti anthu ochokera ku mayiko ena ambiri amene anabwera ku Yerusalemku phwando limeneli athe kumva zomwe ankayankhula.</li> <li>4. Anthu ena anakti ophunzirawa aledzera vinyo.</li> <li>5. Petulo akuyimirira ndi kufotokoza kwa anthuwo zomwe zachitika. Iye akuwafotokozena kuti uneneri wa Yoweli wakwanirtsidwa ndipo Mzimu Woyerwa wabwera. (<i>Yoweli 2:28-32</i>)</li> <li>6. Molimba mtima akuwauza kuti iwo ndi amene anapha Yesu koma Mulungu anamuukitsa kwa akufa.</li> <li>7. Anthu anakhudzika kwambiri ndipo anafunsa chomwe ankayenera kuchita.</li> <li>8. Petulo anawauza kuti ankayenera kutembenuka mtima ndi ku batizidwa ndipo tsiku limenelo anthu zikwi zitatu anakhala otsatira a Yesu.</li> </ol> <p><b>Fotokozani Vesi Yoloweza ndipo limbikitsani ophunzira kuti aloweze.</b></p> <p><b>Tsirizani Phunziro Loyamba.</b></p> <p><b>Kuonetsa:</b> Onani FBI pa Zoonjezera B – Petulo alalikira.</p>	<p><b>Perekani Nkhani ya m'Baibulo</b></p> <p><b>Kambiranani ndi Kufotokoza:</b></p> <ol style="list-style-type: none"> <li>1. Lonjezo la Ambuye Yesu linakwanirtsidwa pamene ophunzira analandira Mzimu Woyerwa pa Tsiku la Pentekoste.</li> <li>2. Fotokozani zomwe zinachitika Mzimu Woyerwa atabwera.</li> <li>3. Petulo anati mtundu wa Ayuda ndi umene unapha Yesu, koma Mulungu anamuukitsa kwa akufa ndipo ali kudzanja lamanja la Mulungu Kumwamba ndipo tsopano watumiza Mzimu Woyerwa.</li> <li>4. Anthu anatsutsika mu mtima chifukwa chochita cholakwika. (<i>2:37</i>)</li> <li>5. Iwo amene anakhulupirira tsiku limeneli anakhala ziwalo zoyamba za Mpingo. Mpingo unayamba tsiku limeneli ndipo ulipo mpaka lero.</li> <li>6. <i>Kambiranani zomwe zinachitika kwa anthu amene anakhulupirira. (Onani vesi 38-39.)</i></li> <li>7. <i>Taonani zomwe anachita zosonyeza kuti miyoyo yaho inasinthadi. (Onani vesi 42.)</i></li> </ol> <p><b>Fotokozani Vesi Yoloweza ndipo limbikitsani ophunzira kuti aloweze.</b></p> <p><b>Tsirizani Phunziro Loyamba.</b></p> <p><b>Kuonetsa:</b> Onani FBI pa Zoonjezera B – Pentekosite.</p>
<b>KUKUMBUTSANA</b>	<ol style="list-style-type: none"> <li>1. Ganizirani za mphamvu zomwe Mzimu Woyerwa amapereka kuti tikhale mboni.</li> <li>2. Kambiranani za kufunika kofalitsa Nkhani Yabwino pa dziko lonse lapansi.</li> <li>3. Kambiranani m'magulu, njira zimene ophunzira angatsatire pochitira umboni sabata ino.</li> <li>4. Fufuzani zomwe anthu ankapereka ngati malipiro a kutembenuka mtima zaka zambiri za m'buyomo.</li> </ol>	<ol style="list-style-type: none"> <li>1. Talingalirani kuti zinatheka bwanji kuti Petulo amene anali wa mantha, alalikire molimba mtima za Yesu.</li> <li>2. Werengani ndime zonse ndipo mulembe fundo zisanu zofunika zimene Petulo anayankhula za Yesu.</li> </ol>
<b>KHALANI MOYO UMENEWU</b>	<p><b>Zomwe tikuphunzira m'phunziroli:</b></p> <ol style="list-style-type: none"> <li>1. Kodi zikutanthauza chiyani kuhala mboni?</li> <li>2. Kodi kutembenuka mtima kumatanthauza chiyani?</li> </ol>	<p><b>Zomwe tikuphunzira m'phunziroli:</b></p> <ol style="list-style-type: none"> <li>1. Kambiranani za kufunika kwa ntchito ya Mzimu Woyerwa.</li> <li>2. Kambiranani za ubwino osonkhana pamodzi pa chiyanjano monga Mpingo.</li> <li>3. Pezani dzina la Mpingo umene unkakula mofulumira ndipo tchulani zomwe zinkachitika.</li> </ol>

	<p><b>A5 – KALASI Lachitatu</b>  <b>Phunziro Lachiwiri – Moyo wa Petulo</b>  <b>Mutu – Petulo achiritsa munthu</b></p>	<p><b>A5 – KALASI Yachinayi</b>  <b>Phunziro Lachiwiri – Moyo wa Petulo</b>  <b>Mutu – Kuchiritsa munthu wolumala</b></p>
	<p><b>Ndime Yowerenga:</b> <i>Machitidwe 3:1-16</i>  <b>Vesi Yoloweza:</b> <i>Machitidwe 3:6</i></p> <p><b>Ife tikuphunzira kuti:</b></p> <ol style="list-style-type: none"> <li>1. Ambuye ali ndi mphamvu zochiritsa zifooko ndi matenda onse.</li> <li>2. Iye angathe kusintha miyoyo yathu ngati tamukhulupirira.</li> </ol>	<p><b>Ndime Yowerenga:</b> <i>Machitidwe 3:1-26</i>  <b>Vesi Yoloweza:</b> <i>Machitidwe 4:10</i></p> <p><b>Ife tikuphunzira kuti:</b></p> <ol style="list-style-type: none"> <li>1. Inali mphamvu ya Mulungu yomwe inachiritsa munthu wolumala uja osati ophunzira ayi.</li> <li>2. Mulungu amatiyika ife pa malo oyenera pa nthawi oyenera kuti tigwire ntchito yake.</li> </ol>
<b>MAWU OYAMBA</b>	<p>Petulo ndi ophunzira ena sakanatha kuiywala fanizo la Msamariya Wachifundo limene Yesu anawaphunzitsa za kufunika "kokonda anansi athu". (<i>Luke 10:25-37</i>) Pamene iwo anaona munthuyu anadziwa kuti ankayenera kuchita zomwe Yesu akanachita.</p>	<p>Chimodzi mwa ziphunzitso zofunika kwambiri za Ambuye Yesu ndi chosamalira anthu ena. Iye ankaonetsa ophunzira ake nthawi zambiri chikondi chake pa munthu aliyense, makamaka kwa anthu osowa. Iye anawauza kuti akapita, ophunzirawo adzachita zazikulu zoposa zomwe lye anachita. (<i>Yohane 14: 12</i>)  Ganizirani zimenezi pamene tikuona chodabwitsa choyamba chomwe Petulo anachita.</p>
<b>KUTSIRIZA</b>	<p><b>Perekani Nkhani ya m'Baibulo</b></p> <p><b>Kambiranani ndi Kufotokoza:</b></p> <ol style="list-style-type: none"> <li>1. Petulo ndi Yohane akupita ku Nyumba ya Mulungu kukapemphera.</li> <li>2. Iwo akumana ndi munthu amene anabadwa wosayenda ndipo anali ndi zaka makumi anayi.</li> <li>3. Munthuyo akupempha ndalamala, koma Petulo akuyankhula kuti ali ndi chinthu china choposa ndalamala; iye atha kuchiritsidwa.</li> <li>4. Iye anathandiza munthuyo kuti ayimirire ndipo kenaka munthuyo anayamba kulumphalumpha, ndipo anayenda ndi kulowa m'Nyumbayo akuyamika Mulungu. Ichi chinali chodabwitsa choyamba mu Mpingo woyambawu.</li> <li>5. Pamene gulu la anthu linasonkhana, Petulo anafotokoza kuti munthuyo sanadzichiritsye yekha kapenanso ndi Petulo koma m'dzina la Yesu amene anthuwo anamupachika. (<i>Onani vesi 16.</i>)</li> <li>6. Onani kutsindika kwa kufunika kwa chikhulupiro cha munthuyo pa <b>vesi 16.</b></li> </ol> <p><b>Fotokozani Vesi Yoloweza ndipo limbikitsani ophunzira kuti aloweze.</b>  <b>Tsirizani Phunziro Lachiwiri.</b></p> <p><b>Kuonetsa:</b> Onani FBI pa Zoonjezera B – Petulo achiritsa munthu.</p>	<p><b>Perekani Nkhani ya m'Baibulo</b></p> <p><b>Kambiranani ndi Kufotokoza:</b></p> <ol style="list-style-type: none"> <li>1. Pasanathe masiku ambiri Pentekoste itachitika, Petulo ndi Yohane anakapita ku Nyumba ya Mulungu kukapemphera.</li> <li>2. Iwo ataona munthu wolumala, anadziwa zomwe Ambuye Yesu akanachita.</li> <li>3. Mwachikhulupiro, Petulo anathandiza munthuyo kuyimirira. Nthawi yomweyo munthuyo anachiritsidwa ndipo anayamba kuyenda ndi kulumphalumpha ndi kulowa m'Nyumbayo akuyamika Mulungu.</li> <li>4. Iye anachiritsidwa nthawi yomweyo; monga zodabwitsa zambiri zimene Yesu anachita.</li> <li>5. Mphamvu za Ambuye Yesu zinayamba kuonekera tsopano mwa atumwi ake kudzera mwa Mzimu Woyeram amene anali mwa iwo.</li> <li>6. Kambiranani za fundo zazikulu za uthenga wa Petulo pomwe ankafotokoza za Yesu ndi zomwe angachite lero!</li> <li>7. <i>Ganizirani momwe Petulo anagwiritsira ntchito mpata umenewu kuthandiza munthu wina.</i></li> </ol> <p><b>Fotokozani Vesi Yoloweza ndipo limbikitsani ophunzira kuti aloweze.</b>  <b>Tsirizani Phunziro Lachiwiri.</b></p> <p><b>Kuonetsa:</b> Onani FBI pa Zoonjezera B – Kuchiritsa munthu wolumala.</p>
<b>KUKUMBUTSANA</b>	<ol style="list-style-type: none"> <li>1. Ganizani za chodabwitsa cha machiritso ndiponso zakutisi onse odwala amene amachiritsidwa.</li> <li>2. Kambiranani kufunika koti Akhristu azichitira umboni kwavo (Yerusalemu wathu) asanapite kumalekezero a dziko lapansi.</li> <li>3. Pezani munthu lero amene anachiritsidwa modabwitsa.</li> <li>4. Kambiranani za kusinthika kumene Yesu amabweretsa m'miyoyo yathu tikamukhulupirira.</li> </ol>	<ol style="list-style-type: none"> <li>1. Ganizirani zifukwa zomwe zinachititsa kuti Petulo asinthe kwambiri atakana Ambuye.</li> <li>2. Kambiranani za kufunika kokhala ndi nthawi yapadera ndi Yesu pa ntchito yochitira umboni tsiku ndi tsiku.</li> <li>3. Khalani ndi nthawi yopemphera pamodzi ndi Akhristu ena kuti Mulungu akupatseni mphamvu ndi mpata omutumikira lye.</li> </ol>
<b>KHALANI MOYO UMENEWU</b>	<p><b>Zomwe tikuphunzira m'phunziroli:</b></p> <ol style="list-style-type: none"> <li>1. Kodi inu mukuganiza kuti ndi chifukwa chiyani Mulungu sachiritsa anthu onse?</li> <li>2. Kodi ife tingadalire Mulungu motani tsiku ndi tsiku?</li> </ol>	<p><b>Zomwe tikuphunzira m'phunziroli:</b></p> <ol style="list-style-type: none"> <li>1. Kodi mungazindikire bwanji kuti muli pamalo pamene Mulungu akufuna kuti mupezekepo?</li> <li>2. Kodi ife tingamuyamike motani Mulungu chifukwa chotikululukira machimo athu ndi kusintha miyoyo yathu?</li> </ol>

	<p><b>A5 – KALASI Lachitatu</b>  <b>Phunziro Lachitatu – Moyo wa Petulo</b>  <b>Mutu – Petulo achitira umboni</b></p>	<p><b>A5 – KALASI Yachinayi</b>  <b>Phunziro Lachitatu – Moyo wa Petulo</b>  <b>Mutu – Pamaso pa bwalo lalikulu la Ayuda</b></p>
	<p><b>Ndime Yowerenga:</b> <i>Machitidwe 4:1-22</i>  <b>Vesi Yoloweza:</b> <i>Machitidwe 4:12</i></p> <p><b>Ife tikuphunzira kuti:</b></p> <ol style="list-style-type: none"> <li>1. Mzimu Woyeranana anabweretsa kusintha kwakukulu m'moyo wa Petulo.</li> <li>2. Akhristu akuyenera kuyankhula za Ambuye mopanda mantha.</li> </ol>	<p><b>Ndime Yowerenga:</b> <i>Machitidwe 4:1-31</i>  <b>Vesi Yoloweza:</b> <i>Machitidwe 4:13</i></p> <p><b>Ife tikuphunzira kuti:</b></p> <ol style="list-style-type: none"> <li>1. Mulungu anamupatsa Petulo kulimba mtima ndi mphamvu zochitira umboni kwa akuluakulu achipembedzo.</li> <li>2. Okhulupirira akuyenera kukhala okonzeka kuza ena za Yesu ngakhale angakumane ndi zovuta zotani.</li> </ol>
<b>MAWU OYAMBA</b>	Bwerezani kuona zomwe zili m'phunziro lapita. Kumbutsani ophunzira kuti m'mayiko ena, munthu akayankhula za Ambuye Yesu mopanda mantha, amatha kuzunzidwa kapenango kuponyedwa m'ndende. Nthawi imeneyi Petulo ndi Yahane anazunzidwa ndi akuluakulu achipembedzo.	Kumbutsanani zomwe munaphunzira m'phunziro la m'mbuyo. Petulo analalikira uthenga wamphamvu. ( <i>Chapatala 3</i> ) Chiwerengero cha okhulupirira chinali 5,000. ( <i>4:4</i> ) Akuluakulu achipembedzo ankaganiza kuti pamene Ambuye anapachikidwa, anthu adzasiya kumutsatira. Koma tsopano akumutsatira ndi ochuluka kwambiri!
<b>KUTSIRIZA</b>	<p><b>Perekani Nkhani ya m'Baibulo</b></p> <p><b>Kambiranani ndi Kufotokoza:</b></p> <ol style="list-style-type: none"> <li>1. Akuluakulu achipembedzo anamva uthenga wa Petulo ndipo anakwyia kwambiri chifukwa udindo olalikira unali wawo, komanso chifukwa chakuti Petulo ankalalikira kuti Ambuye Yesu anali moyo.</li> <li>2. Petulo ndi Yohane anagwidwa ndipo anaponyedwa m'ndende.</li> <li>3. Tsiku lotsatira anayenera kuyima pamaso pa Gulu Lolamulira (bwalo la milandu yachipembedzo) monga anachitira Yesu.</li> <li>4. Iwo ankafuna kudziwa kuti Petulo anagwiritsa ntchito mphamvu za yani kuti munthuyo ayende.</li> <li>5. Petulo anawauza kuti zinali mphamvu za dzina la Yesu. (<i>4:10</i>)</li> <li>6. Atsogoleri achipembedzo anachita chidwi ndi kulimba mtima kwa Petulo ndi Yohane.</li> <li>7. Iwo anawauza kuti aleke kulalikira za Yesu.</li> <li>8. Petulo anati ankayenera kumvera Mulungu osati anthu.</li> </ol> <p><b>Fotokozani Vesi Yoloweza ndipo limbikitsani ophunzira kuti aloweze.</b></p> <p><b>Tsirizani Phunziro Lachitatu.</b></p> <p><b>Kuonetsa:</b> Onani FBI pa Zoonjezera B – Petulo achitira umboni.</p>	<p><b>Perekani Nkhani ya m'Baibulo</b></p> <p><b>Kambiranani ndi Kufotokoza:</b></p> <ol style="list-style-type: none"> <li>1. Petulo ndi Yohane amangidwa.</li> <li>2. Taonani ulamuliro wa Gulu Lolamulira (akuluakulu achipembedzo 71 nthawi imeneyo).</li> <li>3. Petulo anawauza akuluakuluwa molimba mtima kuti zinali mphamvu za Yesu zomwe zinachiritsa munthuyo, ndipo anawafotokozena kuti lye ndi Mpulumutsi mmodzi yekhayo. (<i>4:12</i>)</li> <li>4. Gulu Lolamulira linadabwa kwambiri ndi kulimba mtima kwa Petulo ndi Yohane ndipo anazindikira kuti anali ndi Yesu.</li> <li>5. Iwo anawauza kuti asiyé kulalikira dzina la Yesu. Koma Petulo anawauza kuti iwo adzamvera Mulungu osati Gulu Lolamuliralo.</li> <li>6. Petulo ndi Yohane anapita komwe kunali okhulupirira ena aja ndipo onse anapemphera kuti athe kulalikira uthenga molimba mtima. Onani momwe Mulungu anayankhira mapemphero awo m'njira yodabwitsa kwambiri.</li> </ol> <p><b>Fotokozani Vesi Yoloweza ndipo limbikitsani ophunzira kuti aloweze.</b></p> <p><b>Tsirizani Phunziro Lachitatu.</b></p> <p><b>Kuonetsa:</b> Onani FBI pa Zoonjezera B – Pamaso pa bwalo lalikulu la Ayuda.</p>
<b>KUKUMBUTSANA</b>	<ol style="list-style-type: none"> <li>1. Lembari mwachidule mitu yofunika ya chikhulupiriro cha Chikhristu yomwe iyenera kukhala maziko. Kumbukirani kuti Ambuye Yesu ndiye akuyenera kukhala maziko a chikhulupiriro cha okhulupirira. (<i>Ganizira vesi 12</i>.)</li> <li>2. Fufuzani za Mkhristu wotchuka amene ‘anayima mopanda mantha’ pa chikhulupiriro chake. Mwachitsanzo: Eric Liddell.</li> </ol>	<ol style="list-style-type: none"> <li>1. Kambiranani momwe ife tingakhaliire olimba pa chikhulupiriro chatu ndi kuchitira umboni.</li> <li>2. Fufuzani za ntchito za Open Doors kapena Barnabas Trust kuti muone momwe Akhristu angapambanire kumalo kumene kuli mazunzo.</li> </ol>
<b>KHALANI MOYO UMENEWU</b>	<p><b>Zomwe tikuphunzira m'phunziroli:</b></p> <ol style="list-style-type: none"> <li>1. Kodi chimatilepheretsa ife kuti tisauze ena za Yesu n'chiyan?</li> <li>2. Kodi zimatanthauza chiyani tikati wokhulupirira ndi ‘mwala wamoyo’? (<i>1 Petulo 2:4 ndi 5</i>)</li> </ol>	<p><b>Zomwe tikuphunzira m'phunziroli:</b></p> <ol style="list-style-type: none"> <li>1. Kodi ife tingadalire motani Mzimu Woyeranana kuti atithandize pamene tikuchitira umboni?</li> <li>2. Kodi zotsutsa Uthenga Wabwino zingakulitse motani chikhulupiriro chatu?</li> </ol>

	<b>A5 – KALASI Lachitatu</b> Phunziro Lachinayi – Moyo wa Petulo Mutu – Petulo m'ndende	<b>A5 – KALASI Yachinayi</b> Phunziro Lachinayi – Moyo wa Petulo Mutu – M'ndende
	<p><b>Ndime Yowerenga:</b> <i>Machitidwe 12:1-19</i>  <b>Vesi Yoloweza:</b> <i>1 Yohane 5:14</i></p> <p><b>Ife tikuphunzira kuti:</b></p> <ol style="list-style-type: none"> <li>1. Mazunzo ndi chinthu chomwe chimakhudza anthu a Mulungu.</li> <li>2. Baibulo limaphunzitsa kuti Mulungu amatikonda ndipo amadziwa zinthu zomwe ndi zabwino kwa ife.</li> </ol>	<p><b>Ndime Yowerenga:</b> <i>Machitidwe 12:1-19</i>  <b>Vesi Yoloweza:</b> <i>1 Yohane 5:5</i></p> <p><b>Ife tikuphunzira kuti:</b></p> <ol style="list-style-type: none"> <li>1. N'kofunika kudalira Mulungu monga anachitira Petulo, ngakhale nthawi zovuta kwambiri.</li> <li>2. Mulungu amachita zosathea ndi munthu, koma zotheka amatisiya kuti tichite.</li> </ol>
<b>MAWU OYAMBA</b>	<p>Ambuye Yesu ananena kuti monga dziko lapansi linamuda iye, choncho lidzadananso ndi atumwi ndi anthu onse a Mulungu. (<i>Yohane 15:18</i>) Yesu akanali wamng'ono, Herode ankafuna kumupha. Tsopano mdzukulu wake, Herode wina akufunanso kupha Petulo.</p>	<p>Fotokozani mwachidule zomwe zinachitika pamene Petulo anali m'ndende nthawi yoyamba ija. Panonso Petulo ali m'ndende chifukwa cha chikhulupiriro chake ndi kulakilira kwake. Iye mwina anali ndi chikhulupiriro chachikulu chomwe chinamuchititsa kugona m'ndende, usiku woti mawa lake akazengedwa mlandu. Kodi n'kuti Petulo atazindikira kale choonadi chomwe analemba m'tsogolo? (<i>1 Petulo 5:7</i>)</p>
<b>KUTSIRIZA</b>	<p><b>Perekani Nkhani ya m'Baibulo</b></p> <p><b>Kambiranani ndi Kufotokoza:</b></p> <ol style="list-style-type: none"> <li>1. Mfumu Herode anapha Yakobo ndipo atazindikira kuti zinasangalatsa Ayuda, iye anamanganso Petulo</li> <li>2. Petulo ali m'ndende, kudikira kuzengedwa mlandu.</li> <li>3. Mpingo unasonkhana kupempherera.</li> <li>4. Usiku woti mlandu uli mawa, mngele anabwera kudzatulutsa Petulo m'ndende.</li> <li>5. Iye anapita ku nyumba imene anzake ankapemphera.</li> <li>6. Mtsikana wantchito amene anatsekula chitseko anawauza kuti Petulo ali pa khomo, koma palibe amene anamukhulupirira.</li> <li>7. Kenaka anazindikira kuti Mulungu wayankha mapemphero awo.</li> <li>8. <i>Ganizirani za kufunika kwa chiyanjano choona pakati pa okhulupirira.</i></li> <li>9. <i>Ganizirani za momwe tingamapempherere nthawi zonse, ndi kuyembekezera kuti Mulungu ayankha ndiponso kuvomereza chifuniro cha Mulungu pa miyoyo yathu.</i></li> </ol> <p><b>Fotokozani Vesi Yoloweza ndipo limbikitsani ophunzira kuti aloweze.</b></p> <p><b>Tsirizani Phunziro Lachinayi.</b></p> <p><b>Kuonetsa:</b> Onani FBI pa Zoonjezera B – Petulo m'ndende.</p>	<p><b>Perekani Nkhani ya m'Baibulo</b></p> <p><b>Kambiranani ndi Kufotokoza:</b></p> <ol style="list-style-type: none"> <li>1. Mpingo unali ndi nkawa chifukwa cha Petulo ndipo unkamupempherera kwambiri.</li> <li>2. Petulo ankayang'aniridwa ndi asilikali 16 ndipo anamangiridwa kwa asilikali awiri.</li> <li>3. Mngele anabwera ndi kudzutsa Petulo, kumasula maunyolo ake ndi kumutulutsa m'ndende. Petulo anataluka m'ndende modabwitsa.</li> <li>4. Petulo anazindikira kuti anali Ambuye amene anamutulutsa.</li> <li>5. Iye anazindikira kuti mpingo unkamupempherera koma sunkakhulupirira kuti Mulungu angachite zinthu zosathekazi.</li> <li>6. Fotokozani zomwe zinachitika pamene Petulo anafika ku nyumba imene ankapemphera.</li> <li>7. Apa zikuoneka kuti Mulungu anali ndi ntchito yambiri yoti Petulo agwire. Iyi sinali nthawi yake yoti afe, choncho Mulungu analepheretsa zimenezi.</li> </ol> <p><b>Fotokozani Vesi Yoloweza ndipo limbikitsani ophunzira kuti aloweze.</b></p> <p><b>Tsirizani Phunziro Lachinayi.</b></p> <p><b>Kuonetsa:</b> Onani FBI pa Zoonjezera B – M'ndende.</p>
<b>KUKUMBUTSANA</b>	<ol style="list-style-type: none"> <li>1. Kambiranani chomwe chimalepheretsa Akhristu kupemphera nthawi zonse.</li> <li>2. Kambiranani za nthawi yomwe munazindikira kuti simukuchita chifuniro cha Mulungu.</li> <li>3. Pezani ndime ziwiri za m'Baibulo zomwe zikufotoza za kutsogozedwa ndi Mulungu ndipo mukambiranе pa gulu.</li> </ol>	<ol style="list-style-type: none"> <li>1. Ganizirani za kufunika kopemphera kwa Mulungu m'nthawi ya mavuto.</li> <li>2. Lingalirani za momwe tingapempherere ndi chiyembekezo kuti Mulungu ayankha.</li> <li>3. Funsani mnzanu/m'bale za momwe Mulungu anayankhira pemphero lawo ndipo afotokozena ena onse.</li> </ol>
<b>KHALANI MOYO UMENEWU</b>	<p><b>Zomwe tikuphunzira m'phunziroli:</b></p> <ol style="list-style-type: none"> <li>1. Kodi n'chifukwa chiyani nthawi zina njira za Mulungu zimakhala za chinsinsi (ena amachirtsidwa ena ayi)?</li> <li>2. Kodi mungazindikire bwanji chifuniro cha Mulungu pa miyoyo yanu?</li> </ol>	<p><b>Zomwe tikuphunzira m'phunziroli:</b></p> <ol style="list-style-type: none"> <li>1. Kodi n'chifukwa chiyani nthawi zambiri timakayika zoti Mulungu ayankha zomwe tamupempha?</li> <li>2. Kodi timadziwa bwanji kuti mphamvu za Mulungu ndi zoposa zathu?</li> </ol>

	<b>A6 – KALASI Lachitatu</b> <b>Phunziro Loyamba – Maulendo wa Abrahamu</b> <b>Mutu – Kukhulupirira Mulungu</b>	<b>A6 – KALASI Yachinayi</b> <b>Phunziro Loyamba – Abrahamu</b> <b>Mutu – Mayitanidwe ake</b>
<b>MAWU OYAMBA</b>	<p><b>Ndime Yowerenga:</b> <i>Genesis 12:1-9</i>  <b>Vesi Yoloweza:</b> <i>Ahebri 11:8</i></p> <p><b>Ife tikuphunzira kuti:</b></p> <ol style="list-style-type: none"> <li>1. Abramu anali munthu wachikhulupiro: lye analalira Mulungu ngakhale sankadziwa kumene Mulungu ankamutsogolera.</li> <li>2. Pamene Mulungu watiyitana, monga anachitira ndi Abramu, tikuyenera kumudalira, kumutsatira ndi kumumvera.</li> </ol>	<p><b>Ndime Yowerenga:</b> <i>Genesis 11:27-32; 12:1-9</i>  <b>Vesi Yoloweza:</b> <i>Machitidwe 7:2-4</i></p> <p><b>Ife tikuphunzira kuti:</b></p> <ol style="list-style-type: none"> <li>1. Abramu anali munthu wachikhulupiro: lye analalira Mulungu ngakhale sankadziwa kumene Mulungu ankamutsogolera.</li> <li>2. Pamene Mulungu watiyitana, monga anachitira ndi Abramu, tikuyenera kumudalira, kumutsatira ndi kumumvera. Kunena zonna, ife tikuyenera kupereka miyoyo yathu kwa lye.</li> </ol>
<b>KUTSIRIZA</b>	<p><b>Perekani Nkhani ya m'Baibulo</b></p> <p><b>Kambiranani ndi Kufotokoza:</b></p> <ol style="list-style-type: none"> <li>1. Mulungu anayankhula ndi Abramu ndipo anamuza kuti achoke ndi kupita ku dziko lina pamodzi ndi banja lake limene Mulungu adzamusonyeza. Izi sizinali zophweka kwa iye. Kuyenda nthawi ya Abramu kunali kovuta ndi kwa pang'ono pang'ono. Komanso iye anali ndi katundu wambiri oti anyamule pamodzinso ndi anthu.</li> <li>2. Mulungu anamulonjeza mwapadera kuti adzadalitsa Abramu ndi kupanga banja lake kukhala mtundu waukulu. Kudzera mu mtundu umenewu anthu onse a pa dziko lapansi adzadalitsida.</li> <li>3. Abramu anayamba ulendo wake pamodzi ndi mdzukulu wake Loti ndi mkazi wake Sarai. Iwo ananyamula katundu wawo yense. Abramu anali ndi zaka 75!</li> <li>4. Atayenda kwa kanthawi, Yehova anaonekera kwa Abramu pamalo otchedwa Sekemu. Iye anauza Abramu kuti adzapereka dziko limenelo kwa zidzukulu zake.</li> <li>5. Abramu anamanga guwa lansembe ndipo anapembedza Yehova. Kenaka anapitanso ku mapiri a pakati pa Beteli ndi Ai ndipo anamangako tenti yake. Kumenekonso anamanga guwa lansembe ndi kupembedza Yehova. Kuchoka kumeneko analowera mbali ya ku chipululu cha Negevi.</li> </ol> <p><b>Fotokozani Vesi Yoloweza ndipo limbikitsani ophunzira kuti aloweze.</b>  <b>Tsirizani Phunziro Loyamba.</b></p> <p><b>Kuonetsa:</b> Onani FBI pa Zoonjezera B – Kukhulupirira Mulungu.</p>	<p><b>Zokambirana mukuyenda.</b> Funsani gulu kuti liyerekeze kuti likukonzekera ulendo wautali kupita ku dziko limene sanapiteko n'kale lomwe, ndipo azikakhala kumeneko. Kodi pali mavuto otani kwa iwo? (Kwa Abramu ndi banja lake ena mwa mavuto amene akanumana nawo anali monga chiyankhulo, chakudy, nyengo ndi miyambo komanso kukhala kutali ndi abale ake.) Lembanji mawu amodzi pa pepala limodzinso la A4: KUKAYIKIRA; KUDANDAULA; KUSANGALALA; KUDA NKHAWA; KUNYINYIRIKA. Matani mapepalawa pa khoma pamalo osiyana. Funsani ophunzira kuti apite ndi kukayima pamene pali pepala lomwe likufotoza bwino za iwo. Kambiranani za zisankho zawo: N'chifukwa chiyani akuona motero?</p>
<b>KUKUMBUTSANA</b>	<p>Jambulani mapu a ulendo wa Abramu kuchokera ku Harani mpaka ku Beteli ndipo mulembepo mayina a malo amene akutchulidwa m'nkhani imeneyi. Onetsetsani kuti mwayikapo Moreya ndi maguwa awiri amene Abramu anamanga ndi kupembedza Mulungu.</p>	<p><b>Fotokozani Vesi Yoloweza ndipo limbikitsani ophunzira kuti aloweze.</b>  <b>Tsirizani Phunziro Loyamba.</b></p> <p><b>Kuonetsa:</b> Onani FBI pa Zoonjezera B – Mayitanidwe ake.</p>
<b>KHALANI MOYO UMENEWU</b>	<p><b>Zomwe tikuphunzira m'phunziroli:</b></p> <ol style="list-style-type: none"> <li>1. Abramu anamvera Mulungu pamene anamuza kuti ayambe ulendo wake, ngakhale zinali zovuta kutero. Kodi izi zikuonetsa chiyani za khalidwe lake?</li> <li>2. Kodi chikhulupiro chathu mwa Mulungu chimakhudza motani makhalidwe athu a tsiku ndi tsiku, ngakhale mu nyengo imene sitikumvetsetsa zomwe zikuchitika?</li> </ol>	<p><b>Zomwe tikuphunzira m'phunziroli:</b></p> <ol style="list-style-type: none"> <li>1. Kambiranani m'magulu - Abramu anamvera Mulungu. Kodi izi zikuonetsa motani za maganizo a Abramu pa Mulungu?</li> <li>2. Ganizani nthawi imene kumvera Mulungu kumakhala kovuta.</li> <li>3. Kodi nkhanzi ya Abramu ikutiphunzitsa kuti tizikhala motani, ngakhale tilibe chitsimikizo, tikunyinyirika kapena kudandaula?</li> </ol>

	<p><b>A6 – KALASI Lachitatu</b>  <b>Phunziro Lachiwiri – Maulendo wa Abrahamu</b>  <b>Mutu – Zisankho</b></p>	<p><b>A6 – KALASI Yachinayi</b>  <b>Phunziro Lachiwiri – Abrahamu</b>  <b>Mutu – Chisankho chake</b></p>
	<p><b>Ndime Yowerenga:</b> <i>Genesis 13:1-18</i>  <b>Vesi Yoloweza:</b> <i>Miyambo 3:5-6</i></p> <p><b>Ife tikuphunzira kuti:</b></p> <ol style="list-style-type: none"> <li>1. N'kofunika kuchita zisankho zoyenera pa miyoyo yathu.</li> <li>2. Ife tikuyenera kuperempha Mulungu kuti atithandize kuchita zisankho ndi ziganizo zabwino. Tipemphe kuti azitsogolera.</li> <li>3. Tikuyenera kukumbukira kuyamika Mulungu ndi kumupembedza.</li> </ol>	<p><b>Ndime Yowerenga:</b> <i>Genesis 13:1-18; 14:1-16</i>  <b>Vesi Yoloweza:</b> <i>Yoswa 24:15</i></p> <p><b>Ife tikuphunzira kuti:</b></p> <ol style="list-style-type: none"> <li>1. Abramu anafuna kuti Mulungu azimutsogolera ndi kumuthandiza nthawi zonse. Iye ankayamika Mulungu nthawi zambiri.</li> <li>2. Ife tikuyenera kuvomereza Mulungu pa zonse zimene timachita, kufuna thandizo lake, chitsogozo chake ndi kumuyamika pa zonse ndi kumupatsa ulemu chifukwa cha madalitso a pa miyoyo yathu.</li> <li>3. Taganizirani zisankho zomwe timachita tsiku lililonse. Ganizani za zisankho zabwino ndi zisankho zoyipa.</li> <li>4. Kutumikira Mulungu ndi chisankho chabwino.</li> <li>5. Kodi ndi kusiyana kotani komwe tingakuone m'moyo mwa anthu amene anasankha kutumikira Mulungu?</li> <li>6. Lembani zimenezi pa chipepala ndipo muzikumbukire pamene tikuphunzira za moyo wa Abramu m'phunziro lino.</li> </ol>
<b>MAWU OYAMBA</b>	<ul style="list-style-type: none"> <li>• Tonse timasankha ndi kuchita ziganizo tsiku lililonse. Funsani gulu kuti liperekere zitsanzo zazing'ono za zisankho zawo za tsiku ndi tsiku ndipo kenaka atchulenso zisankho zomwe zimasinthia moyo wa munthu. Lembani zimenezi pa mapepala awiri.</li> <li>• Perekani kwa munthu aliyense pepala. Mbali imodzi ajambule chithunzi kuyimira zisankho zassing'ono zomwe iwo anachita posachedwapa. Mbali inayo ajambule chithunzi chomwe chikuyimira chiyembekezo chawo, maloto awo kapena zokhumba zawo za m'tsogolo. M'magulu ang'onoang'ono akambilane za zithunzi zawo.</li> <li>• Fotokozani kuti aliyense wa ife amachita zisankho ndi ziganizo ndipo timafuna thandizo ndi chitsogozo pachita zimenezi. Ife titha kudalira Mulungu kuti adzatisogolera bwino pa zisankho zonse tizichita.</li> </ul>	
<b>KUTSIRIZA</b>	<p><b>Perekani Nkhani ya m'Baibulo</b></p> <p><b>Kambiranani ndi Kufotokoza:</b></p> <ol style="list-style-type: none"> <li>1. Abramu anapitanso kumalo amene nthawi ina anakhalako, pakati pa Beteli ndi Ai. Iye anamanga guwa lansembe la Yehova, ndipo anapemphera m'dzina la Yehova.</li> <li>2. Abramu ankayenera kuchita chisankho. M'dzikomo munkakhala anthu ambiri ndipo ankakangana nthawi zambiri. M'dzikomo munalibe malo okwanira aliyense, tsopano inali nthawi yoti Abramu ndi mdzukulu wake Loti asiyane ndi kukakhala ku malo osiyana.</li> <li>3. Abramu anamupatsa Loti mwayi oti asankhe kumene akufuna kupta kukakhala.</li> <li>4. Loti anasankha dziko lachonde, ku chigwa cha mtsinje wa Yorodani kumene kunali madzi wokwanira ndipo anasankha kukhala mu mzinda umodzi kumeneko.</li> <li>5. Abramu anakhala m'dziko la Kanaani.</li> <li>6. Iye atasiyana ndi Loti, Yehova anayankhula ndi Abramu ndi kumulonjeza kuti dziko lonse lomwe ankaliona lidzakhala lake: kumpoto, kummwera, kummawa ndi kumadzulo.</li> <li>7. Mulungu analonjeza Abramu kuti adzakhala ndi ana ochuluka kwambiri amene adzakhale m'dzikomo.</li> <li>8. Abramu anakakhala kufupi ndi mitengo yayikulu ku Mamure, ku Hebron. Iye anamanga guwa lansembe kumeneko ndipo anapembedza Yehova.</li> </ol> <p><b>Fotokozani Vesi Yoloweza ndipo limbikitsani ophunzira kuti aloweze.</b></p> <p><b>Tsirizani Phunziro Lachiwiri.</b></p> <p><b>Kuonetsa:</b> Onani FBI pa Zoonjezera B – Zisankho.</p>	<p><b>Perekani Nkhani ya m'Baibulo</b></p> <p><b>Kambiranani ndi Kufotokoza:</b></p> <ol style="list-style-type: none"> <li>1. Abramu ankayenera kuchita chisankho. Panali anthu ambiri amene ankakhala m'dzikolo ndipo ankakangana chifukwa cha msipu wa ziweto zawo. Inali nthawi yoti Abramu asiyane ndi mdzukulu wake Loti ndi kupta ku dera lina.</li> <li>2. Abramu anamupatsa mwayi Loti oti asankhe kumene akufuna kupta kuhala. Loti anasankha dziko lachonde, ku chigwa cha mtsinje wa Yorodani kumene kunali madzi wokwanira ndipo anasankha kukhala mu mzinda umodzi kumeneko.</li> <li>3. Abramu anakhala m'dziko la Kanaani.</li> <li>4. Loti atachoka, Yehova anamulonjeza Abramu dziko lonse limene ankaliona ku mbali zonse. Mulungu anamulonjeza Abramu kuti adzakhala ndi ana ochuluka kwambiri ndipo dzikolo lidzakhala lawo.</li> <li>5. Abramu anamanga guwa lansembe ndipo anapembedza Yehova.</li> <li>6. Abramu ankakhala nthawi imene kunali mikangano. Adani a Sodomu, kumene Loti ankakhala, anathira nkondo mzindawo ndi kumugwira Loti ndi anthu ena onse pamodzi ndi katundu wawo.</li> <li>7. Pamene Abramu anamva zimenezi, iye anapita ndi gulu lake la nkondo kukathira nkondo adaniwo ndipo analanda katundu yense ndi kupulumutsa anthu onse. Abramu anawagonjetesa ankhondo onse. Iye sanalole kuti Mfumu ya Sodomu imulipire chifukwa anali Mulungu amene anamupatsa mphamu zogonjetsera adani ake.</li> </ol> <p><b>Fotokozani Vesi Yoloweza ndipo limbikitsani ophunzira kuti aloweze.</b></p> <p><b>Tsirizani Phunziro Lachiwiri.</b></p> <p><b>Kuonetsa:</b> Onani FBI pa Zoonjezera B – Chisankho chake.</p>
<b>KUKUMBUTSANA</b>	<p>Lembani mutu wa nkhani ya mu nyazi ndi kulemba nkhani yayifupi yofotokoza za phunziro lathu lero. Mu nkhaniyo mukhale fundo zonse zofunika za m'phunziroli. Muchite zimenezi m'magulu kapena anthu awiriawiri. Matani pa khoma kapena kambiranani zomwe mwalembezo.</p>	<ol style="list-style-type: none"> <li>1. Kodi Abramu anachita chiyani pofuna kuonetsa kuti iye ndi mtumiki wa Yehova kuchokera pa zomwe mwawerenga m'phunziroli?</li> <li>2. Onaniso makhalidwe a atumiki a Mulungu omwe mwalembe mmene mumayamba phunziroli. Kodi chilipo china chomwe munakafuna kuonjezera kapena kusintha? Kodi kutumikira Yehova kungasinthe motani moyo waru lero?</li> </ol>
<b>KHALANI MOYO UMENEWU</b>	<p><b>Zomwe tikuphunzira m'phunziroli:</b></p> <ol style="list-style-type: none"> <li>1. Abramu ankafunsa Mulungu pa zisankho ndi ziganizo zake ndipo Mulungu anamudalitsa.</li> <li>2. Ganizirani za kufunsa Mulungu kuti akutsogolereni pamene mukuchita zisankho ndi ziganizo zofunika kwambiri za moyo waru.</li> </ol>	<p><b>Zomwe tikuphunzira m'phunziroli:</b></p> <p>Mupatseni ophunzira aliyense kadi yosalembapo kanthu. Afunsemi kuti aganizire njira imodzi yomwe angatumikire Yehova mokhulupirika. Iwo alembe pemphero lawo la zimenezi pa kadi ndipo apite nalo ku nyumba kwavo ngati chikumbutso cha phunziroli.</p>

	<p><b>A6 – KALASI Lachitatu</b>  <b>Phunziro Lachitatu – Maulendo wa Abrahamu</b>  <b>Mutu – Malonjezo a Mulungu</b></p>	<p><b>A6 – KALASI Yachinayi</b>  <b>Phunziro Lachitatu – Abrahamu</b>  <b>Mutu – Chitsimikizo chake</b></p>
	<p><b>Ndime Yowerenga:</b> <i>Genesis 17:1-8; 18:1-15; 21:1-5</i>  <b>Vesi Yoloweza:</b> <i>Mateyu 1:21</i></p> <p><b>Ife tikuphunzira kuti:</b></p> <ol style="list-style-type: none"> <li>1. Ngakhale Abramu anayesera kupeza njira yothetsera mavuto ake, Mulungu sanamutaye.</li> <li>2. Mulungu anatsimikiza lonjezo lake kwa Abramu lakuti iye adzakhala atate wa mitundu yambiri. Izi zikutanthauza kuti madalitso sadzakhala a Abramu yekha komanso a anthu onse m'mibado yonse.</li> <li>3. Nthawi zina timatha kukayikira malonjezo a Mulungu chifukwa amaoneka ngati sangattheke. Ife timayesera kupeza njira zathu zothetsera mavuto athu. Phunziro lino likutilimbikitsa kuti tikhulupirire malonjezo a Mulungu ndi kudikira mpaka atakwaniritsidwa.</li> </ol>	<p><b>Ndime Yowerenga:</b> <i>Genesis 15:1-7; 17:1-19; 18:1-15</i>  <b>Vesi Yoloweza:</b> <i>Genesis 18:14</i></p> <p><b>Ife tikuphunzira kuti:</b></p> <ol style="list-style-type: none"> <li>1. Mulungu analonjeza Abramu kuti adzakhala ndi mwana amene adzakhale mlowam'malo wake. Abramu anakhulupirira Mulungu, koma iye ndi mkazi wake anali okalamba ndipo analibe mwana ndi mmodzi yemwe. Iwo anayesera kupeza njira yothetsera vuto limeneli okha.</li> <li>2. Mulungu sanakhumudwe ndi Abramu ndi Sarai. Mulungu anatsimikiza lonjezo lake lakuti Abramu adzakhala atate wa mitundu yambiri.</li> <li>3. Nthawi zina timatha kukayikira malonjezo a Mulungu chifukwa amaoneka ngati sangattheke. Ife timayesera kupeza njira zathu zothetsera mavuto athu. Phunziro lino likutilimbikitsa ife kuti tikhulupirire malonjezo a Mulungu ndi kudikira mpaka atakwaniritsidwa.</li> </ol>
<b>MAWU OYAMBA</b>	<ul style="list-style-type: none"> <li>• Funsani gulu ngati alipo ena amene analonjezapo. Kodi alipo amene analonjeza wina pa gulu lino? Lembanji malonjezo amenewo pa chipepala.</li> <li>• Nthawi zina anthu sasunga malonjezo awo. Kodi zifukwa zake n'zotani? (Kambiranani ndi gulu.) Phunziro lino tikuphunzitsa kuti Mulungu amasunga malonjezo ake, ngakhale kuti nthawi zina zimaoneka ngati sadzakwaniritsidwa.</li> </ul>	<ul style="list-style-type: none"> <li>• Pa khoma kapena pa chipepala, lembani malonjezo amene anthu amachita lero lino (ukwati, lumbiro, mgwirizano, kulowa usilikali, ngongole ndi ena ambiri).</li> <li>• Kambiranani momwe anthu amakwaniritsira kapena kuphwanyira malonjezo amenewa. Phunziro la lero tikuphunzira kuti Mulungu amasunga malonjezo ake nthawi zonse.</li> </ul>
<b>KUTSIRIZA</b>	<p><b>Perekani Nkhani ya m'Baibulo</b></p> <p><b>Kambiranani ndi Kufotokoza:</b></p> <ol style="list-style-type: none"> <li>1. Mulungu analonjeza Abramu kuti adzakhala ndi ana ambiri.</li> <li>2. Abramu ndi mkazi wake Sarai anali okalamba ndipo anayesera kupeza njira yavo yothetsera mavuto awo.</li> <li>3. Komatu Mulungu sanaphwanye lonjezo lake. Iye anabwerezanzo kutsimikizira Abramu and Sarai. Iye anawapatsa mayina atsopano monga chizindikiro cha lonjezo lake – Iwo anatchedwa Abrahamu ndi Sara.</li> <li>4. Mulungu anamuza Abrahamu kuti adzakhala atate wa mitundu yambiri. Iye analonjeza kuti adzapereka dzikolo kwa Abrahamu ndi zidzukulu zake, ndi kuti iye adzakhala Mulungu wawo.</li> <li>5. Amuna atatu anabwera kudzacheza ndi Abrahamu. Abrahamu anawasamalira bwino anthuwo.</li> <li>6. Yehova anauza Abrahamu kuti Sara adzabereka mwana wa mwamuna nthawi ngati yomwego chaka chamawa. Sara anaseka pamene anamva mawu ameneva chifukwa iye ndi Abrahamu anali okalamba kwambiri kuti akhale ndi ana.</li> <li>7. Mulungu anasunga lonjezo lake ndipo Sara anabereka mwana wa mwamuna.</li> <li>8. Abrahamu ndi Sara anamutcha mwanayo Isake, kutanthauza "kuseka" chifukwa Yehova anakwaniritsa lonjezo lake limene linkaoneka ngati losatheka, ndipo anabweretsa chimwemwe chachikulu mu ukalamba wawo.</li> </ol> <p><b>Fotokozani Vesi Yoloweza ndipo limbikitsani ophunzira kuti alowewe.</b>  <b>Tsirizani Phunziro Lachitatu.</b></p> <p><b>Kuonetsa:</b> Onani FBI pa Zoonjezera B – Malonjezo a Mulungu.</p>	<p><b>Perekani Nkhani ya m'Baibulo</b></p> <p><b>Kambiranani ndi Kufotokoza:</b></p> <ol style="list-style-type: none"> <li>1. Mulungu analonjeza Abramu kuti adzakhala ndi ana ambiri.</li> <li>2. Abramu ndi mkazi wake Sarai anali okalamba ndipo anayesera kupeza njira yavo yothetsera mavuto awo. (Onani Chapatala 16.)</li> <li>3. Mulungu sanakhumudwe nawo. Iye anawatsimikizira lonjezo lake. Mulungu anapereka kwa Abramu ndi Sarai mayina atsopano. Iwo tsopano adzayamba kutchedwa Abrahamu ndi Sara, monga chikumbutso cha lonjezo lake.</li> <li>4. Mulungu anauza Abrahamu kuti adzakhala atate wa mitundu yambiri. Iye analonjeza kuti adzapereka dziko limeneli kwa Abrahamu ndi zidzukulu zake, ndipo iye adzakhala Mulungu wawo.</li> <li>5. Amuna atatu anabwera kudzacheza naye, iye anawasamalira bwino anthuwo,</li> <li>6. Mmodzi mwa alendowo (Yehova) anamuza Abrahamu kuti Sara adzakhala ndi mwana wa mwamuna nthawi ngati yomwego chaka chamawa. Sara anaseka, chifukwa iye ndi Abrahamu anali okalamba kwambiri kuti akhale ndi ana.</li> <li>7. Mulungu anasunga lonjezo lake ndipo Sara anabereka mwana wa mwamuna!</li> <li>8. Abrahamu ndi Sara anamutcha mwanayo Isake, kutanthauza "kuseka" chifukwa Yehova anakwaniritsa lonjezo lake limene linkaoneka ngati losatheka, ndipo anabweretsa chimwemwe chachikulu mu ukalamba wawo.</li> </ol> <p><b>Fotokozani Vesi Yoloweza ndipo limbikitsani ophunzira kuti alowewe.</b>  <b>Tsirizani Phunziro Lachitatu.</b></p> <p><b>Kuonetsa:</b> Onani FBI pa Zoonjezera B – Chitsimikizo chake.</p>
<b>KUKUMBUTSANA</b>	<p>Werengani Vesi Yoloweza. Gwiritsani ntchito lonjezo lili pamene na ndipo mupange pepala loyika m'buku. Nthawi zonse mukaona pepalalo, muzikumbukira kuti Mulungu amasunga malonjezo ake, ngakhale nthawi zina zimaoneka ngati ndi zosatheka kwa ife.</p>	<p>M'magulu ang'onoang'ono: Kodi tikuphunzira chiyani za khalidwe la Mulungu, Abrahamu ndi Sara m'phunziro lino? Ophunzira alemba maganizo awo pa pepala ndipo kenaka gulu lonse likambiranе.</p>
<b>KHALANI MOYO UMENEWU</b>	<p><b>Zomwe tikuphunzira m'phunziroli:</b></p> <ul style="list-style-type: none"> <li>• Kodi inu mukudalira Mulungu?</li> <li>• Kodi mumakhulupirira malonjezo ake amene ali m'Mawu a Mulungu?</li> <li>• Kodi phunziro ili lalimbita motani chikhulupiriro chanu mwa Mulungu?</li> </ul>	<p><b>Zomwe tikuphunzira m'phunziroli:</b></p> <p>Kodi zilipo zinthu pa moyo wanu zomwe mukuona ngati kuti Mulungu sangathe kuchitapo kanthu? Kodi mwaphunzira chiyani chokulimbikitsani kudalira Mulungu mbali zonse za moyo wanu?</p>

	<p><b>A6 – KALASI Lachitatu</b>  <b>Phunziro Lachinayi – Maulendo wa Abrahamu</b>  <b>Mutu – Kuyesedwa kwa chikondi chake</b></p>	<p><b>A6 – KALASI Yachinayi</b>  <b>Phunziro Lachinayi – Abrahamu</b>  <b>Mutu – Mayesero ake</b></p>
<b>MAWU OYAMBA</b>	<p><b>Ndime Yowerenga:</b> <i>Genesis 22:1-14</i>  <b>Vesi Yoloweza:</b> <i>Yohane 1:29</i></p> <p><b>Ife tikuphunzira kuti:</b></p> <ol style="list-style-type: none"> <li>1. Mulungu anayesa Abrahamu. Iye anaiza Abrahamu kuti apereke nsembe mwana wake mmodzi yekhayo. Abrahamu anamvera Mulungu ndipo anamudalira kwathunthu.</li> <li>2. Mulungu ndi Woperekwa Wamkulu. Iye anaperekwa nsembe yolowa m'malo mwa Isake.</li> <li>3. Mulungu anaperekwa Ambuye Yesu kutenga malo athu ndi kufa ngati nsembe yochotsa tchimo lathu.</li> </ol>	<p><b>Ndime Yowerenga:</b> <i>Genesis 22:1-19</i>  <b>Vesi Yoloweza:</b> <i>Ahebri 11:17-19</i></p> <p><b>Ife tikuphunzira kuti:</b></p> <ol style="list-style-type: none"> <li>1. Mulungu anayesa Abrahamu. Pamene Mulungu anaiza Abrahamu kuti apereke nsembe mwana wake mmodzi yekhayo, iye anamvera Mulungu ndi kumudalira kwathunthu.</li> <li>2. Mulungu ndi Woperekwa Wamkulu. Iye anaperekwa nsembe yolowa m'malo mwa Isake.</li> <li>3. Mulungu anadziwa kuti Abrahamu amamumvera, ndi kuti anali wokonzeka kuperekwa chilichonse, choncho anatsimikizango malonjezo ake.</li> <li>4. Mulungu anaperekwa Ambuye Yesu kutenga malo athu ndi kufa ngati nsembe yochotsa tchimo lathu.</li> </ol>
<b>KUTSIRIZA</b>	<p>Nthawi zina timagwiritsa ntchito mayeso kuti tidziwe zinthu zina mwa anthu. Lembanji mitundu ya mayeso yomwe anthu amachita (a galimoto, ku sukulu, nyimbo, kumva ndi kuona ndi ena ambiri). Mayeso awa amaonetetsa chinthu china cha anthuwo monga nzeru, kumvetsa zinthu, thupi lawo ndi khalidwe lawo. M'nhhani iyi, Mulungu anagwiritsa ntchito mayeso pofuna kudziwa ngati Abrahamu ankakhulupirira Mulungu.</p> <p><b>Perekani Nkhani ya m'Baibulo</b></p> <p><b>Kambiranani ndi Kufotokoza:</b></p> <ol style="list-style-type: none"> <li>1. Mulungu anamuua Abrahamu kuti apereke nsembe mwana wake mmodzi yekhayo Isake, akhale nsembe yopserenza, amene Mulungu anamulonjeza.</li> <li>2. Abrahamu anamvera malangizo a Mulungu. Iye anayenda masiku atatu kuti akafike ku malo amene Mulungu anamuua kuti apite.</li> <li>3. Pamene Isake anafunsa Abrahamu za nsembe imene amakapereka, Abrahamu anayankha kuti Mulungu adzaperekwa nsembe. Izi zikusonyeza kuti Abrahamu anali ndi chikhulupiriro chachikulu mwa Mulungu.</li> <li>4. Abrahamu anali womvera Mulungu kwathunthu. Iye anali wokonzeka kusiya chilichonse chifukwa cha Mulungu ndi kuperekwa nsembe mwana wake.</li> <li>5. Mulungu anayitana Abrahamu ndipo anamuua kuti asaphe mwana wake Isake.</li> <li>6. Mulungu anaperekadi nsembe imene inalowa m'malo mwa Isake: nkosa yaimuna.</li> <li>7. Mulungu anatsimikiza lonjezo lake kwa Abrahamu lakuti iye adzakhala ndi zidzukulu zambiri zomwe palibe amene adzathe kuziwerenga. Iye analonjezano kuti kudzera mwa zidzukulu zake adzadalitsa mitundu yonse ya pa dziko lapansi.</li> <li>8. Mulungu anatumiza Mwana wake kudzatenga malo athu monga "Mwanawankhosa wa Mulungu". Kudzera mwa Ambuye Yesu, Mulungu amatidalitsa ndi chipulumutso ngati takhulupirira iye.</li> </ol> <p><b>Fotokozani Vesi Yoloweza ndipo limbikitsani ophunzira kuti aloweze.</b></p> <p><b>Tsirizani Phunziro Lachinayi.</b></p> <p><b>Kuonetsa:</b> Onani FBI pa Zoonjezera B – Kuyesedwa kwa chikondi chake.</p>	<p>Kodi chilipo, kapena alipo wina m'moyo mwanu amene simungathe kukhala popanda iye? Kwa Abrahamu mwana wake anali mmodzi wa anthu amenewo. Abrahamu anadikira nthawi yayitali kuti abereke Isake. Kodi Abrahamu akanamva bwanji mu mtima mwake ngati akanataya Isake?</p> <p><b>Perekani Nkhani ya m'Baibulo</b></p> <p><b>Kambiranani ndi Kufotokoza:</b></p> <ol style="list-style-type: none"> <li>1. Mulungu anamuua Abrahamu kuti apereke nsembe mwana wake mmodzi yekhayo Isake, akhale nsembe yopserenza, amene Mulungu anamulonjeza.</li> <li>2. Abrahamu anamvera malangizo a Mulungu. Iye anayenda masiku atatu kuti akafike ku malo amene Mulungu anamuua kuti apite.</li> <li>3. Pamene Isake anafunsa Abrahamu za nsembe imene amakapereka, Abrahamu anayankha kuti Mulungu adzaperekwa nsembe. Izi zikusonyeza kuti Abrahamu anali ndi chikhulupiriro chachikulu mwa Mulungu.</li> <li>4. Abrahamu anali womvera Mulungu kwathunthu. Iye anali wokonzeka kusiya chilichonse chifukwa cha Mulungu ndi kuperekwa nsembe mwana wake.</li> <li>5. Mulungu anayitana Abrahamu ndipo anamuua kuti asaphe mwana wake Isake.</li> <li>6. Mulungu anaperekadi nsembe imene inalowa m'malo mwa Isake: nkosa yaimuna.</li> <li>7. Mulungu anatsimikiza lonjezo lake kwa Abrahamu lakuti iye adzakhala ndi zidzukulu zambiri zomwe palibe amene adzathe kuziwerenga. Iye analonjezano kuti kudzera mwa zidzukulu zake adzadalitsa mitundu yonse ya pa dziko lapansi.</li> <li>8. Mulungu anatumiza Mwana wake kudzatenga malo athu monga "Mwanawankhosa wa Mulungu". Kudzera mwa Ambuye Yesu, Mulungu amatidalitsa ndi chipulumutso ngati takhulupirira iye.</li> </ol> <p><b>Fotokozani Vesi Yoloweza ndipo limbikitsani ophunzira kuti aloweze.</b></p> <p><b>Tsirizani Phunziro Lachinayi.</b></p> <p><b>Kuonetsa:</b> Onani FBI pa Zoonjezera B – Mayesero ake.</p>
<b>KUKUMBUTSANA</b>	<ol style="list-style-type: none"> <li>1. Vesi Yoloweza ikutiphunzitsa kuti Ambuye Yesu ndi nsembe yangwiyo, Mwanawankhosa wa Mulungu, amene amachotsa tchimo la dziko lapansi.</li> <li>2. Kodi inu munadalira Mulungu ndi kulandira Yesu kuhala Mpulumutsi wanu?</li> <li>3. Lembanji Vesi Yoloweza pa kadi ndi kuyikongoletsa.</li> </ol>	<ol style="list-style-type: none"> <li>1. Abrahamu anaperekwa dzina pa malo pamene zinachitika zomwe taphunzirazi lakuti "Yehova Woperekwa." Kodi Yehova watipatsa ife motani? Zimene anachita? Zamoyo wauzimu?</li> <li>2. Kodi ife tichite chiyani ndi chimene Mulungu anatipatsa?</li> </ol>
<b>KHALANI MOYO UMENEWU</b>	<p><b>Zomwe tikuphunzira m'phunziroli:</b></p> <p>Abrahamu anakhulupirira Mulungu kwathunthu ndi kumvera ndipo Mulungu anamudalitsa kwambiri chifukwa cha chimenechi. Kodi ife tingatsatire motani chitsanzo cha Abrahamu?</p>	<p><b>Zomwe tikuphunzira m'phunziroli:</b></p> <p>Abrahamu anadilira Mulungu ndipo anamumvera iye, ngakhale pamene anayesa chikhulupiriro chake. Kodi ife tingatsatire motani chitsanzo cha Abrahamu?</p>

# Malangizo a Aphunzitsi a Kachongedwe ka Maphunziro

## Maphunziro a Kalasi Lachitatu

- Ophunzira sangatsirize maphunziro awa popanda kuwerenga Baibulo ndipo akuyenera kuwerenga ndime imodzi kapena zambiri.
- Kafunsidwe n'kosiyanasiyana, pena pali mabokosi, pena pali mawu amene akusowa ndi njira zina zambiri.
- Mafunso akonzedwa kuti aziyankhidwa kuchokera m'baibulo la Mawu a Mulungu mu Chichewa Chalero ndi Buku Lopatulika ndi Mawu a Mulungu.
- Cholina chathu n'chakuti ophunzira onse, kaya akugwiritsa Baibulo la mtundu wanji, azitha kuyankha mafunso.
- Sabata lilonse lili ndi marikisi 20 ndipo pa mwezi pali marikisi 80, ngati munthu wakhonza bwino maphunziro onse.
- Kalasi Lachitatu - Pali marikisi imodzi pa yankho, monga momwe tasonyezera.

## Maphunziro a Kalasi Lachinayi

- Awa ndi maphunziro ovutirapo kusiyana ndi Maphunziro a Kalasi Lachitatu.
- Muli mafunso ovutirapo ofuna mayankho.
- Marikisi 20 pa sabata ndi marikisi makumi 80 pa mwezi ngati amaliza maphunziro molondola ndiponso mafunso onse ali ndi mayankho ake.

## FUNDO ZA KACHONGEDWE

Choyamba aphunzitsi akupempchedwa kuti:

- Onani phunziro lilonse ndipo chongani moyenera zolondola kapena zolakwitsa.
- Perekani marikisi amene mwalandizidwa kutero.
- Nthawi zonse chongani pogwiritsa ntchito mitundu yosiyana ya zolembra, CHONGANI yankho lolondola.
- Lembani yankho lolondola poyenera kutero ndi kukonza mawu olakwika kalembedwe ake, koma MUSACHOTSE marikisi.
- Perekani marikisi ochepa pa yankho lolondola mbali imodzi yokha.
- Phatikizani marikisi onse a pa mwezi ndipo lembani kumapeto pa malo amene mwapatsidwa.

N'kofunika kusaumira ndi kuchita chilichonse chothandiza kulimbikitsa ophunzira kuti aphanzire Baibulo lawo. N'zothandizanso kuti kumapeto kwa mwezi uliwonse mphunzitsi azilemba mawu a chilimbikitso kwa wophunzira pa malo amene aperekedwa. Mutha kulemba ndemanga yoyamikira kuchekenira bwino, zilembo zabwino ndi kumvetsa bwino phunziro ndi zina zambiri.

Yesetsani kuti ndemanga, mafunso, ziganizo, zomwe mwaona ndi zina zambiri zikhale zosiyanasiyana, kuti zithandize kupanga zinthu kukhala zosiyanayana. Izi zimafunika kuganiza bwino, ndipo ndi kofunika kuti wophunzira azikhala ndi chidwi nthawi zonse. Ngati chiganizo chomwecho kapena funso lomwe likubwera mwezi uliwonse, zimachotsa chidwi cha wophunzira.

## KALASI Lachitatu

### Ndemanga zina

"Ntchito yabwino kwambiri! Inu munamvetsa bwino mafunso onse. Ine ndasangalala ndi yankho la funso lotsiriza limene mwaliyankha bwino kwambiri."

"Moni Yonatani. Ndikuyamika chifukwa cha kulimbikira kwako. Ndi zosangalatsa kwambiri kuti wayesetsa kuyankha mafunso onse. Ine ndalembe mayankho a mafunso ena amene sunayankhe."

### Ndemanga zauzimu

"Mose anali ndi mavuto ndi ana a Israeli, koma Mulungu sanamusiyekha kuti athetse mavutowo."

"Yosefe sanayiwale kuti abambo ake anamuphunzitsa kukonda Mulungu. Iye anakumbukira zimenezi ngakhale anali kutali ndi kwavo."

"Bartimeyu anatsimikiza mtima zofuna kulandira kuchokera kwa Ambuye Yesu. Iye sanakhumudwitsidwe chifukwa tsopano ankatha kuona ndipo anadziwa kuti Ambuye Yesu anali munthu wapadera kwambiri."

## KALASI Lachinayi

### Ndemanga zina

"Maphunziro enanso abwino kwambiri. Zikuoneka kuti tsopano ukumvetsa bwino Nkhani za m'Baibulo ndipo ndikukhulupirira kuti wasangalala nazo. Zikomo kwambiri chifukwa chokhala ndi nthawi yokwanira yochita mosamala maphunzirowa. Zikanatheka kuchita mofulumira, choncho ine ndi kuyamika kwambiri."

"Rakele, wayetsetsa ndithu. Ine ndikaona mayankho akowa, zikuonetsa kuti sunamvetse bwino Nkhani za m'Baibulo. Bwanji uwerengenso zimenezi."

### Ndemanga zauzimu

"Mafanizo nthawi zina amatchedwa nkhani wamba koma zokhala ndi matanthauzo akumwamba kapena ozama. Kodi ungaganizire tanthauzo lozama la fanizo lomwe lili mu Phunziro 3?"

"Stefano anafa imfa yowawa kwambiri, koma iye sanachite mantha ndi imfa, chifukwa ankadziwa kuti anali ndi Mulungu, ndipo ankadziwa kuti akakhala ndi Ambuye Yesu kumwamba."

## Zoonjezera A - Kalasi Lachitatu Zinthunzi Zaulelele m'Baibulo

	Mutu	Nkhani m'Chithunzi
A1	Pachiyambi	<p><b>Mulungu analenga dziko lonse</b></p> <p><a href="https://www.freebibleimages.org/illustrations/creation/">https://www.freebibleimages.org/illustrations/creation/</a></p>
		<p><b>Mulungu analenga munthu</b></p> <p><a href="https://www.freebibleimages.org/illustrations/creation/">https://www.freebibleimages.org/illustrations/creation/</a></p>
		<p><b>Zinthu zinayamba kusokonekera!</b></p> <p><a href="https://www.freebibleimages.org/illustrations/adam-eve-fall/">https://www.freebibleimages.org/illustrations/adam-eve-fall/</a></p>
		<p><b>Kuchita zinthu m'njira ya Mulungu</b></p> <p><a href="https://www.freebibleimages.org/illustrations/cain-abel/">https://www.freebibleimages.org/illustrations/cain-abel/</a></p>
		<p><a href="https://www.freebibleimages.org/illustrations/rp-faith-hebrews-11-a/">https://www.freebibleimages.org/illustrations/rp-faith-hebrews-11-a/</a></p>
		<p><a href="https://www.freebibleimages.org/illustrations/gnpi-001-word-flesh/">https://www.freebibleimages.org/illustrations/gnpi-001-word-flesh/</a></p>
A2	Nowa ndi Chigumula	<p><b>Kupanga Chombo</b></p> <p><a href="https://www.freebibleimages.org/illustrations/noah-ark/">https://www.freebibleimages.org/illustrations/noah-ark/</a></p>
		<p><b>Kulowa m'Chombo</b></p> <p><a href="https://www.freebibleimages.org/illustrations/noah-ark/">https://www.freebibleimages.org/illustrations/noah-ark/</a></p>
		<p><b>Kupulumuka mu Chombo</b></p> <p><a href="https://www.freebibleimages.org/illustrations/noah-ark/">https://www.freebibleimages.org/illustrations/noah-ark/</a></p>
		<p><b>Kunja kwa Chombo</b></p> <p><a href="https://www.freebibleimages.org/illustrations/noah-ark/">https://www.freebibleimages.org/illustrations/noah-ark/</a></p>
A3	Moyo wa Petulo	<p><b>Yesu ayitana Petulo</b></p> <p><a href="https://www.freebibleimages.org/illustrations/gnpi-015-first-disciples/">https://www.freebibleimages.org/illustrations/gnpi-015-first-disciples/</a></p>
		<p><a href="https://www.freebibleimages.org/photos/lumo-fishers-men/">https://www.freebibleimages.org/photos/lumo-fishers-men/</a></p>
		<p><b>Kugwira nsoma zambiri</b></p> <p><a href="https://www.freebibleimages.org/photos/jesus-calls-disciples/">https://www.freebibleimages.org/photos/jesus-calls-disciples/</a></p>
		<p><a href="https://www.freebibleimages.org/photos/galilee-fish-nets/">https://www.freebibleimages.org/photos/galilee-fish-nets/</a></p>
		<p><b>Yesu apulumutsa Petulo</b></p> <p><a href="https://www.freebibleimages.org/illustrations/jesus-water/">https://www.freebibleimages.org/illustrations/jesus-water/</a></p>
		<p><a href="https://www.freebibleimages.org/illustrations/gnpi-054-walking-water/">https://www.freebibleimages.org/illustrations/gnpi-054-walking-water/</a></p>
		<p><b>Kodi Yesu ndi yani?</b></p> <p><a href="https://www.freebibleimages.org/illustrations/gnpi-056-peter-confession/">https://www.freebibleimages.org/illustrations/gnpi-056-peter-confession/</a></p>
		<p><a href="https://www.freebibleimages.org/photos/jesus-teaching/">https://www.freebibleimages.org/photos/jesus-teaching/</a></p>

## Zoonjezera B - Kalasi Lachitatu Zinthunzi Zaulelele m'Baibulo

	Mutu	Nkhani m'Chithunzi
A4	<b>Moyo wa Petulo</b>	<p><b>Chitsanzo cha chikondi</b>  <a href="https://www.freebibleimages.org/illustrations/last-supper-jesus/">https://www.freebibleimages.org/illustrations/last-supper-jesus/</a></p> <p><b>Iye anakana Mbuye wake</b>  <a href="https://www.freebibleimages.org/illustrations/gethsemane-peter/">https://www.freebibleimages.org/illustrations/gethsemane-peter/</a></p> <p><b>Imfa ya Ambuye Yesu</b>  <a href="https://www.freebibleimages.org/illustrations/jesus-crucified-dies/">https://www.freebibleimages.org/illustrations/jesus-crucified-dies/</a></p> <p><b>"Kodi umandikonda Ine?"</b>  <a href="https://www.freebibleimages.org/illustrations/peter-reinstated/">https://www.freebibleimages.org/illustrations/peter-reinstated/</a></p> <p><b>Petulo alalikira</b>  <a href="https://www.freebibleimages.org/illustrations/jesus-ascension/">https://www.freebibleimages.org/illustrations/jesus-ascension/</a></p> <p><b>Petulo achiritsa munthu</b>  <a href="https://www.freebibleimages.org/illustrations/lame-beggar-healed/">https://www.freebibleimages.org/illustrations/lame-beggar-healed/</a></p> <p><b>Petulo achitira umboni</b>  <a href="https://www.freebibleimages.org/illustrations/peter-john-arrested/">https://www.freebibleimages.org/illustrations/peter-john-arrested/</a></p> <p><b>Petulo m'ndende</b>  <a href="https://www.freebibleimages.org/illustrations/peter-john-arrested/">https://www.freebibleimages.org/illustrations/peter-john-arrested/</a></p>
A5	<b>Moyo wa Petulo</b>	<p><b>Kukhulupirira Mulungu</b>  <a href="https://www.freebibleimages.org/illustrations/abraham-canaan/">https://www.freebibleimages.org/illustrations/abraham-canaan/</a></p> <p><b>Zisankho</b>  <a href="https://www.freebibleimages.org/illustrations/abraham-lot/">https://www.freebibleimages.org/illustrations/abraham-lot/</a></p> <p><b>Malonjezo a Mulungu</b>  <a href="https://www.freebibleimages.org/illustrations/abraham-isaac/">https://www.freebibleimages.org/illustrations/abraham-isaac/</a></p> <p><b>Kuyesedwa kwa chikondi chake</b>  <a href="https://www.freebibleimages.org/illustrations/abraham-isaac/">https://www.freebibleimages.org/illustrations/abraham-isaac/</a></p>
A6	<b>Maulendo a Abrahamu</b>	<p><b>Malonjezo a Mulungu</b>  <a href="https://www.freebibleimages.org/illustrations/abraham-strangers/">https://www.freebibleimages.org/illustrations/abraham-strangers/</a></p> <p><b>Hathor a Mulungu</b>  <a href="https://www.freebibleimages.org/photos/prophecies-birth-jesus/">https://www.freebibleimages.org/photos/prophecies-birth-jesus/</a></p>

## Zoonjezera A - Kalasi Lachinayi Zinthunzi Zaulelele m'Baibulo

	Mutu	Nkhani m'Chithunzi
A1	<b>Chilengedwe</b>	<b>Pachiyambi</b>  <a href="https://www.freebibleimages.org/illustrations/creation/">https://www.freebibleimages.org/illustrations/creation/</a>
		<b>Kutsiriza</b>  <a href="https://www.freebibleimages.org/illustrations/creation/">https://www.freebibleimages.org/illustrations/creation/</a>
		<b>Kubwera kwa tchimo</b>  <a href="https://www.freebibleimages.org/illustrations/creation/">https://www.freebibleimages.org/illustrations/creation/</a>
		<b>Zotsatira za tchimo</b>  <a href="https://www.freebibleimages.org/illustrations/adam-eve-fall/">https://www.freebibleimages.org/illustrations/adam-eve-fall/</a>
		<a href="https://www.freebibleimages.org/illustrations/adam-eve-fall/">https://www.freebibleimages.org/illustrations/adam-eve-fall/</a>
A2	<b>Zochitika Zoyamba</b>	<b>Kupembedza Mulungu – Kaini ndi Abele</b>  <a href="https://www.freebibleimages.org/illustrations/cain-abel/">https://www.freebibleimages.org/illustrations/cain-abel/</a>
		<a href="https://www.freebibleimages.org/illustrations/rp-faith-hebrews-11-a/">https://www.freebibleimages.org/illustrations/rp-faith-hebrews-11-a/</a>
		<b>Kuyenda ndi Mulungu – Enoki ndi Nowa</b>  <a href="https://www.freebibleimages.org/illustrations/rp-faith-hebrews-11-a/">https://www.freebibleimages.org/illustrations/rp-faith-hebrews-11-a/</a>
		<a href="https://www.freebibleimages.org/illustrations/elijah-chariot/">https://www.freebibleimages.org/illustrations/elijah-chariot/</a>
		<a href="https://www.freebibleimages.org/illustrations/noah-ark/">https://www.freebibleimages.org/illustrations/noah-ark/</a>
		<b>Kugwira ntchito ya Mulungu – Nowa ndi Madzi a Chigumula</b>  <a href="https://www.freebibleimages.org/illustrations/noah-ark/">https://www.freebibleimages.org/illustrations/noah-ark/</a>
		<a href="https://www.freebibleimages.org/illustrations/rp-faith-hebrews-11-a/">https://www.freebibleimages.org/illustrations/rp-faith-hebrews-11-a/</a>
		<b>Kupembedza Mulungu – Nowa ndi Banja Lake</b>  <a href="https://www.freebibleimages.org/illustrations/noah-ark/">https://www.freebibleimages.org/illustrations/noah-ark/</a>
		<a href="https://www.freebibleimages.org/illustrations/rp-faith-hebrews-11-a/">https://www.freebibleimages.org/illustrations/rp-faith-hebrews-11-a/</a>
		<a href="https://www.freebibleimages.org/illustrations/isc-animals/">https://www.freebibleimages.org/illustrations/isc-animals/</a>
A3	<b>Petulo</b>	<b>Mayitanidwe ake</b>  <a href="https://www.freebibleimages.org/illustrations/gnpi-015-first-disciples/">https://www.freebibleimages.org/illustrations/gnpi-015-first-disciples/</a>
		<b>Mavuto ake</b>  <a href="https://www.freebibleimages.org/illustrations/jesus-water/">https://www.freebibleimages.org/illustrations/jesus-water/</a>
		<a href="https://www.freebibleimages.org/illustrations/gnpi-054-walking-water/">https://www.freebibleimages.org/illustrations/gnpi-054-walking-water/</a>
		<b>Kuvomereza kwake</b>  <a href="https://www.freebibleimages.org/illustrations/gnpi-056-peter-confession/">https://www.freebibleimages.org/illustrations/gnpi-056-peter-confession/</a>
		<b>Pa phiri</b>  <a href="https://www.freebibleimages.org/illustrations/gnpi-057-transfiguration/">https://www.freebibleimages.org/illustrations/gnpi-057-transfiguration/</a>

## Zoonjezera B - Kalasi Lachinayi Zinthunzi Zaulelele m'Baibulo

	Mutu	Nkhani m'Chithunzi
A4	<b>Petulo</b>	<p><b>Maphunziro a kudzichepetsa</b></p> <p><a href="https://www.freebibleimages.org/photos/last-supper/">https://www.freebibleimages.org/photos/last-supper/</a></p> <p><a href="https://www.freebibleimages.org/photos/jesus-washes-feet/">https://www.freebibleimages.org/photos/jesus-washes-feet/</a></p> <p><b>Phunziro la kudzipereka</b></p> <p><a href="https://www.freebibleimages.org/photos/last-supper/">https://www.freebibleimages.org/photos/last-supper/</a></p> <p><a href="https://www.freebibleimages.org/photos/jesus-gethsemane/">https://www.freebibleimages.org/photos/jesus-gethsemane/</a></p> <p><a href="https://www.freebibleimages.org/photos/peter-denies-jesus/">https://www.freebibleimages.org/photos/peter-denies-jesus/</a></p> <p><b>Nthawi yachisoni ndi yachimwemwe</b></p> <p><a href="https://www.freebibleimages.org/photos/jesus-dies/">https://www.freebibleimages.org/photos/jesus-dies/</a></p> <p><a href="https://www.freebibleimages.org/photos/jesus-alive/">https://www.freebibleimages.org/photos/jesus-alive/</a></p> <p><a href="https://www.freebibleimages.org/photos/jesus-appears-disciples/">https://www.freebibleimages.org/photos/jesus-appears-disciples/</a></p> <p><b>Maphunziro mwa chikondi</b></p> <p><a href="https://www.freebibleimages.org/illustrations/gnpi-105-peter-restored/">https://www.freebibleimages.org/illustrations/gnpi-105-peter-restored/</a></p> <p><a href="https://www.freebibleimages.org/photos/jesus-questions-peter/">https://www.freebibleimages.org/photos/jesus-questions-peter/</a></p>
A5	<b>Moyo wa Petulo</b>	<p><b>Pentekosite</b></p> <p><a href="https://www.freebibleimages.org/illustrations/jesus-ascension/">https://www.freebibleimages.org/illustrations/jesus-ascension/</a></p> <p><a href="https://www.freebibleimages.org/illustrations/pentecost/">https://www.freebibleimages.org/illustrations/pentecost/</a></p> <p><b>Kuchiritsa munthu wolumala</b></p> <p><a href="https://www.freebibleimages.org/illustrations/lame-beggar-healed/">https://www.freebibleimages.org/illustrations/lame-beggar-healed/</a></p> <p><b>Pamaso pa bwalo lalikulu la Ayuda</b></p> <p><a href="https://www.freebibleimages.org/illustrations/peter-john-arrested/">https://www.freebibleimages.org/illustrations/peter-john-arrested/</a></p> <p><b>M'ndende</b></p> <p><a href="https://www.freebibleimages.org/illustrations/peter-prison/">https://www.freebibleimages.org/illustrations/peter-prison/</a></p>
A6	<b>Abrahamu</b>	<p><b>Mayitanidwe ake</b></p> <p><a href="https://www.freebibleimages.org/illustrations/abraham-canaan/">https://www.freebibleimages.org/illustrations/abraham-canaan/</a></p> <p><a href="https://www.freebibleimages.org/illustrations/bj-maps-eden-egypt/">https://www.freebibleimages.org/illustrations/bj-maps-eden-egypt/</a></p> <p><b>Chisankho chake</b></p> <p><a href="https://www.freebibleimages.org/illustrations/abraham-lot/">https://www.freebibleimages.org/illustrations/abraham-lot/</a></p> <p><b>Chitsimikizo chake</b></p> <p><a href="https://www.freebibleimages.org/illustrations/abraham-promise/">https://www.freebibleimages.org/illustrations/abraham-promise/</a></p> <p><a href="https://www.freebibleimages.org/illustrations/abraham-strangers/">https://www.freebibleimages.org/illustrations/abraham-strangers/</a></p> <p><b>Mayesero ake</b></p> <p><a href="https://www.freebibleimages.org/illustrations/abraham-isaac/">https://www.freebibleimages.org/illustrations/abraham-isaac/</a></p> <p><a href="https://www.freebibleimages.org/photos/shepherds-sheep/">https://www.freebibleimages.org/photos/shepherds-sheep/</a></p> <p><a href="https://www.freebibleimages.org/photos/jesus-dies/">https://www.freebibleimages.org/photos/jesus-dies/</a></p>



© Bible Educational Services 2020

[www.besweb.com](http://www.besweb.com)

Registered Charity UK CIO 1186004

NY - 02/2023  
(Chichewa)